MSUNTHO: MLOZO WOLANGIZIRA GULU

CONTENTS

MWALANDIRIDWA KU MSUNTHO 3

MLOZO WA PHUNZIRO 9

PHUNZIRO 1: MWALANDIRIDWA KU MSUNTHO 9

PHUNZIRO 2: CHIZINDIKIRO CHA MLALIKI 13

PHUNZIRO 3: UTHENGA WA MLALIKI 17

PHUNZIRO 4: NTCHITO YA MLALIKI 21

PHUNZIRO 5: MPHAMVU YA MLALIKI 26

PHUNZIRO 6: KUDZIPERERKA KWA MLALIKI 31

PHUNZIRO 7: KUGONJERA KWA MLALIKI 35

PHUNZIRO 8: KHALIDWE LA MLALIKI 40

PHUNZIRO 9: MWAYI WA MLALIKI 45

PHUNZIRO 10: KUDZIPERERKA KWA MLALIKI 50

PHUNZIRO 11: CHILIMBIKITSO CHA MLALIKI 55

PHUNZIRO 12: M'BINDIKIRO 60

ZOWONJEZERA 64

ZIPHUNZITSO ZA UTHENGA WABWINO 64

KUSIMBA UTHENGA WABWINO 65

CHITSANZO CHA KULANKHULA UTHENGA WABWINO KWA ACHINYAMATA 66

MAFUNSO A KUKHALA ADINDO A MOYO WANU 69

UTHENGA WABWINO. PALIBE NDONDOMEKO INANSO.

UTHENGA WABWINO NDI NKHANI YABWINO YOYENERA KULENGEZEDWA NDIPO SINATAYE MPHAMVU ZAKE ZOPULUMUTSIRA ANTHU KUDZERA MMAGULU A ANTHU OCHEPA OWATSOGOLERA, MSUNTHO UMAPEREKA ZIDA KULIMBIKITSANA KUPEREKA MPHAMVU KU MPINGO ZA KUFALITSA MAWU KOMANSO KUTAKASA. KUKUZA MPHATSO ZA ULALIKI MWA IWO AMENE ANAITANIDWA NGATI ALALIKI.

Msuntho unakula kuchokera ku kudzikhutula kwa Mlaliki Andy Hawthome (Uthenga wa Chikhulupiriro) ndi Andrew Palau (Luis Palau Association) kusonkhanitsa pamodzi alaliki 12 achinyamata olkalikira mmagulu ang'onoang'ono mmilaga ndi cholinga chowakuza ndi kuwanola.

Kudzera mmisonkhano ya pa mwezi, iwo amene ali mmagulu amalandira maphunziro, kunolana wina ndi nzake kudzera mu zokambirana ndi kugawana mosabisilana zokhuza moyo wawo wa kuthupi ndi wa Uzimu. Amatumizira za zomwe zawachitikira pafupipafupi pakati pa ndime zokumana mmagulu (pogwiritsa ntchito **WhatsApp kapena zina zofananirapo zotumizira uthenga**), zokhudza mwayi ndi ntchito zawo zimene ayenera kugawana Uthenga wabwino ndi kulimbikitsana wina ndi nzake ndi zipatso zochokera ku mwayi umene unapezeka.

Patatha chaka choyamba atakhala nawo mu gulu, Msuntho, komanso popitiiliza pamodzi, mu magulu awo oyambirira, mamembala onse a gulu aganiziranso zopeza anthu 12 ena owonjezera amene angaitanidwe ku gulu latsopano kuti awaphunzitse mu njira yomweyo pamene kukufunafuna kukulitsa chiwerengero cha Akhristu amene popanda manyazi komanso molimba mtima angagawe uthenga - kaya kulalikira pa gome kapena pa nsanja kapena kudzera mukukumanga kwa tsiku ndi tsiku ndi banja lawo, anzawo kapena alendo mu kulalikira kwawo.

Kuchokera pamene linakaazikitsidwa mchaka cha 2015, Msuntho wakula kuchokera ku gulu kuyambira ku Manchester, Uk, kukhala gulu la chitsitsimutso la dziko lonse lapansi la mazanamazana a magulu okumana pafupipafupi kuzungulira dziko lonse lapansi amene ali odzipereka kuwuzira moto wa mphatso ya Mulungu mmoyo mwawo kuti dziko lapansi limudziwe Mulungu.

NGODYA ZISANU ZA GULULI

Izi ndi ngodya zisanu zimene gulu la Msuntho linakhazikika:

1. KUKUMANA PAFUPIPAFUPI
Mamembala a gulu ziyenera kuyika mu mlozo wawo ngati chinthu chofunikira kwambiri misonkkhano yawo ya pa mwezi. Ndi chofunikira kwambiri ngati anthu amene alowa mu gulu ili kudzikhuthula ku misonkhano. Magulu alimibikitse kutenga ndimezi ngati chopatulika – mamaembala achite chirichonse chothekera kuti apewe ntchito zina zimene zingapezeka pa tsiku limene agwirizana zokumana kapena misonkhano ina kudzikhuthula kwakukulu kukukonzekera ku ntchito imene Mulungu wakuitanni kuti mugwire naye ntchito limodzi ndipo ichi ndi chida cha maziko cha ulendo wagulu la Msuntho.

2. KUNOLANA
Kudzipereka kukuphunzira Buku Lopatulika kupeza nzeru zakuya za uthenga wabwino kumatenga gawo lalikulu la nthawi ya maphunziro a pamwezi uliwonse, ndi kuphatikizanso kukhala ndi nthawi yoyenera yabwino yakulangizana kapena kudzudzulana wina ndi mnzake kumvetsetsana ndi kugwiritsa ntchito ulaliki ndi uthenga wabwino mu chiyambi cha kudzera mu kukambirana.

3. KUKHALA MDINDO WA KHALIDWE
Kudzisanthula mowona mtima kudzera mukuyankhidwa mmafunso ndi kugawana moonetsera mkati mwa nthawi ya gulu yokonzedwera kutsimikiza kuti tikukhala moyo wosadzibisa zimene tikuchita ndi moyo wachiyero pomwe tikuyesera kukhala moyo okhulupirika mmakhalidwe ndi kugawana uthenga wabwino. Kudzichepetsa ndi kuchita moona mtima mugulu lanu kungathe kutenga nthawi kuti zikatheke koma zilimbikitsidwe ndi kutsogozedwa ndi mtsogoleri wagulu.

4. KULANKHULANA
Kudziwitsana zimene zikuchitika za mwayi opezeka pa uthenga wabwino, zopemphererana, ndi nkhani za chipulumutso kudzera mu e-mail kapena kulemberana muthenga pa lamya, kumatsimikizra kuti gulu limathandizana wina ndi mnzake ngati mudzi, kukhala olumikizana pamene palibe maphunziro kumapanga gulu kukhala lamphamvu.

5. KUCHULIKITSA
Kudzipereka kupeza maganizo ochulikitsa ndi malingaliro a mamembala a gulu kutenga gulu lawo (pomwe akupitiliza ndi gulu loyamba) mkati mwa miyezi 12 mpaka 18 kuchokera pamene analowa gulu. Sionse omwe analowa gulu adzakwaniritsa kupanga gulu lawo koma kugwiritsa ntchito bukuli ndi kukhala ndi cholinga chofuna kutero, ambiri angathe ndpoi adzatha – kutsimikizira, kukonzekeretsa, kupereka mphamvu ndi kulimbikitsa akhristu odzipereka, kufalitsa, kukhulupirila, kukula ndi kufala dziko lonse lapansi.

KODI NDI ZA INE?

Buku Lopatulika limavumbulutsa kuti ntchito ya ulaliki ndi mphatso yapaderadera yochokera kwa Mulungu yomangira mpingo (Aefeso 4:11-12). Mlaliki adzapindula pobweretsa anthu kwa Khristu pomwe akugawana nawo uthenga wabwino, komanso adzapindula popereka zida ndi kutakasa mpingo onse kukhala okhulupirika pakuchira umboni za uthenga wabwino.

Komabe, magulu a Msuntho sali a okhawo amene ali ndi mphatso ndi maitanindwe ku gawo lapaderadera la (nthawi zina limatchedwa 'office') mlaliki, ndi aliyense amene akufuna kukula mu mumamvetsedwe a uthenga wabwino ndi kuthekera kwawo kwakupereka chiyembekezo paliponse pamene pali mwai umene Mulungu wapereka. Ntchito iyi yayikulu ya Yesu Khristu yopita mu dziko monse ndi kupanga ophunzira ake ndi ntchito ya okhulupirira onse. Kufalitsa, moyenerera ndi chochita cha mkhristu aliyense kaya ndife "odalitsika" timulalikire mmau ndi mu zochita kapena ayi, tinayitanidwa "kuchita ntchito ya mlaliki povumbulitsira Khristu kwa anthu a dziko lapansi (2 Timoteo 4:1-5). Mu njiramo, ena atha kutulukira mphatso ndi maitanidwe ku ntchito ya mlaliki mmoyo mwao. Mwa njira ina, pokhapokha atatsimikizidwa, mau akuti mlaliki akugwiritsidwa ntchito mu Mlozo wa Msuntho ngati mawu oyitanira aliyense kuti achite nawo

mu kufalitsa osangoti okhawo opatsidwa ‘mphatso’.

Kuti mwapeza mwayi wolalikira pa gome kapena muli ndi khumbo lofuna kufikira anthu amene mumakumna nawo tsiku ndi tsiku, mafunso atatu ophweka awa adzakuthandizani kupanga chiganizo choyamba (kapena kulowa) gulu la Msuntho kwa inu,

CHIKHULUPIRIRO
Kodi muli nacho chikhulupiriro chakuti uthenga wabwino sunataye mphamvu yake ndi pang’ono pomwe, ndipo ndi njira yokhayo imene munthu angadziwire moyo weniweni ndi chipulumutso?

KUMVEKA BWINO
Kodi muli ndi khumbo lopereka uthenga wabwino momveka bwino kudzera mu mwayi ulionse opezeka kwai nu kuti mugawane ndi ena?

KUITANIRA
Kodi muli ndi kufunitsitsa kwa kuitanira ena ku chiyembekezo cha uthenga wabwino, ndi kuona anthu akusunthira mu ubale wa muyaya ndi Yesu?

Ngati mungayankhe kuti ‘Inde’ ku mafunso amenewa, ndihe kuti Msuntho adzakuthandiza. Mungathe kuymaba posnkhanitsa gulu laling’ono la ena amenenso angathe kunena ‘inde’ ku mafunso amenewo ndi kugwiritsa ntchito Bukhu la Msuntho: Mzolo Wolangizira Gulu kuti tiyambire limodzi ulendowu.

MLOZO WA PHUNZIRO

Mlozo uwu ukuphatikiza maphunziro a chaka choyamba cha kuyendetsa gulu la Msuntho kamodzi pa mwezi. Ngai muli mkhalakale ngati mlaliki ndipo ndinu odzidalira ku zinthu ngati izi, mungathe kufuna kugwiritsa ntchito maphunziro awa ngati oyambira, kuphatikiza ndi kukonzanso nkhani kuti mukwaniritse zosowa za gulu lanu ndi kugwiritsa ntchito upangiri wanu wakale. Ngati muli woyamba kumene, ndiye kuti mumasuke, kutsatira maphunzirowa, mau ndi mau, malangizo ndi malangizo, muli nazo zonse zofunikira kuti mukule pamodzi ngati gulu.

MUONI WA MLALIKI

Maphunziro khumi ndi awiri oyambirira akupereka kumvetsa kwa uthenga wabwino, ulaliki ndi khalidwe la mlaliki. Maphunziro agawidwa magawo akuti aphunzitsa makhalidwe asanu a mlaliki amene akupezeka mu chiyambi cha maphunziro (**Phunziro 1**).

ALALIKI OPHUNZITSA BUKU LOPATULIKA: DZIWANI UTHENGA WABWINO MWAKUYA (PHUNZIRO 2–4)
Tidziwe uthenga omwe tikufalitsa mwakuya kwambiri ngati kungatheke kuti tithe kuchita izi tidzikhutule kukuwerenga ndi kuphunzira mau a Mulungu, ndi cholinga chakuti kufalitsa kwathu kusakhale maganizo athu okha kapena zongoyerekeza zokhudza uthenga wabwino, koma muzomwe mau a Mulungu akutiphunzitsa. Mau otumiza a Yesu pa Mateyu 28 akutiyitanira ife kupanga ophunzira a mitundu yonse, kuwaphunzitsa anthu kumvera zimene Yesu anatilamula. Tinayitanidwa osati tingokhala aliliki chabe, koma alaliki ophunzitsa Buku Lopatulika kugawana choonadi mmalo mwa malingaliro athu. Maphunziro atatu awa adzalingalira za uthenga wabwino ndi kufalitsa molingana ndi chimene Buku Lopatulika limaphunzitsa ife za Atate, Mwana ndi Mzimu Woyera.

ALALIKI APEMPHERO: CHITANI MU MPHAMVU YA MZIMU (PHUNZIRO 5–6)
Tiyenera tigonjere mphamvu ya Mzimu Woyera kuti ntchito ya kufalitsa, pakuti simphamvu yathu koma mphamvu ya Mulungu imene imabweretsa chipulumutso. Choncho, tidzikhuthure mukukhala moyo wapemphero, kupempha Mulungu kuti atipatse mwayi wogawana chikhulupriro chathu ndi ena ndi kuwona miyoyo yambiri ikusandulika kumapeto kwake. Maphunziro awa akuunikira moyo wauzimu wa mlaliki ndi kupereka mwayi wounikira kudzipereka kwa miyoyo yathu ndi mphamvu imene ipezeke mwachindunji mu ntchito yathu yakufalitsa.

ALALIKI A UDINDO LA KHALIDWE LAWO: KHALANI MOYO WACHIYERO (PHUNZIRO 7–8)
Chiyero ndi mtima wa uthenga wabwino kugawana mphamvu ya kusandulika ya uthenga wabwino mu choona chenicheni ndi njira

yokhalira moyo wa udindo wa khalidwe lake, umene moyo wathu 'akakhala pa gome' ulingane ndi 'akachoka pa gome'. Kuchemererana mkati mwakupambana ndi kuima pamodzi wina ndi mnzake nthawi yakulephera ndi kufunikira kwambiri pomwe tikufunafuna kukula ngati anthu a chiyero omwe akugawana uthenga. Maphunziro awa akuunikira pa chiyero cha mlaliki, kutsindika kufunikira kwa kuika moyo pa mbalambanda ndi pa malo odzichepetsa ngai khalidwe lalikulu kwambiri la iwo amene akutumikira Yesu.

ALALIKI ODZIKHUTULA: KUKHALA NDI MTIMA WA PA NTCHITO (PHUNZIRO 9–10)
Kukhala ndi mtima wolakaka ndi fungolo wa kufalitsa uthenga. Tikhale tikudziwa – kulanda – mwayi wa tsiku ndi tsiku wofuna kugawana chikondi cha Mulungu, osati kungogawa nthano ya Yesu. Koma kuitanira iwo amene akumva ku moyo watsopano umene akupereka ndi kuwathandiza kuyamba ulendo wokhala ophunzira. Maphunziro awa akuwunikira mifungolo iwiri ya zolinga zimene ndi zowonekera kwambiri mu mphatso za kufalitsa mwayi wochuruka wopezeka wa mphamvu wogawira uthenga wabwino tsiku lirilonse ndi kufunitsa kuitana anthu ku ufumu pa chimake cha mwayi uliwonse wa uthenga wabwino.

ALALIKI A CHILIMBIKITSO: KUTAKASA MPINGO UCHITIRE UMBONI (PHUNZIRO 11)
Pamene tikugawana uthenga wabwino ndi dziko limene ukulifuna, tiyenera kutakasa mpingo kuti uchite chimodzimodzi. Kufalitsa uthenga ndi ntchito ya mkhristu aliyense, choncho kulimbikitsa ndi kutakasa mpingo ku ntchitoyi kukhalenso kudzikhutula kwa mlaliki. Phunziro ili likuwunikira udindo wa mlaliki ngati wolimbikitsa wa mpingo kusunga kuchitra umboni wa chikhristu ngati ngodya za chimene tili monga otsatira a Yesu.

Msuntho uliwonse wa pa chaka umabwera kumapeto ndi mbindikikilo wa mtundu wina wake, ndipo phunziro 12 limapereka dongosolo la mmene mungagwirire ntchito ndi uthenga opereka ku glu lanu danga loyang'ananso zonse zimene aphunzira mu chakacha, zonse zimene zachitika mwa inu ndi Mulungu, ndi kuyang'ana mtsogolo pamodzi kuti chotsatira ndi chiyani.

KUYENDETSA GULU

Limbikitsani gulu la anthu mpaka 12 (magulu akazi kapena amuna okhaokha amagwira bwino ntchito pa khalidwe lakuyang'anira ntchito pa khalidwe lakuyang'anira la mphamvu la maphunziro koma sizofunikira kwenikweni). Kukumana kamodzi pa mwezi kwa maora awiri. Nthawi iyi mtsogoleri wa gulu adzatsogolera phunziro - kuphatikizapo pemphero, kuphunzitsa, kukambirana ndi kudzionetsera mu chikhalidwe. Mlozo uwu ukupatsani inu chilichonse chimene mungafune kuti muyendetse gulu mwezi uliwonse kwa chaka choyamba.

MPHUNZITSI KAPENA MTSOGOLERI?
Mwina mukhoza kumadzifunsa ngati muli oyenera kutsogolera gulu la Msuntho izi ndi njira ziwiri zimene mungaganizire za mmene mungayendetsere gulu monga ngati mtsogoleri kapena ophunzitsa.

Atsogoleri kawirikawiri amakhala anthu amene ali ndi upangiri wakale wa kufalitsa komanso mkutheka alinso ndi upangiri wotsogolera ena powaphunzitsa ndi kukambirana.

Mphunzitsi ndi anthu amene akufuna kuti gulu la Msuntho liyambike ndiye kuti palibe mtsogoleri amene angayendetse gulu, amatenga udindo wowonetsetsa kuti zachitika ndi kutsogolera kuphunzira maphunziro a bukhuli mmalo mwa gulu (kapena kuvomereza kutuma ena mkati mwa njira).

Kaya mukabwera ndi upangiri wanu ku gulu kapena mukudalira bukhu la (Advance Group Guide), kutsogolera gulu la Msuntho kukudalira kudzikhuthula kwanu ku zolinga zenizeni kuposera china chilichonse ndi njira inanso. Ndi chofunikira kwambiri kwa gulu kumva ngati ndi anthu ochita zofanana mu upangiri umene ngakhale ndi osiyana mulingo wa upangiri wawo kapena chidziwitso chawo aliyense amakulira pamodzi ngati gulu.

KUGAWA PHUNZIRO
Mlozo wa phunziro lililonse likuyamba ndi chidule cha **kufotokozera phunziro**.

Gawo la **chiyambi cha phunziro** likuwonanso zomwe mukudziwa likupereka kuphunzitsa

kumene kwakhazikika pakamangidwe ka phunziro. Mudzafuna kuwerenga izi musanayambe kutsogolera phunziro pakati mudzathandizidwa ndi kumvetsa kwakuya kwa mapangidwe onse a phunziro. Masukani kugwiritsa ntchito bukhu ili mmaphunziro anu ngati muli ndi nthawi yochita choncho ndipo mukuganiza kuti zitha kuthandiza koma choyambirira liri pamenepa kukuthandizani kukonzekera kutsogolera kuphunzitsa zimene zikutsatila.

Kuchokera pano mutha kulondola mlozo ulionse wa phunziro, kuchokera pa zomwe mungachite mpaka pamene nthawi yoyikira zochitikayo yakwana (muma bracket amene ali mbali ya gawo lililonse la phunziro) molondoloza kapena mukuthandizikira pamene mfundo yeniyeni ya phunziro ikuperekedwa momveka bwino ndi mwadongosolo lowoneka bwino, ndipo pali mpata wa pemphero ndi kuchita khalidwe moyenera komabe, ndi nzeru zabwino kumatilila kufupi ku mlozo wa maphunziro ndi cholinga chakuti mutenge zabwino kwambiri mu bukhuli.

Phunziro lililonse likuyamba ndi kulandirana/ kukumbutsana za mbuyo. Mumaphunziro oyamba ichi chikukhudza kudziwana ndi kuwunikira njira zimene gulu lingayendere. Pamene maphunziro akupitilira, nthawi yambiri yaperekedwa yogawana nkhani komanso kuwuzana mmene zinakhalila kuchokera pomwe tinasiyana phunziro lapitalo zimene **tinapatsana kuti tikachite**.

Kenako ndi nthawi ya **Pemphero**. Palibe kulozera kuli konse kwa nthawi imene mungatenge popemphera komanso palibe kulondola kapena kulakwitsa mmachitidwe ake. Mukhoza kupemphera ngati gulu pamodzi kapena pachinzake, kwa nthawi yochepa kapena yayitali.

Gawo Lalikulu la **Kuphunzitsa** likutsatira komanso kuphatikiza kalozera wa mau a Buku **Lopatulika**, mawu otengedwa mu Buku Lopatulika ndi mfundo zokambirana. Iyi ndi nthawi imene maso anu ayenera kuyang'ana pa watchi kutsogoloko kuli nthawi ya zokambirana, komanso kofunikira kwambiri mudzafuna kusiya danga la gawo losonyeza khalidwe kumapeto a phunziro. Musalole nthawi imeneyo ifinyidwe podzikakamiza pa fundo ina yaying'ono yophunzitsa! (komanso onani kuti nthawi yoyikika ya gawo ili ikusiyana kuchoka kuphunziro lina ndi phunziro lina, choncho onetsetsani kuti chidwi chanu chili ku nthawi yoyikika ndipo sinthani molingana ndi zochitika).

Likatha gawo Lophunzitsa kuli gawo la zokambirana limene lili ndi mafunso angapo ndi mawu otengedwa kwina ogwirizana ndi mutu wa phunzirolo. Mwachidziwikile simungakhale ndi nthawi yokambirana chili chonse mugawo limenelo, koma tiyikamo zambiri zoposera zimene mungazifune ndiye mungathe kusankha ndi kutola zimene zili zothandiza kwambiri. Musamve ngati mukufunika mmalo mwake lunjikani pa zinthu zofunikira zochepa.

Gawo lililonse lili ndi gawo la zinthu zoti mukachite mmoyo wanu mutaphunzira kwa phunziro, chimene mukachite pakati pa phunziro la lero ndi la mwezi ukubwerawo. Masukani kuchita zanu zimene mwafuna mmakamaka zimene zikuthandiza kuphunzitsa ndi kuti zidzathandiza gulu kukula mudera limenelo.

Nthawi ina ya **pemphero** ikutsatira nthawi iyi motsogozedwa pa zimene mungapemphere muunikiridwa ndi phunziro, koma mmene mungachitire komanso nthawi yayitali bwanji zikhala ndi inu eni ake.

Pamapeto, phunziro lililonse limatha ndi nthawi ya udindo wa khalidwe lanu pamene kuwunikiranso mwapadera mogwirizana ndi maphunziro operekedwa pamodzi ndi masamba a kudziwunikanso kwatokha amene ayenera amalizidwe, kugawidwa ndi kupemphereperedwa. Pangani makope ena a mapepala kumboyo kwa mlozowu kapena kutenga pa internet (PDF Version) kuchokera ku advancegroups.org.

Ngati simunakonze kale tsiku la mkumano wotsatira, onetsetsani kuti mwachita izi musanamalize. Zidzakhala zophweka kulankhula za izi pamaso kuposera pa email patatha masiku angapo, ndipo potsazikana mupatsane zimene zili mu gawo la "Osayiwala..." limene limaphatikiza chinthu china chimene gulu lingachite pa website kapena zolembedwa zina za Msuntho zimene zingapezeke mkati mwa njira.

Magulu ambiri a Msuntho amatenga maora awiri akukumana pamodzi ndipo maphunziro a mu mlozo uwu akonzedwa ndi mulingo wa nthawi umenewo. Gawo lililonse mkati mwa maphunziro linapatsidwa nthawi pambali pake kukulondolerani inu nthawi imene itenge, koma masukani kusintha magawidwe a nthawi zimenezi, ndi kutalika kwa nthawi ya msonkhano

wa gulu lanu - kaya ndi yayitali kapena yayifupi - kukwaniritsa zosowa za gulu lanu.

ZOSANKHA ZOYAMBIRIRA ZA PHUNZIRO

Zinthu zotsatirazi zikhoza kukhala zowonjezera za pamwamba kwambiri ku nthawi za gulu zimene zili zaphindu kuthandizira ulendo onse umene mukuyendera limodzi.

PEMPHERO LACHINDUNJI

Khalani ndi nthawi yopempherera anthu ochepa mgululo mkati mwaphunziro lililonse – kupempherera miyoyo yawo, mabanja awo, utumiki ndi china chili chonse chimene anganene. Ngati muli ndi gulu lalikulu, mungathe kuyesera mukhoza kumachita izi kwa aliyense pa misonkhano itatu iliyonse kapena kuposera apo, kenako ndikuyambiranso.

NTCHITO YOYESERERA

Mukhoza kupita ku misewu kwa ora limodzi kuti mukayeserere zina mwa zokambirana ndi zopempherera zimene mugwiritse ntchito ku ntchito yanu yofalitsa kapena zina mwa zoyeselera zosonyeza kufalitsa. Magulu anapangidwa kutithandiza ife kuti tikonzekere ntchito yofalitsa, koma nthawi iperekedwe kukuyeserera kufalitsa ngati mungakonde. Onetsetsani zotsatila za zimene munakambirana mwachidule ndi kupereka maganizo anu za zimene zachitika.

ZOBWERA NDI ALENDO

Ngati mwapeza mwayi wokhala ndi munthu wapadera okuphunzitsani kapena mlendo amene atha kupereka maganizo awo ku nthawi zophunzitsa ndi zokambirana ndi kubweretsa upangiri wosiyanasiyana kapena china chake chatsopano ku gulu, ndiye kuti muwayitanane kuti agawane nanu ngati gulu.

ZOTHANDIZA KUTSINA KHUTU MMENE MUNGAYENDETSERE GULU

1. Konzani nthawi ya misonkhano ya magulu nthawi yokumana ikadali kutali zedi ndipo musunge masiku amene angati ofunikira kwambiri (mwina miyezi 6 kapena kuonjezera ngati ndi kotheka. Gwiritsani ntchito doodle.com ngati chida chogwiritsira ntchito.

2. WhatsApp signal, facebook, Messenger Telegram kapena china chilichonse chothandiza kupereka uthenga pa lamya kapena computer zimagwira ntchito bwino ngati njira yotumizira uthenga mwachangu, kupempha zopempheredwa ndi nkhani za chipulumutso isanafike nthawi ya msonkhano wa magulu. Onetsetsani kuti mwasankha chimodzi chimene aliyense ali nacho kugwiritsa ntchito momasuka ndipo ngati mtsogoleri wagulu, yesetsani kukhala wotsogolera zokambirana popereka maganizo anu kwambiri mmene mungathere. Gawanani nkhani zanu, afunse anthu zimene akufuna apempheredwe, perekani maina a mabuku, podcasts ndi you Tube clips. Ngati mutsogolera zochita ena onse adzachita nawo.

3. Chakudya chikhoza kukhala njira ina yayikulu yobweretsera anthu pamodzi ndi kulumikizana, mwina mukhoza kupanga maphunzirowa mukudya chakudya china chake.

4. Muyambitse gulu lanu kuti liyambe kuganizira zoyambitsa magulu awo kummayambiriro kwa maphunziro ndipo pamene mamembala a gulu abwera ena ndipo akuoneka othekera koma achedwa kwambiri kuti alowe gulu lanu, mungathe kuwalumikizitsa ndi magulu atsopano amene akhazikitsidwa kuchokera pa magulu anu amene alipo kale.

5. Kumanani mmalo amene aliyense atha kukhala omasuka kukambirana, kupemphera ndi kugawana za nthawi ngati mdindo wa moyo wake. Malo a chigulugulu monga malo odyera amakhala bwino kwa ena, koma ena amafuna podikha mphepo pamene akupanga izi, choncho muyenera kuganizira mosamala zamalo anu a msonkhano. Misonkhano yochitika kudzera pa computer monga ngati zoom kapena zofananirapo zingagwirenso bwino ntchito, makamaka pamene mamembala ali m'malo oti ndi ovuta kukumana, koma ngati kungatheke kukumana kwapamaso.

PHUNZIRO 1: MWALANDIRIDWA KU MSUNTHO

Msonkhano woyambirira wagulu ugwiritsidwe ntchito ngati mwayi woyamba kudziwana wina ndi mnzake ndi kukhazikizitsa malamulo akayendetsedwe ka gululi. Mkatikati mwa kudziwana pakhalanso kukambirana za kufalitsa uthenga ndi chiyani ndiponso kuunikirana machitidwe asanu amene akhale ofunikira pakugwira ntchito monga mlaliki.

KUFOTOKOZERA PHUNZIRO

Kupyolera mu maphunziro oyambirira khumi ndi awiri a Msuntho tidzakulira limodzi mukuunikirana makhalidwe asanu a mlaliki, kulimbikitsana ndi kupatsana zinthu zofunikira pamene tikudalira mphamvu za Mulungu pakugwira ntchitoyi.

CHIYAMBI CHA PHUNZIRO

Malo abwino olandiririra anthu pa ulendo wa Suntha ndikuyamba kukambirana za kufalitsa uthenga ndi kukumbutsana kuti mayitanidwe a mlaliki ndi a payekhapayekha. Mu buku la Marko (Marko 1:16-18) tiyeni tione mmene Yesu anaitanira Andreya ndi Petro kuti amutsate Iye. Anaitana msodzi wa nsomba pa gombe la Nyanja ndi kuwafunsa iwo asiye maukonde awo (msika wawo) ndi kumutsata Iye, pakuti tsopano awaphunzitsa mmene akhalire asodzi a anthu. Kodi Mulungu akadagwiritsabe ntchito mawu awa masiku ano? Pokhapokha ngati inunso muli msodzi ngati abale aja amene Yesu anawaitana ku utumiki. Yesu anaitana Andreya ndi Petro payekhapayekha, pakugwiritsa ntchito mwambi wa usodzi monga poyambira.

Mulungu amaitana aliyense payekhapayekha ku utumiki wake, amalumikiza luso limene tili nalo ndi kudikira nthawi yoyenera yakuzindikira kuti Mulungu ndi ndani. Kaya ndinu woyimba, wojambulajambula, wa sayansi, namwino, kuyendetsa bizinesi.... Kaya ndi luso lanji limene muli nalo, Mulungu amagwiritsa ntchito lusolo mu ntchito yake ndi nthawi yake yakuikika kuti mukalalike uthenga wabwino.

Cholinga cha kufalitsa ndicho kulumikiza anthu ku uthenga wabwino wa Mulungu. Uthengawu umankhala maitanidwe a chikhulupiriro mwa Yesu Khristu – kukhulupirira ndi kumumvera Iye, ndi kutembenuka kuchoka komukana Mulungu ndi kuyamba kuvomereza kuti akhale Ambuye. Tikadziwaa kuti tinalengedwa chifukwa cha Iye, ndi kuzindikira chimene timapembedza, ndi kukhala ndi mphamvu ya Mzimu Woyera mmoyo mwathu. Munthu wangwiro moyo wake ukatembenuka ndi kukhazikika pa kupembedza kupyolera pakumvera, kudzipereka, kukhulupirira ndi chikondi. (Agalatiya 5:13-26).

Mu Eksodo 8:1, Mulungu akuuza Mose kuti apite akalankhule ndi Farao, "Lola anthu anga amuke..." Chikhumbokhumbo cha Mulungu, masiku ano, ndi kumasula omangidwa ndi uchimo. Monga Mose, tikufunsidwa kupita ku dziko lapansi ndi kukalikira uthenga wa ufulu – kunena kuti palibe chifukwa kuti munthu akhalebe mgoli pakuti Mulungu anaonetsa kuthekera kuti ife tikhale a ufulu kudzera mwa Yesu ndi mphamvu za Mzimu wake (Aroma 8:2). Cholinga cha kufalitsa uthenga chili monga chinali mu nthawi ya Mose ndi ana a Israeli – Chipembedzo.

'Lola anthu anga amuke kuti anditumikire'

Tiyenera kukhala wopembedza komanso wochitira umboni kuti enanso atitsate mu chipembedzo ndi umboni.

MLOZO WA PHUNZIRO

KUKUMBUTSA ZA MBUYO (MPHINDI 20–30)

Khalani ndi nthawi yodziwana aliyense wina ndi mnzake. Iyi ikhoza kukhala nthawi yopuma pang'ono ndi kukhala ndi zinthu zina zoti gulu lichite kapena kufotokozerana mbiri ya aliyense payekhapayekha. Mukamaliza kambiranana za mmene gululi liziyendera malingana ndi zimene zafotokozedwa pa kayendetsedwe ka gulu ndipo liyenda bwanji gululi mmiyezi ukubwerayi.

PEMPHERO

Khalani ndi nthawi yakupereka gulu lonse la Msuntho ndi ulendo wake kwa Mulungu, ndiponso kuyikiza mmapemphero zosowa zonse zimene zadza mukukambirana.

KUPHUNZITSA (MPHINDI 20–30)

Gwiritsani ntchito zida izi zophunzistira mu njira imene ikhoza kukhala yosavuta kwa inu, pakuwerenga liwu ndi liwu kapena kupereka phunziro lanu.

> "Komatu sindiyesa kanthu moyo wanga, kuti uli wa mtengo wache kwa ine ndekha; kotero kuti ndikatsirize njira yanga, ndi utumiki ndinaulandira kwa Ambuye Yesu, kuchitira umboni Uthenga Wabwino wa chisomo cha Mulungu."
>
> **MACHITIDWE 20: 24**

Mwachidule, 'kufalitsa' kutanthauza kuti "kulalikira nkhani yabwino'. Nkhani yabwino ikunenedwa apa ndi ya uthenga wabwino wa Yesu Khristu: kuti munthu wochimwa (wowukira) wayanjanitsidwanso ndi Mulungu kupyolera mu ntchito yachipulumutso ya mwa Yesu. Tikhoza kudziwa za moyo wosatha lero ndi kunthawi zosatha, kukondweera ndi ubale wachiyanjanitso ndi Mulungu chifukwa Yesu anafa mmalo mwathu.

Tiyeni tione kumasulira kwina kwa Kufalitsa:

> 'Kufalitsa ndi kupatsidwa mphamvu ndi Mzimu Woyera kulalikira Uthenga Wabwino wa Yesu Khristu ku dziko lapansi lochimwa ndi chiyembekezo chakuti angathe kuvomereza chikhululukiro cha Mulungu ndi kukhala Ambuye, chikondi mmoyo, lero ndi ku nthawi zosatha.'

> 'Kulalikira mbiri ya Khristu wa mu Buku Lopatulika monga **Mpulumutsi** ndi **Ambuye**, ndi malingaliro okopa anthu kubwera kwa Iye **eni ake**, kuti **ayanjanitsidwe** ndi Mulungu.'
>
> **THE LAUSANNE COVENANT**

Funso: Kodi tikhoza kuphunzirapo chiyani pa kufalitsa kuchokera ku mau amene amasuliridwa (makamaka kukambirana mawu amene awalitsidwa)?

Kufalitsa kumafunika kupereka uthenga wa pakamwa, kuonetsa Yesu amene anauka, ndi kuyesetsa kukopa omvera kulandira ndi kuvomereza uthenga wabwinowo. Chofunikira kwambiri ndi mau amene tikufalitsa ndi kuyesetsa kuti uthengawo usangokhala wa pakamwa pokha.

Kufalitsa ndi ntchito ya uzimu, imagwira ntchito Mulungu akakhalamo ndi mphamvu zake.. Kufalitsa kukanakhala kuti ndi kungosintha malingaliro a anthu, bwenzi tikudalira ntchito yongokopa anthu chabe. Koma kwakukulu kufalitsa tikulankhula za chipulumutso: kupyolera mu uthenga wathu, Mzimu wa Mulungu kutitsutsa, kutipatsa chikhulupiriro, ndi kuyamba kutembenuza mitima yathu. Kufalitsa uthenga wopanda mphamvu ya Mzimu kumaoneka ngati kutsatsa malonda chabe. Kunena mu njira ina monga anafotokozera Mlaliki Leonard Ravehill – tikhoza kupatsidwa mphamvu kugwiritsa njira ina iliyonse ya kufalitsa pokhapokha Mulungu ayigwiritse ntchito.

Cholinga cha kufalitsa uthenga ndi kupanga ophunzira. – wopembepedza amene apembedza mu mzimu ndi mchoonadi (Yohane 4:23). Choncho alaliki akhalenso opembedza mchoona. Zinalankhulidwa kuti kupembedza ndi kufalitsa zili ngati mbali ziwiri za ndalama

ya chitsulo, ndipo zoonadi kuti kupembedza ndi mbali imodzi yakuchitira umboni ku dziko lapansi – kuonetsa mchitidwe womvera ndi wodzipereka kwa mfumu imene timayichitira umboni ku dziko lapansi.

Magulu awa a Msuntho adzatithandiza kukula monga wopembedza woonadi ndi kukuyang'anirani mukukula mmakhalidwe asanu oyenera Mlaliki.

ALALIKI – WOLALIKIRA BUKU LOPATULIKA

Tiyenera kudziwa mozama uthenga umene tikulalikira. Kuti tikwaniritse izi tiyenera kuwerenga ndi kuphunzira mozama mau a Mulungu, kuti uthenga umene tikulalikira usakhale wongochokera mmaganizo athu kapena mu zolinga zathu za uthenga wabwino, koma zikhale monga mau a Mulungu aphunzitsa.

ALALIKI WOPEMBEDZERA

Tiyenera kudzipereka kwathunthu ku mphamvu ya Mzimu Woyera pa ntchito imene kwa ife ya kufalitsa uthenga. pakuti simphamvu zathu koma ndi mphamvu za Mulungu zimene zibweretsa chipulumutso. Kotero kuti tidzikhutule pakukhala moyo wapemphero, kupempha Mulungu atipatse nthawi yoyenera kugawana ndi ena za chikhulupiriro chathu ndi kuwona zotsatira zosinthika mmiyoyo yathu.

ALALIKI AMENE ALI ADINDO WA MOYO WAWO

Chiyero ndicho chimene chili pa mtima wa uthenga wabwino. Kugawana ndi ena za mphamvu ya uthenga wabwino wakusintha anthu mu njira ya choonadi ndi kukhala adindo a moyo wao, amene sasintha makhalidwe awo, 'akakhala pa gome' zifananenso ndi 'akachoka pa gome'. Kulimbikitsana pamene zinthu zikuyenda bwino ndi kugwirana manja pamene zisazikuyenda ndipo izi ndi zofunikira kwambiri pamene tikusinkhasinkha kukula monga anthu oyera mtima ndi kugawana uthenga oyera wa Mulungu (Mlaliki 4:9-12, Miyambo 27:17, 1 Atesalonika 5:11, Yakobo 5:16).

ALALIKI ODZIPEREKA

Kufunitsitsa kuchita chinthu ndiye fungulo wa kufalitsa uthenga (Machitidwe 17:30). Tiyenera kudziwa kuti - mugwiritse- tsiku lirilonse liri ndi nthawi yoyenera kugawana ndi ena za chikondi cha Mulungu, osati kungogawana za mbiri ya Yesu koma kuitana omwe amva za mbiri yake kuti akadze mmoyo watsopano umene ukuperekedwa, ndi kuwathandiza kuyamba ulendo wophunzira a Buku Lopatulika.

ALALIKI A CHILIMBIKITSO

Pamene tikugawa uthenga wabwino pa dziko lapansi kwa iwo amene akuwusowa, tiyenera kulimbikitsa mpingo kuti uchitenso chimodzimodzi. Kufalitsa uthenga ndi ntchito ya Mkhristu aliyense ndipo ilimbikitse ndi kutakasa mpingo kuti udzipereke pa ntchito imeneyi ndiponso ikhale ntchito yodzipereka ya Mlaliki amene ali ndi mphatso ya kufalitsa, kufunitsitsa kuchitira umboni uthenga wabwino ku mpingo ndi kuti mpingo ukakhale chiyembekezo choonadi cha dziko lapansi ndi kukwaniritsa utumiki wa Khristu (Ahebri 10:24-15).

Funso: Lingarirani makhalidwe asanu awa. Kodi ndi mbali iti imene mukuwona kuti kuli mphamvu zanu komanso ndi mbali iti imene mukowona kuti muli wofooka?

KUKAMBIRANA (MPHINDI 15)

Dzifufuzeni pa mafunso otsatirawa/ kapena kukambirana mau amene ali mu koteshion maliki:

1. Kodi mbali yanji imene tili nayo pa kufalitsa uthenga nanga Mulungu ali ndi mbali yanji?
2. Ndingaonetsetse bwanji kuti tikhale Alaliki woonadi ndi opembedza wowonadi?
3. Mukuyembekeza kukula bwanji mmiyezi ikubwerayi kudzera mu gulu la Msuntho?

"Ngati ochimwa adzatayidwe, iwo adzaponyedwa ku gehena pamutu pathu. Ndipo ngati adzaponyedwa ku chionongeko, iwo adzaponyedwa ndi manja athu atagwada ndi maondo kochondelera kuti asakhalemo. Ngati gehena ikhale yodzadza, idzadzadzidwa ndi okukuta mano, ndipo asapite asanachenjezedwe ndi kupemphreredwa."

CHARLES SPURGEON

ZOCHITA MMOYO WANU MUTAPHUNZIRA (MPHINDI 5)

Lembani pogwiritsa ntchito Buku Lopatulika tanthauzo la kufalitsa (gwiritsani ntchito ndime za mu Buku Lopatulika) ndi kutumiza ku gulu lanu kupyolera mu njira ina iliyonse a masamba a mchezo (WhatsApp, Facebook, email, ndi zina zambiri). Cholinga sikuti mulembe mau abwino kwambiri, koma kuti mukaonetse kumvetsetsa tanthauzo la kufalitsa ndi kulingalira pa zimene mumaphunzira. Nthawi ikapezeka mu phunziro lina mungathe kukambirana mwatsatanetsatane za matanthauzowo pagulu lanu.

PEMPHERO

Yamikani Mulungu chifukwa cha uthenga wabwino wodabwitsa. Yamikani Iye kuti wasankha inuyo kutenga nawo gawo mu utumiki wake pa dziko lapansi. Pempherani kuti akupatseni mphamvu kuti mukhale mtumiki wake mu mzimu ndi mchoonadi. Mupempheni iye akuthandizeni kukula ndi makhalidwe asanu a mlaliki pamene mukupita chitsogolo ndi gulu la Msuntho.

KUKHALA MDINDO WA MOYO WANU (MPHINDI 15)

Fotokozani za mmene mafomu a kukhala mdindo wa moyo wanu angagwire ntchito, lembani ndi kugawana anthu awiriawiri pa gulu lanu. Tsirizani mwa kupemphererana wina ndi mnzake.

MAUTHENGA NDI MASIKU (MPHINDI 10)

Tsekani phunziro loyamba pa kufunsa aliyense kukhala ndi tsamba la mchezo limene mungagwiritse ntchito mosavuta pagulu lanu (WhatsApp, facebook). Khalani ndi gulu limene mukhoza kumalankhulana pa masamba a mchezo amenewa pakati pa maphunziro anu, kuwuzana za zimene zikuchitika, kupatsana zopempherera, kupereka ma umboni ndi zina zambiri.

Pomalizira, khazikitsani masiku amene mungathe kuphunzira maphunzirowa. Kukhala okonzekeratu kwa miyezi isanu ndi umodzi kuti aliyense athe kukonzekera masikuwo mu nthawi yoyenera ndi kuti chikhale chinthu chofunikira pa moyo wake.

OSAIWALA...

Aliyense amene ali mu gululi alembetse pagulu la Msuntho pa www.advancegroups.org ndi kulandira makalata apa computer (email) mwezi uliwonse a zimene zikuchitika ndiponso kulandira nkhani za chilimbikitso kuchokera ku gulu la Msuntho pa dziko lonse lapansi, komanso ndi chida chofunikira kuthandiza pa maphunziro ndi kumvanso nkhani zatsopano.

POLEMBA

PHUNZIRO 2: CHIZINDIKIRO CHA MLALIKI

Mukukumana kwathu kwachiwiri muyang'ana za chizindikiro cha Mlaliki molumikizitsa ndi chizindikiro cha Mulungu mwini ndi mbiri ya uthenga wake wabwino.

KUFOTOKOZERA PHUNZIRO

Chizindikiro cha Mlaliki chayima pa chizindikiro cha Mulungu, Atate: ife ndife ana ake onyamula uthenga wake.

CHIYAMBI CHA PHUNZIRO

Utumiki wa Billy Graham utafika pa chiindeinde, a chinyamata a chikhristu analakalaka mtima wotengera chitsanzo chake ndi kukhala alaliki a uthenga wabwino. Kwa zaka makumi awiri zapitazi zaoneka kuti panabwera mphepo yosintha pa zolakalaka za achinyamata a Chikhristu. Pamene ntchito ya mlaliki imaoneka ya pamwamba zedi mu utumiki wa Chikhristu, koma masiku ano achinyamatawa akulakalaka kukhala wotsogolera kupembedza, kukhala mtsogoleri wa achinyamata kapena kukhala mbusa.

Mpingo wapindula koposa kuchokera luso la woyimba nyimbo, wopanga makanema ndi ena ambiri a maluso osiyanasiyana amene athandizira ena kupemphera ndi kupembedzera pa mpingo, ndipo akukondwerera ndi kumkweza Mulungu kupyolera mwa anthu okhulupirika. Koma, munthu asanakhale wopembedza woonadi – wopembedza mu mzimu ndi mchoonadi (Yohane 4:23) – ndiye kuti anamvapo ndi kuvomereza uthenga wabwino (Aroma 10:14-17).

Chimodzimodzi, ntchito ya mbusa kapena mphunzitsi ndi yofunikira pakupanga ophunzira. Koma, mbusa sangathe kukhala ndi gulu la anthu limene angasamalire ngati iye satumikira ndi kulalikira ku dziko lapansi.

Kubweretsa anthu ku chipembedzo choonadi zifunikira ife kufotokozera uthenga wabwino kwa iwo, ndipo ndi malingaliro amenewa wina aliyense wa ife tisachite ukamberembere pa udindo wathu wakugawana ndi ena nkhani yabwino ku dziko lapansi, pakuchitira umboni za chikhulupiriro chathu mwa Khristu kwa onse ndi mphamvu ya Mzimu (Machitidwe 1:8). Buku Lopatulika likuphunzitsa kuti onse anaitanidwa kukachita ntchito ya Mlaliki (Mateyu 28:19; 2 Timoteo 4:5), komanso alipo ena amene anaitanidwa mwapaderadera akhale alaliki (Aefeso 4:11). Makamaka kwa iwotu, akulalika uthenga wabwino pakuti achitira umboni tsiku ndi tsiku, komanso kulunjika pa miyoyo yawo.

MLOZO WA PHUNZIRO

KUKUMBUTSA ZA MBUYO (MPHINDI 20–30)

Mukhale ndi nthawi yakukokera amene akutsalira mbuyo kuti ayendere limodzi ndi anzawo, kugawana nkhani, kulimbikitsana, kukonzana ndi kuuzana zolimbikitsa gulu. Funsani gulu ligawane mau ofotokozera za Kufalitsa kuchokera mu Buku Lopatulika (Phunziro 1; Pa Zochita mmoyo wanu mutaphunzira) ndi kukambirana pa gulu mokumbutsira phunziro la mbuyomu. Gawanani magulu ang'onoang'ono. Izi zimathandizira ena amene sanathe kukhala nawo pa phunziro loyamba.

PEMPHERO

Dzipatulireni nthawi kwa Ambuye ndi kupempherera zomwe zikuchitika, zabwino kapena mavuto, ochokera pa gawo la kukokera otsalira kukhala limodzi ndi anzawo.

KUPHUNZITSA (MPHINDI 20–30)

Gwiritsani ntchito zida izi zophunzistira mu njira imene ikhoza kukhala yosavuta kwa inu, pakuwerenga liwu ndi liwu kapena kupereka phunziro lanu.

> 'Ndikuchitira umboni pamaso pa Mulungu ndi Khristu Yesu, amene adzaweruza amoyo ndi akufa, ndi pa maonekedwe ake ndi ufumu wake; lalikira mawu, chita nawo pa nthawi yache popanda nthawi yache; tsutsa, dzudzula, chenjeza, ndi kuleza mtima konse ndi chiphunzitso. Pakuti idzafika nthawi imene sadzalola chiphunzitso cholamitsa; komatu poyabwa m'khutu adzadziunjikitsa aphunzitsi monga mwa zilakolako za iwo okha: ndipo adzalubza dala pa choonadi, nadzapatukira kutsata nkhanu zachabe. Koma iwe, khala maso m'zonse, imva zowawa, chita ntchito ya mlaliki wa Uthenga Wabwino, kwaniritsa utumiki wako.'
>
> **2 TIMOTEO 4:1–5**

Kodi chitanthauzanji *kuitanidwa* kukhala mlaliki? Kodi si onse okhulupririra aitanidwa kugawana nkhani yabwino ya Yesu Khristu ku dziko lapansi? Yesu pa Mateyu 28 analamula onse otsatira iye kuti apite ku dziko lapansi akapange ophunzira. Koma pa Aefeso 4 (ndime 11-12) ikufotokoza makamaka ntchito ya mlaliki pamodzi ndi mbusa, mphunzitsi, mneneri ndi mtumwi, kuti onse agwritsidwe ntchito mu thupi la Khristu. Tikukumananso ndi munthu wotchedwa Filipo mu Buku la Machitidwe amene anapatsidwa ntchito yapadera ya Mlaliki (Machitidwe 21:8). Ndiye tikuti bwanji za maitanidwe a Mlaliki? Kodi akuitana aliyense kapena alipo ochepa apaderadera?

Mukhoza kudziwa mau opezeka pa 2 Akorinto 5:17, pamene Paulo akulankhula za kulengedwa kwatsopano mwa Yesu. Mwinanso inuyo mwagwiritsapo ntchito ndimeyi mbuyomu pakugawana ndi ena uthenga wabwino. Koma, nthawi zambiri sitimagwiritsa ntchito mau onse ali pa ndimeyi:

> 'Chifukwka chake ngati munthu aliyense ali mwa Khristu ali wolengedwa watsopano; zinthu zakale zapita, taonani, zakhala zatsopano. Koma zinthu zonse zichokera kwa Mulungu amene anatiyanjanitsa kwa Iye yekha mwa Khristu, natipatsa utumiki wa chiyanjanitso; ndiko kunena kuti Mulungu anali mwa Khristu, alinkuyanjanitsa dziko lapansi kwa Iye yekha, osawawerengera zolakwa zawo, ndipo anaikiza kwa ife mau a chiyanjanitso. Chifukwa chake tiri atumiki mmalo mwa Khristu, monga ngati Mulungu alikudandaulira mwa ife; tiumiriza inu m'malo mwa Khristu yanjanitsidwani ndi Mulungu.'
>
> **1 AKORINTO 5:17–20**

Funso: Kodi ndimeyi ya mu Buku Lopatulika ikutitsimikizira bwanji kapena kusintha motani za tanthauzo la kufalitsa limene tinakambirana poyamba paja mu phunziro la lero?

Mulungu ali otanganidwa kuyanjanitsa wolengedwa ake kwa Iye mwini ndipo akutifuna, tikhale anthu oyanjanitsidwa, kukhala akazembe onyamula uthenga wa kusinthika kwathunthu. Ntchito iyi si ya alaliki okhawo 'amene ntchito yao ndi ya ulaliki', awa ndi maitanidwe a onse amene ali okhulupirira. Komatu, ukazambe umenewu umakhala wosiyana kwa aliyense.

Tiyeni tilingalire motere: mu timu ya mpira, wosewera aliyense amakhala ndi cholinga chopambana pa masewerowo. Koma, wosewera kutsogolo ndi amene amapatsidwa ntchito yochinya zigoli. Izi sizitanthauza kuti wosewera enawo sikuti sangathe kuchinya, koma ntchito yofunikira kwambiri mu timu ndi ya osewera kutsogolo kuti azigoletsa.

Chitsanzo china chimene chingatithandize ndicho cha ukwati. Woitanidwa aliyense amene ali ndi phone za makono akhoza kujambula chithunzi chooneka bwino ndi kusunga zokumbukira za tsikuli, ndipo zina mwa zinthunzizo za akwatiwo akhoza kuzisunga mu bukhu la zithunzi (album). Pamene, mkwati ndi mkwatibwi akhoza iwo kuitana mwa paderadera katswiri wodziwa kujambula kuti adzajambule zinthunzi za tsiku lawoli. Pakugwiritsa ntchito luso lake, zida zake, ndi kujambula zinthunzi zooneka bwino kwambiri.

Monga mpingo ife tonse tifunefune cholinga chakubwezeretsa Ufumu wa Mulungu. Pa chifukwa ichi, ife tonse tili ndi gawo lakuchitira umboni ndi kufalitsa uthenga. Koma alipo ena amene anaitanidwa mwa padera kuika patsogolo kulalikira uthenga wabwino. Awa ndiwo alaliki monga Filipo amene tawerenga pa Machitidwe 21:8.

Ngati ziganizo zili munsimu zikumveka moona kwa inu ndiye kuti maitanidwe a mlaliki akhoza kukhala mmoyo wanu:You long to see the lost saved.

- Mukufunitsitsa kuona otaika akupulumutsidwa.
- Mukukopedwa kulalaikira uthenga wabwino mu nyengo ya kututa ndiponso nyengo yopuma.
- Kupirira pa ntchito yake ngakhale mutakumana ndi zovuta kapena zokhumudwitsa.
- Osataya chiyero cha Uthenga wabwino pa kulalikira uthenga wosangalatsa makutu a omvera ndi zimene afuna iwo.
- Muli ndi lingaliro lakufikira anthu otaika ndi uthenga wamphamvu, wakusintha kwathunthu moyo wawo, ndi kupulunutsa moyo wawo.
- Mwamvapo mau a ulosi wanu wakuti mukhale mlaliki.
- Mumatha kulankhula momveka bwino.
- Nthawi zambiri mumapezeka mukupempherera otaika.
- Muli ololera kupita kwina kulikonse kukalalikira uthenga wabwino.
- Mulakalaka kuthandizira kugawana chikhulupiriro chawo.

Funso: Khalani ndi nthawi yokambirana ziganizo zimenezi kuti kodi zina mwa ziganizozi zikumveka moona kwa inu. Ngati pakati panu alipo alaliki afunseni agawane nanu kuti anazindikira bwanji za mphatso yawo ndi gawo lawo.

Buku Lopatulika likutiuza kuti Mulungu akufunitsitsa kuti wina aliyense asatayike (2 Petro 3:9). Mlaliki akhale ndi makopedwe wopita ku dziko lapansi ndi kukhala ndi mtima wonga wa Atate. Sitilalikira chifukwa chakuti mtima wathu uli ngati wa Atate. Chizindikiro cha mlaliki sichionekera pa ntchito yake, koma pakuti ali mwana wa Mulungu, ali mlowa malo kupyolera mwa uthenga wabwino umene tilalikira (Yohane 1:12).

Angakhale tili ndi mphatso kapena maitanidwe, palibe amene ali ndi mphamvu yakudzipulumutsa yekha. Koma kuti tikhale ife a mithenga pakuti ndi Mulungu yekha amene apulumutsa. Atiyitana ife kugawana mtima wake kuti otaika akakule pakumudziwa Iye kwatunthu monga Atate wathu wokondwedwa ndi kuvumbulutsa mphamvu zake ku dziko lapansi.

KUKAMBIRANA (MPHINDI 20)

Dzifufuzeni pa mafunso otsatirawa.

1. Kodi pali kusiyana pakati pa kuchitira umboni ndi kufalitsa uthenga?
2. Ngati onse akuyembekezeka kugwira ntchito ya mlaliki, nanga ndi chifukwa chiyani ena achita kuitanidwa kuti akhale alaliki?
3. Mlaliki kapena ayi, ndingachite bwanji kukhala ndi mtima wonga Atate kwa iwo amene ali wotayika.
4. Kodi mungathandize bwanji kulimbikitsa iwo amene amaganiza kuti kufalitsa uthenga ndi ntchito ya alaliki okha ndi kukhala ‘atumiki oyanjanitsidwa’.

ZOCHITA MMOYO WANU MUTAPHUNZIRA (MPHINDI 5)

Sitigawa uthenga wabwino chifukwa chakuti ndife ‘alaliki’ ngakhalenso iwo amene sanaitanidwe kukhala ‘alaliki’ ndi kuwaletsa kugawa uthengawo. Onse okhuluprira ayenera

kugawa kwa ena uthenga wabwino ndi kuvomereza mmene Mulungu aliri ndi zimene amachita. Pamene tili wosinthika kwatunthu ndi chikondi cha Atate, choncho tikhale ndi chikhumbokhumbo kwa ena kuti adziwe za chikondi chosinthachi.

Mwezi ukubwerawu, tiwerenga buku la uthenga wabwino wa Marko mu nthawi ya mapemphero kuwunikirana mitu ikupezeka mu Bukhu La Marko – Yesu Mwana wa Mulungu, mtumiki amene anadza kudzachita chifuniro cha Atate. Pamene mukuwerenga ndi kubwerezanso uthenga wabwino mukhale ndi malingaliro, akufunsa Mulungu kuti akuwuenetsereni chizindikiro, osati mwakuyang'ana mphatso kapena maitanidwe anu, koma kuti mukaone kuti Iye ndani ndi zimene Iye wachita.

PEMPHERO

Yamikani Mulungu, Atate wathu wa kumwamba, amene safuna ngakhale ndi mmodzi yemwe akatayike ndi anaika njira kuti onse akapulumutsidwe mwa Yesu Khristu. Khalani ndi nthawi yakupemphererana wina ndi mnzake kuti Mulungu akakupatseni kuzindikira maitanidwe a Mlaliki, kuti akapereka danga lakugawa uthenga wabwino, ndi kuti mukakhale ndi mphamvu ya ntchitoyi.

KUKHALA MOYO WA UNGWIRO (MPHINDI 15)

Khalani awiriawiri kapena mmagulu ang'onoang'ono, funsanani mafunso pakuyerekeze kuti ndinu Mlaliki ndipo ndinu woyenera kugwira ntchito imeneyi ya Mlaliki. Cholinga chake apa ndi kukopa mnzanu kuti akhale ngati inu, kulingalira za maitanidwe a Mulungu mmoyo wanu, ndi kuti zitanthauzanji kukhala okhulupirika kufotokozera za uthenga wabwino pa mabwalo a Mulungu amene alipo. Pomaliza, lembani mu fomu ya Kukhala moyo wa ungwiro, ndi kukonzana wina ndi mzake ndi kupemphererana.

OSAIWALA...

Pali zinthu zosangalatsa mkatikati mwa Alaliki amene ali akatswiri, 'Chinthu chimodzi', pamene mlaliki adzafotokoza za chinthu chimozi chimene amalakalaka akadadziwa asanayambe kulalikira uthenga wabwino. Werengani ndi kulimbikitsidwa pa advancegroups.org.

POLEMBA

PHUNZIRO 3:
UTHENGA WA MLALIKI

Mu phunziro ili tiunikirana a nkhani imene umapezeka mu uthenga wabwino. Kodi Uthenga wabwino ndi Chiyani? Kodi tili ndi kumvetsetsa kokwanira za uthenga umene timalalikira momveka bwino?

KUFOTOKOZERA PHUNZIRO

Nkhani yayikulu ya kulalikira ndiyo Yesu Khristu. Khristu anadza, Khristu wopachikidwa, Khristu wodzuka kwa akufa, Khristu wokwera kumwamba.

CHIYAMBI CHA PHUNZIRO

St Augustine wotchuka analengeza, 'Haa Ambuye mwatipanga ife kukhala anu ndipo mitima yathu ndi yosakhazikika kufikira itakhazikika mwa inu.

Uthenga Wabwino umasuntha nkhawa. mdima, kusweka mtima, ndi kutaya chiyembekezo cha munthu kupita ku chimwemwe, kuwala, chikondi ndi chiyembekezo. Uthenga umasuntha mitima yosakhazikika kufika pa chikwaniritso cha mlengi. Koma mwangozi, zikuoneka kuti otsatira ambiri a Yesu lero ataya chikhulupiriro mu mphamvu ya uthenga wabwino. Pali zifukwa zambiri zomwe okhulupirira sakugawa uthenga wabwino kwa ena – mantha, kudzimva kusafunikira, ndi kuyembekezera kuti pali ena omwe agwire ntchito kapena kutenga nawo gawo. Choonadi chake, zifukwa zonsezi muzu wao ndi umodzi – kusamvetsetsa kuti uthenga wabwino ndi chiyani kwenikweni ndi kusowa kudalira mphamvu yake.

Mu Aroma 1, Paulo akulengeza kuti, 'Uthenga wabwino sundichititsa manyazi' ndipo akupitiriza ndi kofotokozera chifukwa chiyani izi ziri choncho: 'Pakuti ndi mphamvu ya Mulungu yakupulumutsa munthu aliyense wakukhulupirira' (Aroma 1:16). Kumvetsetsa kuti uthenga wabwino ndi mphamvu ya Mulungu kubweretsa chipulumutsso ndiko kumvetsetsa chinthu china kuti Mulungu ndi ndani, zimene Iye wachita, ndipo izi zitanthauza chiyani ku dziko lapansi. Izi zikukulungidwa kwenikweni kuti Yesu ndi ndani. Koma ichichi sichikuchotsedwa kapena sinzeru ya umunthu yopanda kupindula nayokuposera mchipinda chophunzitsira kapena chipinda cha mtsutso lingaliro lochokera mu holo ya maphunziro kapena mkalasi ya mtsutso. Chinthu chimodzi ndicho, kumvetsetsa uthenga wabwino kutithandiza ife kuyankha mafunso a za kupezeka kwathu ndi chizindikiro cha Mulungu chimene anatilenga ife. Mafunso monga:

NDINE NDANI?
Aliyense mnjira ina amadzifunsa funsoli, Kodi moyo utanthauzanji? Uli ndi cholinga chotani? Kodi chizindikiro changa ndi chiyani? Yankho lake ndi kuti ndinu mwana wa Mulungu, wolengedwa ndi kukondedwa ndi Iye. Lero pa dziko lapansi, choyambirira munthu sakhala wokhudzidwa kwambiri kuti ndikamwalira chidzachitika ndi chiyani, koma kuti kodi ndine ndani pamene ndikukhala mmoyo uno.

KODI MULUNGU NDANI?
Pali zipembedzo zochuluka pa dziko lapansi. Ngakhale kuti Mulungu alipo, tingadziwe bwanji kuti iye ndi ndani nanga kuti tikupembedza woyenererayo? Mulungu anadzionetsera yekha kupyolera mu chilengedwe, kupyolera mu Buku Lopatulika, kupyolera mu zochitika za akhristu mu dziko lonse lapansi, ndipo kupyolera mwa Yesu Khristu. Iye ndi mlengi ndi mwini wa moyo, mfumu ya dziko la mwamba ndi pansi pano, wolungama ndi Atate wa kumwamba amene afunitsitsa kubweretsa munthu wosweka ndi woukira kuti akayanjane ndi iye mwini.

KODI YESU NDANI?
Munthu wofunika ndi wachikoka mu mbiri zonse za munthu. Ndi akadaulo ochepa amene amakaikira zakupezeka kwake kwa Yesu, koma iye anali ndani? Wochenjeretsa? Wamisala? Ndithudi, Yesu ndi iye amene ananena za Iye aliri; Mpulumutsi wa dziko lapansi, amene kupyolera mmoyo wake, imfa ndi kuukanso kwa akufa, zinachititsa munthu akathe kukhala mwana wa Mulungu ndi kudziwa Mfumu ya moyo wosatha.

Mafunso ngati awa akhoza kukhala poyambira kukambirana kwa uthenga wabwino. Ngakhale kuti satitsogolera kumvetsetsa kwatunthu za tanthauzo la uthenga wabwino. Koma, ndi fundo zimene zitilumikizitsa ndi kutha kuyamba kupanga ubale. Choncho tiyenera tizame mu mmalembo ndi kuonetsetsa kuti kupyolera mu mafunso amenewa tikathe kufikira kwathunthu ndi mphamvu za uthenga wabwino wa Yesu Khristu.

MLOZO WA PHUNZIRO

KUKUMBUTSANA ZA MBUYO (MPHINDI 15–25)

Mukhale ndi nthawi yakukokera amene akutsalira mbuyo kuti ayendere limodzi ndi anzawo, kugawana nkhani, kulimbikitsana, kukonzana ndi kuuzana zolimbikitsa gulu. Funsani gulu ligawane mau ofotokozera za Kufalitsa kuchokera mu Buku Lopatulika (Phunziro 2). Gwiritsani ntchito nthawiyi kufufuza ndi kutsimikiza chizindikiro chenicheni monga ana a Mulungu chifukwa cha kutumikira mu ntchito ya Mwana wosatha wa Mulungu, koposa kuitanikdwa ku utumikiwu, ndipo kuyankha kwathu kukhale ku chizindikirochi ndiko kuchita Utumiki wa chiyanjanitso kuimira abale. Tithange tafuna otayika kuti iwonso azindikire kuti akhoza kubwerera kwawo.

PEMPHERO

Perekani nthawi kwa Ambuye ndi kupempherera mavuto amene tikumana nawo amene atchulidwa mu nthawi ya Kukokera otsalira kuyendera pamodzi.

KUPHUNZITSA (MPHINDI 25–35)

Gwiritsani ntchito chidachi munjira yanu, kaya muzingowerenga liu ndi liu kapena kupereka phunziro lanu.

> "Ndipo ine abale mmene ndinadza kwai inu, sindinadza ndi kuposa kwa mau, kapena kwa nzeru, polalikira kwa inu chinsinsi cha Mulungu. Pakuti ndinatsimikiza mtima kuti ndisadziwe kanthu mwa inu, koma Yesu Khristu ndi iye wopachikidwa."
>
> **1 AKORINTO 2:1-2**

Paulo akuonetsa kudzipereka kwake ku choonadi ndi mphamvu mu mbiri ya Yesu pa kulengeza kuti, 'Ndinatsimikiza mtima pamodzi ndi inu kuti ndisadziwe kanthu koma Yesu ndi iye wopachikidwa.' Uwu ndi mtima wa uthenga wabwino; kuti Mulungu iye mwini analowa mu chivundi cha dziko lapansi mwa munthu Yesu Khristu, amene anakhala moyo wolungama, nafa mopachikidwa pamtanda imene timayenera kulandira, nauka kwa akufa atakhala mmanda masiku atatu, kuphwanya temberero la imfa kwa onse. Chipulumutso ndi moyo wachilungamo zimapezeka kupyolera mu chikhulupiriro mwa iye yekha. Tigawana za choonadi ichi osati kungobweretsa kusintha mmaganizo, koma kuti kubweretsa moyo watsopano – kusintha kwathunthu kumene kungatheke mwa chikhulupriro mwa Yesu Khristu.

Funso: Zambiri za phunziroli zikhala zofufuza kuti uthenga wabwino ndi chiyani. Gwiritsani ntchito magawo (amene akupezeka kumbuyo kwa mlozuwu) kuyatsa kukambirana za zimene timakhulupirira kuti uthenga wabwino ungakhale chiyani.

ZIPHUNZITSO ZA UTHENGA WABWINO (TSAMBA 64)
Mayalidwe olongosoka a uthenga wabwino.

KUSIMBA UTHENGA WABWINO (TSAMBA 65)
Kunena mwamphamvu, uthenga umene ukunenedwa pano uli ndi kayalidwe kake, koma apa akutsindika kwenikwnei za kulongosola bwino monga mwa kuwerenga nkhani.

CHITSANZO CHA KULANKHULA UTHENGA WABWINO KWA ACHINYAMATA (TSAMBA 66)

Pali kulongosola kosiyanasiyana kwa uthenga wabwino ndi njira zake zokhazikika bwino, ili yonse ndi cholinga chake kuti uthenga ufotokozedwe ndi kuyika mu phukusi labwino kuti wina akaulandire momveka bwino.

Kuonetsetsa kuti tikukakamizidwa kulengeza choonadi cha uthenga wabwino. Kumbukirani kuti, sitingatumikire wina, uthenga wabwino ndi mphamvu ya Mulungu yakubweretsa chipulumutso (Aroma 1:16). Ngati uthenga wabwino uthiriridwa madzi, ndi kulimbikitsa mtima omvera, tingathe kuona manja ambiri akukwezedwa mwamba 'kuvomereza' uthengawo, koma kuti iwo akuvomereza chiyani kwenikweni?

Uthenga wabwino umabwera ndi maganizo ovuta kwambiri. Umatiuza kuti ife tonse ndi 'ochimwa' ndipo likunenanso kuti ndife anthu ophwanyika amene tiyenera kulandira imfa. Nkhani yabwino ya uthenga wabwino ndi yokoma chifukwa umavomereza kuti mmene munthu aliri kuti ndi oipa kwambiri.

Maganizidwe athu pa za Mulungu wachikondi ndi wachisomo aima pa mavuto amene tilingalira tchimo lathu mmene lili. Anthu ambiri amalimbana ndi ganizo la Mulungu amene aweruza ife chifukwa cha tchimo ndiponso lingaliro la Mulungu wokonda olola anthu kupita ku gahena. Ndi chinthu chophweka kulankhula maganizo otere mu uthenga wabwino, kapena kungowusiyiratu, koma izi sizingathandize. Kufalitsa kwathu kuli ndi udindo waukulu kuti timasule vuto la tchimo kuti mphamvu ya mtanda ndi chiyembekezo chachipulumutso zikamveke bwino monga mmene zili- chisomo chopambana cha Mulungu chopatsidwa kwa ana ake okondedwa ndi chiyembekezo chokhacho cha munthu.

Tchimo ndi vuto lalikulu limene limathetsedwa ndi Mulungu wamkulu. Kuchepetsa chimodzi cha maganizo ndi kupeputsa maonekdwe a ena, ndipo tiyenera kudzipereka ku choonadi ngakhale titajhala ndi zotsamwitsa.

Gawo lina limene lingaphonyedwe ndi ganizo lakuti tiyenera kufa ku kudzikundikira, ndi kutenga mtanda wathu ndi kutsatira Yesu mzonse tili nazo (Mateyu 16:24). Kuitanidwa ku moyo umene uli nsembe imene imagwiritsidwa ndi kukonderedwa ndi uthenga wakuti 'Mulungu adzakupangani kukhala wokondwa'. Komanso, ngati tionjezera za ife eni, kapena kudalira luso lathu kubweretsa anthu zotsatira zake ndi kutembenuza uthenga wabwino umene umayenera kukhala wa mphamvu wa kupulumutsa miyoyo, kuoneka wosakhala bwino konse.

Lero m'badwo wa achinyamata umakhudzika kwambiri ndi mafunso a 'zochitika tsopano' monga cholinga, chizindikiro, ndi chilungamo, kuposa 'zimene sizinachitike' ganizo lakuti chimachitika ndi chiyani tikamwalira. Izi zikuunikira za kufunikira kuti nthawi zonse tizinndikire kuti pakupereka uthenga wabwino tisaphonye mafunso amene anthu amafunsa. Phukusi la uthenga limasintha molingana ndi nyengo yake, koma choonadi chake sichisintha. Kuti tikalankhule za uthenga wabwino moyenera wolumikiza anthu, tiyenera kudziwa uthenga wabwinowo mozama ndithu ndi kuupereka momveka bwino. Kulalikira uthenga wabwino woperewera utitsogolera kwa Akhristu onyenchera choncho sitikufuna kuitana anthu okhala ndi maganizo kapena malangizo a pamwamba, koma kuti uthenga weniweni wa Yesu Khristu ukamveka bwino kwa munthu kapena anthu mwa mphamvu ya Mzimu.

Kuika patsogolo kuphunzira Buku Lopatulika ndi chinthu chofunikira kwa okhulupirira onse. Koma makamaka kwa iwo amene alalikira choonadi nthawi zonse. Tinganene bwanji kuti tili ndi chivumbulutso cha malembo ngati sitikudzidyetsa mmoyo wathu tsiku ndi tsiku? Tinaitanidwa kukhala Alaliki, koma akulalikira Buku Lopatulika.

KUKAMBIRANA (MPHINDI 20)

Unikirani mafunso otsatirawa:

1. Kodi mukuganiza kuti uthenga wabwino mumaumvetsetsa bwanji?

2. Kodi ndi mavuto anji amene akufotokozoredwa mu uthenga wabwino wa masiku ano?

3. Kodi tingaike fundo zanji polumikizana ndi omvera athu?

4. Kodi zitanthauzanji chiyani kukhala Mlaliki wolalikira Buku Lopatulika?

ZINTHU ZOTI MUCHITE MUTAPHUNZIRA (MPHINDI 5)

Limbikitsani membala aliyense mu gulu kuyamba kapena kupitiriza kukhala ndi dzongosolo lowerenga tsiku ndi tsiku pakugwiritsa ntchito "application' ya lamya wanu wa mmanja pa gawo lolembapo notsi. Kukhala mmalemba ndi kofunikira ngati tikufuna kukula monga otsatira a Yesu ndi kumvetsetsa uthenga wabwino mozama kuti tikathe kugawana ndi anzathu mosavuta.

Pakugwiritsa ntchito zida zikupezeka mu bukuli ndi Buku Lopatulika lanu, fotokokozani momveka bwino mwachidule (fundo 3-5) za uthenga wabwino pakuthandiziridwa ndi ndime za mu Buku Lopatulika zomwe mungathe kugawana ndi gulu lanu nthawi ya nkumanoo ukubwerawo. Ntchito iyi si mayeso, koma ndi kudzikhutula kwanu ngati njira yina yonena za choonadi cha uthenga wabwino ndi ena. Chiphunzitso cha uthenga wabwino chikupezeka pa tsamba kumbuyo kwa bukuli lingathandize kukwaniritsa ntchito iyi.

PEMPHERO

Ambuye Yesu, zikomo kuti munadza ndi kukhala moyo wangwiro pa dziko, ndi kuti munatenga malo athu pamtanda, ndipo kupyolera mu kuuka kwa akufa tikhoza kugawana mu moyo watsopano. Tithandizeni kukhulupirira mwa inu ndi kukula mu chikondi chanu. Tithandizeni kumvetsetsa Mau anu kwatunthu, kudziwa uthenga wabwino mozama ndi kutha kugawana choonadi ndi ena otizungulira. Zikomo chifukwa chakutipatsa ife mwayi, ndi kutipatsa ife zida kukhala wokhulupirika pa nthawi yoyenerera pamene mukugwiritsa ntchito nthawi mmalembo ndi kupezeka kwanu.

UDINDO WAKHALIDWE LANU (MPHINDI 15)

Lero tikhale wokhulupririka kwa wina ndi mnzake za chizolowezi chowerenga Buku Lopatulika. Mmagulu ang'onoang'ono, kapena awiriawiri, kambiranani za zizolowezi za kuwerenga Buku Lopatulika - zabwino kapena zoipa- ndi zinthu zina zimene mumakonda pakuwerenga mau komanso zina zimene mumavutika nazo powerenga. Ganizirani mosamala za nyengo yatsopano ya Buku Lopatulika, ikani cholinga, ndi kukokera pafupi, koma osakhala ndi kufuna kuluma chachikulu ndikulephera kumeza ndi kuziika pa mlingo wolephera – dzifunseni nokha za udindo wanu pa khalidwe lanu ndi kudziyesa mwezi winawo kuti mukuchita bwanji. Kumbukirni, osati kungowerenga Buku Lopatulika, koma kukhala ndi chimwemwe cha kudziwa Mulungu ndi uthenga wabwino tsiku ndi tsiku.

Pomaliza, lembani mu mafomu a udindo wa khalidwe lanu, gawanani mmagulu ang'onoang'ono ndi kupemphererana wina ndi mnzake.

OSAIWALA...

Msuntho uli ndi zida zowerengera Buku Lopatulika ndipo zikupezeka pa YouVersion. Bwanji kudzipatsa masiku asanu ndi awiri kudzikhutula pa ntchitoyi. "Guardians of the Gospel" chikhale cholinga cha sabata imeneyi ndi kuphatikizirapo dongosolo lanu la tsiku ndi tsiku.

POLEMBA

PHUNZIRO 4: NTCHITO YA MLALIKI

Kodi kulalikira ndi kulengeza zimasiyana bwanji? Phunziro ili ndi danga lowunikira mfundo zimene kuchokera mu Buku Lopatulika ndi pochita, kulimbikitsana wina ndi nzake pokonza ndi kunora maluso a malankhulidwe – kaya pa kulankhula awiri kapena kulalikira mogonjera kwathuthu ku mphamvu ya Mzimu Woyera pa ntchito ya mlaliki.

KUFOTOKOZERA PHUNZIRO

Ntchito ya kufalitsa ndi kulankhula ndi pakamwa uthenga wabwino monga mmene unabvumbulutsidwa kudzera m'mawu Opatulika a Mulungu ndi Mphamvu ya Mzimu Woyera.

CHIYAMBI CHA PHUNZIRO

Malingana ndi chikhalidwe, St. Francis wa ku Asis ananena kuti:

> 'Lalikirani uthenga wabwino nthawi zonse ngati ndi koyenera gwiritsani ntchito mawu.'

Mawu awa obwerekera ndi otchuka kwambiri pamene mukufotokoza kufunika kokhala wotsogozedwa ndi uthenga wabwino. Ngakhale pali mavuto awiri apa. Loyamba palibepo umboni wakuti St. Francis ananenapo zimenezi – sanalembe pena pali ponse.

Lachiwiri ndi lofunikira kwambiri, sizikugwira ngati chiganizo. Pomwe ndi zoona kuti moyo wathu uyenera kusonyeza nkhani yabwino ya Ufumu wa Mulungu momwemo mmene alili mawu athu, kulalikira kwa uthenga wabwino pa tanthauzo lake ndi ndondomeko yokhala pa mawu. Chiganizocho chikhoza kulembedwanso monga:

> 'Lalikani uthenga wabwino nthawi zonse, ndipo chifukwa ndi kofunika, gwiritsani ntchito mawu.'

Zoonadi mawu akuti "lalika" ndi "lengeza" amalumikizana bwino potengera mawu olakhulidwa- ndi zolengezedwa ndi pakamwa pakutha pa zonse "uthenga kukhala moyo wagwiro wa "uthenga wabwino" koma ngati simungayankhule za chiyembekezo cha mwa Yesu tsono nanga dziko lidzadziwa bwanji chifukwa chiyani moyo wanu Mmoyo umene mukukhalawo?

Lalikira kunali chinthu choyambirira chofalitsira uthenga wabwino mu Chipangano Chatsopano (Machitidwe Atumwi 2:14) ndiye palibe anthu ena tsiku la lero amene amakhulupirira kuti kulalikira ndi zinthu zachikale ndipo sinjira yabwino yoyenera za uthenga wabwino ku dziko. Ndithudi tikuyenera kukhala aluso mukulalikira kwathu ndi kuchita nawo mukulankhula kwathu (mwina kuwunikiranso njira zina za kulankhulana, monga kukonza kanema, kapena kulemba nyimbo) koma Buku Lopatulika limakakamiza alaliki kuti akangamile ulaliki umene ungathandizire omvera kuti amvetse uthenga ndi kukhala ndi mwayi ovomera maitanidwe a kwa Mkhristu ngati Mbuye ngati maziko akulu a ntchito yakugawana uthenga wabwino (1 Akorinto 1:21; 2 Timoteo 4:2; Marko 1:17; Luka 9:23).

Siwonse okhulupirira anayitanidwa kuti afalitse uthenga ngati alaliki mu njira iyi yapaderadera kwa okhulupilira ochuluka, kufalitsa ndi kuchitira umboni zikhoza kugwira bwino ntchito kudzera mu malankhulidwe a maso ndi maso munthu wina ndipo ichi ndi njira yoyambira imene uthenga wabwino umalankhulidwa kapena "kulengezedwa" kwa anthu ena.

Munjira ina iliyonse, tidzikumbukira kuti mawu paokha ngakhale ndi ofunikira kwambiri ku kufalitsa sangathe kufalitsa Mau onenedwa

kuchokera ku moyo osagonjera udzayimba belu lopanda phindu ndi chinyengo, ndiponso mawu amasiyanitsidwa ku Mzimu wa Mulungu adzakhala osowa mphamvu ya Mulungu yobweretsa chipulumutso kwa onse amene akhulupirira (Aroma 1:16).

MLOZO WA PHUNZIRO

KUKUMBUTSANA ZA MBUYO (MPHINDI 10–20)

Khalani ndi nthawi yodziwitsana za madanga zachitika kwa wina ndi, kukambirana nkhani, kulimbikitsana, kuwuzana za madanga amene anapezeka ndi china chili chonse chimene chingalimbikitse gulu. Pemphani munthu modzi kapena awiri agawane mongodzipereka kuti apereke mmene amagawila uthenga wabwino. (Phunziro lachitatu: kugwiritsa ntchito zochita moyo wanu mutaphunzira) ndi kupereka ndemanga osaiwala kutsindika kwabwino.

PEMPHERO

Perekani nthawi kwa Ambuye ndipo pempherani chinthu chili chonse chimene chinatchulidwa mwapadera pamene mmakambirana zimene munakumana nazo musanasonkhane mugawo la kukokera otsalira kukhala pamodzi ndi anzawo.

KUPHUNZITSA (MPHINDI 20–30)

Werengani bwino bukhu lotsatirayi munjira yoyenera kwa inu mwina powerenga liwu lililonse kapena powerenga pamene mukupereka phunziro lanu.

> 'Kuti ngati udzavomereza mkamwa mwako "Yesu ndiye Ambuye" ndi kukhulupirira mumtima mwako kuti Mulungu anamuukitsa kwa akufa, udzapulumuka ... pakuti, amene aliyense adzaitana pa dzina la Ambuye adzapulumuka. Ndipo iwo adzaitana bwanji pa Iye amene sanamukhulupirira? Ndipo adzakhulupirira bwanji Iye amene sanamva za Iye? ndipo adzamva bwanji wopanda wolalikira? Ndipo adzalalikira bwanji ngati satumidwa? Monganso kwalembedwa, "Okometsetsa ndithu ali mapazi a iwo akulalikira Uthenga Wabwino wa zinthu zabwino!"'
>
> **AROMA 10:9, 13–15**

Pali zokamba zambiri zolengezedwa za mu Buku Lopatulika pali mawu pafupipafupi 33 osiyana a chilankhulo cha Greek amene kawirikawiri amatanthauzira mawu akuti "kulalikira" kapena "kulengeza" mu ndime iyi kuchokera mu bukhu la Aroma, tikupeza kuti Paulo akugwiritsa ntchito mawu awa molozera kukagawana kwa uthenga wabwino. Kwa Paulo, kulalikira ndi chofunika koposa , ndipo akumuuza Timoteo kuti kulalikira kukhale chinthu choyambirira kuchita mu utumiki wake (2 Timoteo 4:1-2) tikuona pa tsiku la Pentecost chitsanzo cha mmene Mulungu anasankhira kugwiritsa anthu ku chikhulupiriro mwa Iye- zikwi za anthu anapulumutsidwa osati chifukwa chongokumana ndi zizindikiro za zozwizwitsa (malilime a moto, kulankhula malilime a zilankhulo zina) komanso kudzera mukumva zolengeza za Petro zodzadzidwa ndi Mzimu Woyera.

Mawu a Chigiriki kumene kunachokera mawu akuti "kufalitsa" kwenikweni akutanthauza kulengeza nkhani yabwino- mawu otengera a chochita polankhula mawu. Koma kulalikira mu khalidwe la makono kumaoneka ngati zachikalekale,ndipo zowoneka ngati njira yosakumana moyang'anizana popereka nkhani yabwino monga mmene kawirikawiri zimakondedwera monga ngati timatchulira njira ya kufalitsa ya wina ndi mnzake kapena yapaubwezi pomwe kufalitsa kwa iwe mwini ndi maubale ena ndi chindunji cha ulaliki. Ena amatailatu kufunikila kwa mphamvu ya mawu apakamwa ndi kufuna kuchitira umboni posesa zochita zawo zokha basi, ndi utumiki wokhazikika pantchito zokhuza moyo wa munthu zimaonetsera chikondi cha Mulungu chimaonekera mu ntchito zathu zachifundo. Komatu Paulo akupempha Aroma, kuti ngati okhulupilira sakulongosola momveka bwino gwelo la ntchito zathu zosonyeza Chikondi mdziko, kapena chiyembekezo chimene tili nacho, kodi pali wina amene angathe chowonadi cha Yesu ndi kumukhulupilira Iye monga Mbuye

Kambirnani: Ngati tikudziwa kuti kulengeza ndi ntchito yofunikira yakukhala mlaliki, kodi titsimikiza bwanji kuti uthenga

wa mu uthenga wabwino ukuperekedwa momveka bwino kwa omvera kuti aumvetsetse ndi kukhala ndi danga lakusonyeza mwatanthauzo zazimene amva ? Kodi kulalikira kukadalibe ndi malo mkati mwa zimenezi?

Mchitidwe wabwino wa kufalitsa kwa anthu monga zimakhalira kawirikawiri, kukupezeka kuti “mwina /kapena “ kuchokera ku zosankha zaperekedwa mmwambozo, koma pozindikira phindu la njira zosiyanasiyana kulankhulana kudzera pakamwa imene nthawi zonse ndi yofunika ngati tifotokozera Yes uku dziko-kuchokera kwa anthu osiyanasiyana amene amavumbulutsa chenicheni cha uthenga wathu pamphamvu yake yakusanduliza mmiyoyo yathu.

Njira ina iliyonse ya kulankhulana imene tingagwilitse ntchito mu chipiringu cha anthu (chitsanso kutalika) kapena (mukulankhulana wina ndi mnzake) nthawi zonse pali njira zambiri zimene tingapange pomwe tikufuna kuti timveke bwino mu uthenga umene tikupereka .Kudziwa gulu limene tikulankhula ndi chinthu china chofunikura kwambiri mumoyo wawo ndi kufunikira kwambiri pakuti ndi zothandiza kuti tiganize mosamala pamene tikufuna kufotokozera mopereka chitsanzo kapena mfundo zolumikizitsa zimene zingathandizire iwo kuti muyendele limodzi ndi kumvetsa chimene chikugawana nawo. Mwachitsanzo, ngati tikulalikira uthenga wabwino mugulu la achisodzera tingagwiritse ntchito mawu osiyanasiyana ndi mfundo zolumikizitsa za chikhalidwe pamene tili ndi zolankhulana pamaso ndi pamaso ndi munthu wamkulu wa kuti anapuma pa ntchito (pensioner). Uthenga umene uli mu uthenga wabwino pawokha susintha, koma mmene timalankulira za iwo, zitsanzo zofotokozera timagwiritsa ntchito ndi zolozera za chikhalidwe timagwiritsa ntchito zikhoza kutichitira ubwino anthu amene ali patsogolo pathu kumvetsera. Mwachidule,chimene timalalikira sichisintha , koma mmene timalalikira.

Ichi ndi chifukwa chake patokha tizikonzekeretse kugawa uthenga wabwino ngati chinthu chofunikira kwambiri mu ulendo wathu wa chikhristu. Ngati tingadalile chiyankhulo chomwecho chakale cha uthenga wabwino nthawi zonse zimene taima kulalikira tikhoza kukhala alaliki obowa ndi aulesi ngati nthawi zonse tingadalire njira yomweyo ya kufotokozera uthenga wabwino, ndi kotheka kuti sitingagwiritse ntchito mitundu yosiyanasiyana ya anthu mukulankhulana kwathu zimene zingathandizile iwo kupeza Yesu. Choyamba komanso chofunikira kwambiri titenge chikonzero chathu cha ulaliki mopemphera, kupempha Mulungu kuti atilankhule kudzera mu Mzimu wake ndi kupereka mawu amene tikanene.Tikhalenso okonzeka kulankhulana ndi anthu za uthenga wabwino mu njira zosiyanasiyana poyesera kutenga m’maganizo athu anthu omwe tingakumane nawo.

Kambirnani: Onetsetsani mfundo zisanu ndi ziwiri zotsatilazi za kulankhula pakamwa uthenga wabwino ndi kuganizila za mmene mungazigwiritsire ntchito panokha pa danga limene mungapezeke nalo la kufalitsa. kodi chikonzero ichi chingakhale bwanji ntchito ya kupembedza?

TIYENERA KULENGEZA:

- **Momveka bwino:** kumveka bwino ndi cholinga chachikulu cha kulankhulana kwabwino. Kufotokonza momveka bwino kukhale ndi kumvetsetsa kwa uthenga wabwino paokha, kudziwa iwo mwa kuya mokwanira kwakuti titha kuwupereka mosaphonya ndi mophweka.

- **Muuzimu:** kuti mitima yakufa itsitsimusidwe ndi uthenga wa mu uthenga wabwino mu Mzimu woyera udzagwire ntchito - choncho kulalikira kwathu kukhale kogonjera kuntchito ya mphamvu ya Mzimu.

- **Mwachikondi:** sitikupindurila anthu ku maganizo athu okha ndi mzeru zathu , koma kuchokhako chimodzi chenicheni cha yesu khritsu. Tilalikire modzichepetsa, kupereka ulemu kwa munthu amene tikugawana naye za (mulungu) ndi chifundo kwa iwo amene tikugawana nawo(ana ake).

- **Molimbika Mtima:** Kudzichepetsa sikuchotsera kulimbika mtima pamene tikupereka choonadi cha uthenga wa bwino.

tikhonza kuyankhula ndi chitsutso ndi kudzidalila kolimba mtima mu chowonadi mu uthenga wathu tikupitilizabe kukhala odekha ,ofatsa ndi ozichepetsa.

- **Mwapaderadera Pachokha:** Khritsu aperekedwe payekha ngati wapaderadera opanda wopikitsana naye kuposa onse omwe anabwera mmbuyo mwake, kukhalebe chindunji cha pakati pa kukambirana za uthenga wa bwino.

- **Umwini:** Tikhoza kuwonetsera choonadi cha uthenga wabwino pogawana mphamvu yake mmiyoyo yathu yomwe,kumanga maulalo ofikira kwa omvera ndi nyengo zawo.

Mfundo zonsezi ndi zofunikira kusunga mmaganizo athu kaya tikulankhula pa kuchezerana kapena kulalikira pa msanja chinthu chapaderadera cha pa danga lolankhulana ngakhalebe ndi kumvetserana. Nthawi zonse tidzikhala okonzekera kumvera bwino kwa iwo amene tikulankhulana nawo. Osangodikira kuti nthawi yanu ifike yakuti muyankhule,funsani mafuso abwino poyankha za zimene mukumva, mukhale ofunsafunsa osati oletsetsa, ndipo musaone ngati mukuyenera kupereka mayankho ku funso lirilonse limene mwafunsidwa kapena kukana mfundo iliyonse imene simukugwirizana nayo. Kulankhulana ndi maulendo, ndipo kawirikawiri zimene ndi zosazolowereka. Ngati maulendo ena onse osazolowereka timafuna kalozera (mapu) wotithandiza kuti tipeze njira ya kumene tikupita. Kumvetsera kwenikweni kwa zocheza zathu ndi mnzathu ogwira naye ntchito pamodzi kumapereka kalozera wotelo ndi nthawi ya malo amene tingathe kumveka bwino kwa iwo amene akulankhulana nafe (onani maphunziro a mchaka chachitatu a 'Evangelism and Listening Evangelism' kuti muone zambiri). Ngakhale kuti mfundo izizi ndi zothandizira kulengeza,ndi chinthu chofunikira kwambiri kukumbukira kuti palibe mulingo wa luso la kalankhulidwe kamene ungathe kubweretsa munthu wina ku umfumu wa Mulungu,koma Mulungu yekha angachite choncho.

Kulankhulana kwathu,munjira iliyonse tingatsate, ipereke mpata kwa Mzimu Woyera kuti uyende ndi mphamvu pamene kuli kufunikira kwambiri kuganizila mosamala za mmene timalankhulila za uthenga wabwino, potsiliza tikuyang'ana kwa Mulungu kugwira ntchito mwa ife ndi kudzera mwa ife mumawu apakamwa ndi kutulutsa chozizwa moyo wathu wa tsopano. Muphunziro latha, tinaona kudzikhuthula kwa Paulo kudziwa ndi kulalika mbiri ya Yesu mu 1 Akorinto 2. mundime zotsatilazo, Paulo akupitiriza kugawa kudzikhuthula kwathu ku kulalikira mbiri ya Yesu mwa mphamvu ya Mzimu ndi cholinga chakuti chikhulupiliro chake cha tsopano chitsamile pa Mulungu mmalo mwa malingalilo a umunthu.

> 'Ndipo mau anga ndi kulalikirta kwanga snakhala ndi mau okopa a nzeru koma muchionetso cha Mzimu ndi cha mphamvu kuti chikhulupiriro chanu chisakhale mnzeru ya anthu koma mu mphamvu ya Mulungu.'
>
> **1 AKORINTO 2:3-5**

Timalakalaka kupembedza Mulungu Muzimu ndi nchoonadi ndipo kufalitsa kwathu kuyenera kukhala kosiyana. Timalengeza choona chake mu mphamvu ya Mzimu ngati wopembedza omwe akupereka umboni kwa amene tikumupembedza cholinga chakuti enanso abwere amupembedze.

KUKAMBIRANA (MPHINDI 20)

Kambiranani mafunso kapena mau obwerekera otsatirawa.

1. Kodi kulalikira ndi kofunikira lero?

2. Za mphamvu zofooka zanu ndi ziti ngati munthu olumizana ndi ena?

3. Kodi mmakonzekera bwanji kuti mukapereka bwanji uthenga kapena zolankhulana za uthenga wabwino? Kodi mumapereka nkhani mosiyana?

4. Ndi gawo lanji limene kumvetsera kumatenga mukulalikira kwanu?

KUGWIRITSA NTCHITO ZIMENE MWAMPHUNZIRA (MPHINDI 5)

Pezani YouTube yabwino yoyenera ya zokamba za uthenga wabwino imene mukhoza kudzizukuta zokhudzana ndi mawonekedwe ake ndi mfundo zake. Pemphani gulu liwonere chidutswa cha kanema pa YouTube pakati pa phunziro, lembani notsi, ndipo mukonzekere

kudzakambirana pomwe mudzakumane mwezi wotsatira mwina pogwiritsa ntchito machenjezo asanu ndi limodzi operekedwa muphunziro ngati zothandizira pa kuyesera zina mwa za mphamvu ndi zofooka za kudzipereka kwathu ku uthenga wabwino.

PEMPHERO

Pempherani pamodzi kuti Mzimu wa Mulungu ugwire ntchito mwa inu podzichepetsa pamene mukupereka zolankhula zanu. Thokozani kuti Mulungu wakusankhani inu kuti mukhale pakamwa pake pa uthenga wake ndi kumupempha iye akuthandizeni kukhala moyo weniweni wa uthenga wabwino kotero kuti mawu ochokera mkamwa mwanu sakusiyanitsidwa ndi omwe akuchokera mkati mwa mtima wanu. Pempherani iwo amene adzamvera uthenga – kuti Mulungu akonzekeretse mitima yawo ndi kuwasintha iwo kufika pa malo avumbulutso amene angathe kusankha kumukhulupirira iye.

KUKHALA ADINDO A KHALIDWE LANU (MPHINDI 15)

Awiriawiri, gwiritsani ntchito nthawi ina pokambirana khalidwe la inu eni pa kulankhula za kufalitsa. Kodi mwatailira chikonzero chabwino cha mpata wa kulalikira ku chipiringu cha anthu kapena panokha? Kodi mwazemba kulankhula ndi pakamwa uthenga wabwino mokondera ntchito za chifundo mmaonedwe anu. Muchite mwachilungamo wina ndi nzake zokhudza pomwe muyenera kukonzanso pang'ono mudera limene mukulankhulira ndi pakamwa za nkhani yabwino ndi kudzikhuthula mopemphera kwa Ambuye kuti achite nanu.

Malizitsani maformu a Kukhala adindo a khalidwe lanu, gawanani awiriawiri kapena mmagulu ang'onoang'ono ndi kupemphererana.

OSAIWALA...

"The Advance Essential series" likupereka mwachidule, mlozo wochitika wa maganizo osiyanasiyana a kuyeserera kufalitsa. Bwanji osayang'ana If Jesus is the Answer – What is the Question? Kuti mupeze zina zambiri za zochenjeza zonora Madera oti tithe kulankhula bwino ndi ena za Yesu. Pezani zina zambiri za advance.org/ AESX.

POLEMBA

PHUNZIRO 5
MPHAMVU YA MLALIKI

Timalakalaka titaona mitima yakufa mu uzimu itatsitsimutsidwa phunziro ili ikuunika chimene chimatanthauza kuti kupatsidwa mphamvu kudzera mu pemphero kutitsogoza ife kuchitsitsimutso chenicheni mkati mwa mitima yathu kutero kuti ifenso obwezera tipereke kudziko.

KUFOTOKOZERA PHUNZIRO

Pemphero ndi tanthwe lakufalitsa ndipo limapereka mphamvu pomwe mphamvu zikuyenera kukhala – osati zoyesetsa za umunthu koma mmanja mwa Mulungu.

CHIYAMBI CHA PHUNZIRO

Mbusa wa presbytery ndi mtumiki Arthur Tappani Pierson anapanga chitsimikizo ichi chodabwitsa: “sipanakhalepo chitsitsimutso chauzimu mu dziko lina lirilonse kapena dera limene sichinayambe mugwirizano wa pemphero.”

Tikhoza kudzipanikiza pamalo polimba kuti tipeze chitsanzo chotsutsana ndi chiganizo ichi. Chikufotokoza kutuma kwa Mulungu kwa anthu ake mmalembo ndipo akulonjeza za zimene zidzatsatira kutenga chitsanzo chimodzi, muulamuliro wa Solomoni, Mulungu analankhula kwa ana a Israel oukira ndikuwapatsa chiyembekezo munthawi ya chisokonezo chosamvera chawo ndi zotsatira zoononga zosathawika zomwe zitsatire.

> ‘...ndipo anthu anga, otchedwa dzina langa, akadzichepetsa, nakapemphera, nakafuna nkhope yanga, nakatembenuka kuleka njira zawo zoipa; pamenepo ndidzamvera, m’Mwamba , ndi kukhululukira choipa chawo, ndi kuchiritsa dziko lawo.’
>
> **2 MBIRI 7:14**

Munjira yomweyo, uthenga wabwino wa Yesu ndi mwayi wobweretsa modzichepetsa mbuye wa Khristu mmoyo wathu mogonja, vomerezani kuti ndi Ambuye ndikumulola iye kutibweretsera machilitso ndi moyo watsopano. Timachoka pa mwano (tchimo lathu) kupita ku chivumbulutso (cha choonadi cha Mulungu) ku kulapa (Chikhulupiriro mwa Mulungu) ku chitsitsimutso (kusandulika kumene kumapereka kusandulikanso kwa ena).

Mau akuti “tembenukani” ogwiritsidwa tchito mu 2 Mbiri ndi mawu omwe atanthauzidwa mu Chipangano Chatsopano a”kulapa”. Yesu anayamba utumiki wake wa ulaliki ndi maitanidwe akuchita ndendende za (Marko 1:15). Vuto la a Israel mu nkhaniyi ndi vuto lomwe lilipo lero - kawirikawiri timayang’ana kwa milungu ina (kuphatikizapo ifeyo) pakuyesera kulamulira mathero athu omwe kusamvera kumeneko kudzangoctitengera imfa, kusweka mtima ndi chisokonezo. Mulungu wakhala akutiyitana kuti tibwerere kwa iye kuchokera pa nthawi imene tinapanduka. Uthenga Wabwino umaulula kuti ngakhale nkusamvera kwathu, chiyembekezo chikupezeka mu chisomo cha Mulungu ndi kudzichepetsa kwathu pamene tibwelera kwa iye.

Kudandaulira oweruza mlandu kawirikawiri kumakhudza chidandaulo chosonyeza kusalakwa muchiyembekezo chomasulidwa, koma pano tikuuzidwa kugwada pamaso pa woweruza wamuyaya ndi kuvomereza kulakwa kwathu pokhapo ndi pamene ndingathe kukhululukidwa. Chilungamo chimafuna chilango cha kulakwa kwathu mofanana ndi chenicheni chimene chikuonetsera mwano wathu kwa mfumu ya ngwiro koma mmalo

mwake Mulungu akuwonjezera chikhululukiro kwa ife kudzera chilungamo changwiro cha pa mtanda. Mmalo mwa imfa, tikupatsidwa machiritso, kubwezeretsedwa ndi moyo. Mulungu amatsitsimutsa odzichepetsa.

Chitsanzo china cha mphamvu ya pemphero ndi umodzi (ndi Mulungu ndi wina ndi nzake) ndi chitsitsimutso chimene chikupezeka mu nkhani ya Yobu kutembenuka kwa Yobu sikuli pamene iye akuyang'ana modzichepetsa koopsa kwa Mulungu, koma pamene iye momvera akupempherera anzake amene anali gawo la vuto lake lomusokoneza mu kudzichepetsa kwake koyambirira. Pa nthawi iyi munkhaniyi, Yobu anachotsa maso ake pa mavuto ake, mwachisomo akupempherera ena (amene anamulakwira iye) ndi anabwezeretsedwa.

Chitsitsimutso chimayamba ndi munthu mmodzi kusankha kumvera kwa Atate wawo wa mwamba ndi Kulengeza (malumbiro) unzika wanu mu ufumu wa mtendere. Zimangotengera munthu mmodzi kulengeza kuti Yesu ndi Mbuye mmawu ndi muzochita, kudalira Mzimu Woyera kuwapatsa mphamvu zokhala wobadwanso mwatsopano. Mwa chisomo cha Mulungu, chitsitsimutso chimayamba ndi ife- ndipo ndi chisomo chomwecho chitsitsimutso chitha kubuka kuchokera pena paliponse pamene anthu amene poyamba anali osamvera ogwirizana modzichepetsa poitanira dziko lawo.

MLOZO WA PHUNZIRO

KUKUMBUTSA ZA MBUYO (MPHINDI 15–25)

Khalani ndi nthawi yowuzana wina ndi nzake za zimene zachitika, kugawana nkhani, zilimbikitso, kupereka za mwayi umene unapezeka ndi china chili chonse chimene chingalimbikitse gulu. Gwiritsani ntchito nthawi iyi kukamba za kilipi (clip) ya mayeso a uthenga wabwino (phunziro lachinayi. Kuchita zimene taphunzira. Ndi chiyani chimene munapeza kuti ndi chothandiza kapena chosathandiza? Kodi chimene taphunzira ndi chiyani kuchokera kuchitsanzo chimene chidzatithandize ife kukula ngati anthu olalikira za nkhani ya bwino?

PEMPHERO

Patulani nthawi kwa Ambuye ndi kupempherera zinthu zanu, zabwino kapena zotsamwitsa zimene zanenedwa mu nthawi yokambirana za m'mbuyo.

KUPHUNZITSA (MPHINDI 20–30)

Werengani bukhu lotsatirali munjira yanu, kaya powerenga liwu ndi liwu kapena kuwerenga pamene mukuwerenga pamene mukupereka phunziro lanu.

> 'Ndikudandaulirani tsono poyambayamba, kuti achitike mapembedzo, mapemphero, mapembedzero, mayamiko, chifukwa cha anthu onse; chifukwa cha mafumu ndi onse akuchita ulamuliro; kuti mmoyo mwathu tikakhale odika mtima ndi achite mkulemekeza Mulungu ndi mekakulemekeza monse. Pakuti ichi nchokoma ndi chandirika pamaso pa Mulungu Mpulumutsi wathu; amene afuna anthu onse apulumutsike nafike pozindikira choonadi.
>
> **1 TIMOTEO 2:1–4**

Mukalata yoyamba ya kwa Timoteo, Paulo akupereka malangizo omveka bwino kwa mnyamata wake za moyo wopembedza wa ku mpingo wa mu Aefeso. Paulo akumuuza iye kupereka nthawi yake yambiri kumapemphero ndi kupembedzera a kwa anthu onse, chifukwa ndi chosangalatsa Mulungu chifukwa chimasangalatsa Mulungu. Chifukwa Mulungu akufuna anthu onse kudziwa mtendere wa ufumu wake. Pemphero ndi njira yokhayo imene tingaitanire Mulungu kuti achite zokhazo angathe kuchita – kubweretsa mtendere pa chisokonezo ndi kubweretsa moyo osatha kuchokera ku imfa.

Pemphero ndi thanthwe la kufalitsa chifukwa ndi kumene timafunafuna mphamvu ya Mulungu kuti tigwire ntchito, limapereka mphamvu pomwe mphamvu zikuyenera kukhala – osati zoyesetsa za umunthu wathu koma mmanja mwa Mulungu.

Mtsogoleri woyamba wa dziko la United States Benjamin Franklin ananena kuti, "Mukalephera kukonzekera, mukukonzekera kulephera" tikonzekeretse mitima yathu kukufalitsa kudzera

mu kupemphera mogonja ndi pemphero kwa Mulungu. Tikoza kunenanso mawuwa motere:

- 'Polephera kukonzekera ndi pemphero kufalitsa, tikukonzera kulephera kufalitsa.'

Ngakhale ndi pemphero lokhulupirika ndiponso ndi nthawi ya uthenga wabwino yopatsidwa mphamvu ndi Mzimu, anthu athabe kusankha kukana uthenga wabwino. Koma mphamvu ya chipulumutso ili mwa Mulungu yekha, ndipo tingathe kukhulupirira Mulungu kugwira ntchito kudzera mmapemphero athu ngakhale sinthawi zonse zimene timaona zotsatira zimene timayembekezera pa nthawi imeneyo. Zotsatira za kufalitsa zili mmanja mwa iye amene amamva uthenga wathu. Ndipo ndi Mulungu mwini wake choncho kupambana ndi kulephera kwathu mukufalitsa sikuyesedwa ndi angati apulumutsidwa koma ndi kumvera kwathu pakuchita chimene Mulungu watifunsa - kupemphera ndi kulalika.

Cholinga chathu choyambirira choti pempheretsa ndi chakuti Mulungu akutilamula kutero. Komabe, cholinga chathu chikhwime pochita lamulo lophweka la Mulungu pamene tikukula mu ubale wathu ndi Atate athu akumwamba, kutero kuti mwachikondi tikhumbe kumulemekeza iye ndi kufunafuna ubwino wake ndi madalitso amene tikuwapempherera. Timatulukira chifuniro cha Mulungu momveka bwino pomwe tikumudziwa iye kwambiri. Pamene tipemphera kwambiri ndi pamenenso timadziwa Mulungu pamene tikumudziwa Mulungu kwambiri kupemphera kotero kuti chifuniro chake chichitike pa dziko pano komanso kumwamba.

Kodi moyo wathu wa pemphero ndi otani? Kwa ena, pemphero limabwera lokha mwachibadwa. kwa ena zimatengera kuikapo mtima. Podzisanthula okha alaliki adzifunse okha funso ili. "kodi ndi chiti chimandiphwekera kuchita, kulaka kapena kupemphera? ndi kochuluka bwanji kamene mokondweretsa mmapitiliza kulalika kudutsa nthawi imene mwapatsidwa ya ulaliki, ndipo mmapitiliza kangati kulalikira kodutsa malire munthawi yanu imene munapatula yodzikhuthula / yachete? Kapena bwanji za nthawi yoyimba nyimbo za matamando. Ambiri mwa ife tilibe vuto kuzama munyimbo zabwino kwambiri ndi muzochitika za kuyimba kwa muchipiringu koma, timapezeka kuti sititero pamene yafika nthawi yapemphero.

Ngati tikufuna kukhala amphamvu mu kufalitsa tikuyenera kukhala anthu opemphera – kaya limabwera mwachibadwa kapena ayi. Kutalika kwa pemphero lathu kulibe ntchito koma kuwona mtima kwathu ndi kofunikira. Pomwe tikupitiliza moona mtima kupempha Ambuye kugwira ntchito yosanduliza miyoyo yathu yomwe ndi miyoyo ya ena, tidzazindikira kuti kuthekera kwathu kokhala nthawi yayitali pamaso pake idzakula. Panthawi iyi tidzamupatsa ulemu, idzakhala yabwino kwa ife, ndipo idzakhala mdalitso kwa ena.

Zokambirana: West Minister Shorter Catechism amafotokozera pemphero ngati, "kupereka kwa zokhumba zathu kwa Mulungu, zinthu zovomelezeka ku chifuniro chake, mudzina la Khristu, ndi kuvomereza machimo athu ndi chithokozo ndi chiyamiko cha zifundo zake."

Kodi kufotokozera ukuku kwaumba bwanji kumvetsetsa kwanu kwa pemphero makamaka muubale ndi kufalitsa?

Kuposera kudzipereka pakupemphera ena ngati gawo lakufalitsa, tingamvetse ndi kugwiritsa ntchito pemphero munjira zitatu pamene yafika nthawi yodzikonzekeretsa tokha kugawana uthenga wabwino:

- **Choyamba**, ngati gawo la ndondomeko imene tikhoza kukula ndi kukhwima ngati ana a Mulungu ndipo ngati ophunzira a Yesu Khristu amene amathandiza ena kukula chimodzimodzinso

AEFESO 4:14 -16

- **Chachiwiri**, monga njira imene mphamvu za Mulungu imabweretsera mwayi wochitira umboni ndi kugwira ntchito kudzera mwa ife ndi kusintha kufalitsa kwathu kuchoka pa kungofalitsa chabe chikhulupiriro cha Khristu kufika pogwedeza mitima kuchoka ku imfa kupita ku moyo

AKOLOSE 4:2-6

Chachitatu, ngati njira imene tingapatsidwe zida za uzimu kutiteteza kumisampha ya mdaniyo pamene tikulowa munkhondo ya uzimu ndi kutsegula maso athu kwa iwo amene apusitsika ndi misampha yake kuti mmalo mwake athe kuwona ndi kudziwa kuwala kwa Yesu

AEFESO 6:10-20

Monga mmene Paulo anachitira ndi Timoteo, tiyenera timemane ndi kulimbikitsa wina ndi nzake kuti tikhale opemphera anthu onse, ndi kuti chidzakhala chokondweretsa Mulungu pamene tikugonja mumphamvu zake mu chiyembekezo chakuti dziko lidzafika podziwa ndi kumagonjera mu choonadi chake chopulumutsa.

ZOKAMBIRANA (MPHINDI 10)

Unikirani mafunso ndio/kapena mawu obwerekera azokambirana zotsatirazi:

1. Kodi ndi zizolowezi ziti ndi malamulo ati a pemphero amene mmachita musanalalikire pamene pali mwayi wapaderadera wochitira umboni?

2. Kodi mmagwiritsa ntchito pemphero mkati mwa ntchito ya kufalitsa? Ngati ndi choncho, mmatani?

3. Kodi mmamvetsa ndikuchita bwanji pa nkhani ya pemphero “losayankhidwa” ndipo mungathandize winawake bwanji kumvetsa maganizo amenewa ngati mungafunsidwe pamene mukugawa chikhulupiriro chanu ndi iwo?

Kubwera kwa chitsitsimutso chimayenera chiyambike ndi chitsitsimutso chachikulu cha pemphero. Ndi muchipinda chitseko chili chotseka, kumene phokoso la mkokomo wa mvula umayamba kumveka. Kuchulutsa kwa pemphero la chinsinsi ndi atumiki chidzakhala chitsitsimikizo chachizindikiro cha madalitso.

ANDREW MURRAY

PEMPHERO (MPHINDI 20)

Awiriawiri kapena atatuatatu, khalani ndi nthawi yowunikanso za moyo wanu wa pemphero, kachitidwe ndi zizolowezi khalani owona mtima ndi wina ndi mnzake zokhudza mphamvu ndi zofooka zanu kupanga chisankho chopanga mpata wa nthawi yanuyanu ya pemphero tsiku lili lonse.

Pempherani mu njira zitatu zotsatirazi.

Khalani ndi nthawi yopemphererana wina ndi nzake. Pempherani kuti Mulungu atithandize kukhala anthu odzichepetsa amene tikukula tsiku ndi tsiku mu ubale wathu ndi Iye.

Khalani nthawi yopempherera dera lanu, boma lanu, kapena mzinda wanu. Pempherani otayika kuti apulumutsidwe ndi kupempha Mulungu akuchiritsa dziko lathu. (mwamphamvu : Mulungu mundipatse mwayi wogawana lero: Mulungu takasani mitima kumoyo lero)

Khalani ndi nthawi yodzipempherera inu nokha. Pempherani kuti mumvekedwe zida zodzadza za Mulungu pamene mukulowa mnkhondo.

KUCHITA ZINTHU ZIMENE MWAPHUNZIRA (MPHINDI 5)

Lembani ndandanda wa maina asanu a anzanu, abale, mamembala, ogwira nawo ntchito kapenanso kuti sanadziwebe Yesu ngati Ambuye. Sungani muphone mwanu, mu chikwama chanu chammanja Buku Lopatulika lanu kapena pamalo pena pake pamene mungamaone tsiku lililonse. Mokhulupirika pempherani anthu amenewa tsiku lililonse, kupempha Mulungu kuwatsitsimutsa ndi kuwabweretsa kuti akhulupirire Iye.

UDINDO WA KHALIDWE LANU GAWO LACHIWIRI (MPHINDI 20)

Malizani fomu ya udindo wa khaliwe lanu, gawanani awiriawiri kapena magulu a anthu ochepa ndi kupemphererana wina ndi nzake.

OSAIWALA...

Tidzakonda kumva kuchokera kwa inu mmene Mulungu akugwirira ntchito mumapemphero anu ndi kudzera mu kufalitsa. Mukhoza kutigaila ife ku advancegroup.org ndi kulimbikitsa ena muulendo wawo monga mukuchitira inu.

POLEMBA

PHUNZIRO 6:
KUDZIPERERA KWA MLALIKI

Kodi mumasungabe chitsimikizo cha miyoyo yathu ndi kufalitsa kwathu? Kumangirira pa zopeza zathu za pemphero mu phunziro kwa moyo wodzipereka wodzadza mu ulendo wathu wa chikhristu ndi kufalitsa.

KUFOTOKOZERA PHUNZIRO

Kudzipereka kumatisunthira ku malo a chiyero pomwe tikukhala ndi nthawi ndi Atate athu akumwamba oyera, pamene mobweza kumatikonzekeretsa ife kukhala kazembe wa ufumu omwe amanyamula uthenga wa chiyembekezo pa lilime chimene chimatsimikiza kusintha kwa mitima yathu.

CHIYAMBI CHA PHUNZIRO

Akuchokera ku ulendo wawo wa pachaka wa phwando la paska ku Yerusalem, Maria ndi Yosefe anazindikira kuti Yesu palibe pakati pawo. Patatha masiku atatu a nkhawa, mapeto ake analumikizana ndi mwana wawo, kumupeza ali mkatikati mwa kachisi. Yesu anakhala pansi pakati pa aphunzitsi a nzeru, komanso kupereka maganizo ake ndi kuwadabwitsa iwo ndi kumvetsa kuwoneka kwa malembo kwa mnyamata wa zaka khumi ndi ziwiri. Atafunsidwa ndi Maria chifukwa chimene wavutitsira kumufunafuna, Yesu anaoneka osokonokera ndi funsoli.

Chisokonezo cha kumene Yesu alili chikukhalapo chifukwa anangoganiza kuti mungathe kutaika kapena kusowa pamene iwo amene akuyesa kukupezani sakudziwa kuti muli kuti. Koma, akadadziwa bwanji kuti anali mnyumba ya Atate ake? Awa anali malo ake a chibadwa opezekemo iye. Kuli ngati kuti mukuyesetsa kufuna mtsogoleri wa dziko la US, malo ena kupatula ku White House, kenako ndikudabwa kuti mwamupeza atakhala pa gome lake mu Oval Office ndiye ndikumafunsa modera nkhawa, “Munali kuti”

Luka akulemba mwapaderadera chilankhulo cha Yesu pamene anayankha Maria chimene chikuwulula ubale wapadera ndi Mulungu. “Sindikudziwa kodi kuti kundiyenera Ine ndikhale mnyumba ya Atate wanga (Luka 2:49). Palibenso pena pali ponse mmalemba pomwe pakufunana ndi mawu amenewa, kupatula pamene Yesu akulankhula. Mawu oyamba amene analembedwa olankhulidwa ndi Yesu olengeza zakuti ndi Mwana wa Mulungu.

Ntchito ya pa mtanda ikusonyeza kuti tikhoza kutengedwa ngati ana a Mulungu mwa chikhulupiriro mwa Yesu, choncho funso kwa ife ndi lakuti; Kodi zimakhala za chibadwa kwa ife kukhala ndi nthawi mu nyumba ya Atate wathu?

Ndi pa malo awa akudzipereka amene timatulukira kwambiri mokwanira kuti kwenikweni ndife ndani. Timakula, timasulidwa za kulakwa kwathu. Timalangizidwa za cholinga chathu. Timakhutitsidwa mukupezeka kwathu ndi moyo. Kudzera mukudzipereka timapangidwa oyera monga iye ali oyera kudzipereka ndi mtsamiro wa moyo wa chikhristu chifukwa kumakonza chiyero, ndipo ndi ntchito yofunikira kwambiri mukafalitsa uthenga chifukwa uthenga wabwino uyenela kukhalidwa mmoyo mwathu ndi kulalikidwa ndi anthu oyera.

Mulungu akutifunsa ife pamene tikubwera pamaso pake osati mowawidwa koma ndi chimwemwe: Munali kuti?

MLOZO WA PHUNZIRO

KUKUMBUTSANA ZA MBUYO (MPHINDI 10–20)

Khalani ndi nthawi yowuzana wina ndi nzake kugawana nkhani, zolimbikitsa, kuwauza za mwayi wopezeka ndi china chili chonse chimene chingalimbikitse gulu, bwerezaninso ndandanda wa zinthu zimene zinapemphedwa kuti zipemphereredwe (phunziro lachisanu: kuchita zimene mwaphunzira) ndi zina zodziwitsa zimene zachitika pamene munayamba kuwapempherera mokhulupirika tsiku lililonse.

PEMPHERO

Khalani ndi nthawi ndi Ambuye pa zinthu zimene zikuchitikira, zabwino kapena zophunthwitsa, zimene zanenedwa mu nthawi yoyamba zokambirana.

KUPHUNZITSA (MPHINDI 25–35)

Werengani bukhu lophunzitsira lotsatirali munjira yanu, mwina powerenga liwu ndi liwu kapena powerenga pamene mukupereka phunziro lanu.

> 'Ndipo m'mawa mwache anauka usikusiku naturuka namuka ku chipululu napemphera kumeneko.'
>
> **MARKO 1:35**

"Timadzipereka" tokha ku zinthu zambiri mmoyo wathu. Tingathe kudzipereka tokha ku banja dni anzathu, kugwiritsa maphindu abwino, kufuna kukwaniritsa maloto athu. Kapena, tingathe kudzipereka ku zochita mwachizolowezi matimu a masewero, kapena kupambana kwambiri pa masewera ochita pa foni yathu ya mmanja ngakhale zili zongopengetsa nthawi chabe.

Yesu anadziperekanso ku banja lake ndi kwa anzakenso. Anadzipereka kwa Yosefe, kuphunzira ntchito ya pa umisili wapabanja. Anadzipereka kwa mayi ake, kutsimikizira kuti mtumiki Yohane adzatenge udindo omusala iye atafa kuuka ndi kukwera kumwamba.

Anadzipereka kukhala mu chiyanjano chabwino ndi anzake, kuoneka kuti amakhala nthawi yambiri ndi amnzake kuposera kulalikira muchipiringu cha anthu.

Ndi kudzipereka uku kowonetseredwa mmoyo wake nthawiyo, kodi Yesu akutanthauza chiyani pamene akuti anabwera kudzatsutsitsa mabanja potsutsana wina ndi nzake (Luka 12:53)? Tingapange kuti zimveke bwino mounikira ndi kudzipereka kwake koyambirira kwa Atate ake a kumwamba, kudzipereka kobwera pamwamba pa kudzipereka koposa zina zonse, osalabadira kuti ndi za khalidwe labwino bwanji. Yesu samanena kuti chinali chinthu cholakwa kukonda makolo anu, kepana kuti mwapaderadera amafuna kuphwanya mabanja chifukwa cha icho, koma Yesu anadziwa kuti chiri chonse chochotsa kudzipereka kwanu kwa Mulungu mapeto ake chidzatsogoza kumoyo wopanda chiyero. Ndi mukudzipereka kwathu kwa Mulungu kumene kumatipangitsa kukhala oyera.

Zokambirana: ndi zinthu ziti zimene zimakuchotsani pakuzipeReka kwanu mosavuta kwa Mulungu? Kambani makamaka pa zinthu zimene sizoipa pazokha koma ndi zakuti zimakhala zosokoneza kapena zotchinga kuti migonjere kwa Mulungu.

Kodi ndi zotheka kukhala odzipereka ku kufalitsa kuposera kwa Yesu mwini? Koma tili ndi moyo kukumpedza mfumu, osati utumiki kapena mayitanidwe. Tiyike maziko kukhala moyo wauzimu umene umamvetsera mwamphamvu kwa Mulungu ndi wodzipeleka kwa iye kuposa china chilichonse.

Yesu anaika patsogolo ubale wake ndi Atate wake pamwamba pazofunika za utumuki ndi maubale ake a pansi pano, kukhala ndi nthawi yam'bindikiro, kupemphera ndi kumvetsera kwa Yesu kukhala ndi Atate ake anali malo ake achibadwa okhalapo uthenga wabwino olembedwa ndi Marko ukutiuza za nthawi zitatu za m'bindikiro – khalani ndi nthawi lingalirani ndimezi

Marko 1:35–39: Kudzuka mmawa kupita Kumalo odekha kukapemphera. Kodi ichi chikutiphunzitsa chiyani za kulandira malangizo kuchokera kwa Mulungu?

Marko 6:45–46: Kubindikira pamwamba pa phiri kupemphera. Kodi ichi chikutiphunzitsa chiyani za kupatsidwanso mphamvu ndi Mulungu?

Marko 14:32–41: Kupemphera mu Getsemane asanamangidwe. Kodi ichi chikutiphunzitsa chiyani pa kubweretsa nyengo za zipsinjo zathu kwa Mulungu?

Pemphero losakhala losakakamizidwa mkati mwa tsiku lonse ndi labwino, koma kupatula nthawi mwadala kupemphera ndi kuwerenga Buku Lopatulika ndi kofunikira kwakukulu. Ena amachita bwino kwambiri pakupemphera koma osachita bwino kwenikweni pakuwelenga Buku Lopatulika, ena amakhala ndi nthawi yabwino yolingalira za Buku Lopatulika koma amazunguzika ikakhala nthawi yopemphera. Zingakhale zamphamvu kuphatikiza zonse ziwiri nthawi imodzi powerenga mutu umodzi kapena yambiri yamalembo ndipo kenaka kupempherera chimene ndimeyo ikunena ndi mmene ingagwiritsidwire ntchito m'miyoyo yathu. Ndi kofunikiranso kwambiri pomwe tikhala ndi nthawi yoyamika ndi kuthokoza Mulungu, ndi kubweretsa zosowa ndi zopempha zanu kwa iye.

Palibe chosowekera kwa Yesu kuti avomereze tchimo, koma kulapa kunali gawo lalikulu pa pemphero limene anaphunzitsa ophunzira ake: 'mutikhululukire mangawa athu....' (Mateyu 6; Luka 11) pemphero la David lovomereza ndi kulapa mu Masalmo 51 ndi chitsanzo chabwino cha ife mmene modzichepetsa tingafikire pamaso nkupemphera molapa.

Khwelero loyamba la chiyero ndi kuzindikira kuti Mulungu ndi woyera ndipo ife ndi ochimwa. Timasowa iye, ndipo pamene tikukhala ndi nthawi tsiku lirilonse kufika pamaso pake mphamvu yakusanduliza ya chikondi chake idzatsimikizira kuti sitili chimodzimodzi. Ndi kusandulika kumeneko kumakhala mboni yayikulu kuti uthenga wabwino ndi woona ndipo uli ndi mphamvu yakupulumutsa. Pamene tikulalikira za ubwino wa Mulungu ndi kugawana mbiri ya Yesu, iwo amene tingawafikire angathe kukula molimba mtima mwa chenicheni cha nkhani yathu ya uthenga wabwino poyesera ntchito ya Mulungu kudzera mmiyoyo yathu yodzipeleka.

Yesu anatipangira njira imene kwa ife yachiyero kudzera mu ntchito yake yopulumutsa yapamtanda, kutiitana ife kuti tife kumoyo wathu wakale ndi kuika chikhulupiriro chathu mwa iye. Pamene tikuyenda mmoyo umenewu watsopano, Yesu anatisonyeza ife mmene kutsatira chiyero kumakhalira mukudzipereka moyo wathu tsiku ndi tsiku kwa Atate. Siife angwiro, komanso sikuti tidzachita bwino nthawi zonse mmoyo, koma pamene tipinda mabondo pamaso pamfumu yathu yachifundo ndi yoyera tingathe kudzipanga tokha kupezeka ku chifundo chake cha kuchiritsa ndi mphamvu zake zotithandiza kukhala oyera monga iye ali oyera.

ZOKAMBIRANA (MPHINDI 20)

Unikirani mafunso otsatirawa:

1. Kodi m'mapanga mpata okwanira wa kukhala modzipereka mmoyo wanu tsiku ndi tsiku? Kodi zochita mwachizolowezi zathu zabwino ndi ziti, nanga zochita mwachizolowezi zofunika kukonza ndi ziti?

2. Kodi mumaona mozindikira ubale pakati pathanzi lamoyo wanu wodzikhuthula ndi maonekedwe a ntchito yanu yofalitsa?

3. Kodi mukhoza kukhala omasuka bwanji kumalangizo ena, kusinthikanso, kuzindikiritsidwa ndi kulapa kudzera mukudzipereka dala kwa masabata akubwera?

KUCHITA ZINTHU ZIMENE MWAPHUNZIRA (MPHINDI 5)

Yambani kupemphera kudzera mmasalimo, kukhala ndi mphindi zochepa tsiku lirilonse kuwerenga ndi kupemphera kuwonjezera pa nthawi yanu yowelenga Buku Lopatulika ndi kupemphera tsiku lirilonse. Ngati mungathe pitilizani kuchita izi kwa mwezi onse kapena chaka chonse. Mungathe kutero potsegula Buku Lopatulika lanu ndi kuwerenga salimo limodzi limodzi kapena kutsatira ndondomeko yakudzipereka monga ngati ya *Tim Keller's My Rock; A year of Daily Devotions in the Psalms*.

PEMPHERO

Thokozani Atate athu a kumwamba kuti amalakalaka ubale ndi ana ake. Dziperekeni mopemphera ku moyo wodzipereka umene umasuntha kuchokera pa alendo adzangoona a uzimu kukhala ana amene akukhala oyera monga iye ali oyera, ndi kuti kusinthika kwa miyoyo yathu kukhale maziko amene kufalitsa kumangike.

UDINDO WA KHALIDWE LANU (MPHINDI 15)

Kambiranani awiriawiri zinthu zimene zingaopseze moyo wanu – kapena zatero kale - kukhala fano lanu ndi kutenga kudzipereka kwanu kuchokera kwa Mulungu.

Modekha funsanani wina ndi mzake njira zothandizira kuyang'ana modutsa mmalo ena obisika amene tinawatayirira ofunika kukonza.

Maliza form ya udindo wa moyo wathu, gawanani awiri awiri kapena mmagulu a anthu ochepa ndi kupemphererana wina ndi mzake.

OSAIWALA...

The Advance Proclaimers Series ndi bukhu limene lingathe kugwiritsidwa ntchito pamaphunziro amtsogolo, komanso amagwira ntchito bwino pakuwerenga modzipereka panokha kukuthandizani inu mukuyenda kwanu kwa tsiku lirilonse. Pezani zambiri pa advancegroup.org/APS

POLEMBA

PHUNZIRO 7:
KUGONJERA KWA MLALIKI

Muphunziro lino tikulitsa pa maganizo a chiyero amene tinalingalira muphunziro lambuyomu, makamaka pamene tikulumikiza kudziwa uweniweni wa Mulungu, chiyembekezo cha uthenga wabwino ndi moyo wa chikhristu. Tidzaona udindo wamoyo wanu ngati chofunika kwambiri muulendo wanu wokhala ophunzira.

KUFOTOKOZERA PHUNZIRO

Mulungu amakhumba kuti anthu ake akhale oyera monga iyenso ali oyera. Ndi kudzera mkugonjera kwa Mzimu Woyera ndi udindo wa moyo wathu ku dera lathu tikukhala kumene tingathe kukula mchiyero.

CHIYAMBI CHA PHUNZIRO

Mawu akuti chiyero ndi kuyera akuoneka modutsa ka 900 muBuku Lopatulika monse kuchuluka koposa kwambiri mukaphatikiza mawu a chikondi, chikhulupiriro, kukhululukira ndi pemphera pamodzi!

Chiyero ndi mutu (theme) ndi mutu waukulu kwambiri mu Buku Lopatulika, ndipo Mulungu amakhumba kuti chikhale chachikulu chenicheni mmiyoyo yathu.

Mulungu ndi woyera chimene chikutanthauza kuti ndi wopatulika, ndi wangwiro, kalonga. ndi mmodzi yekha, ndipo palibenso wofanana naye. Ife siife angwiro: aliyense waife paekha anapelewera pa mulingo wangwiro wa Mulungu wathu woyera. Olemba bukhu la Ahebri akutiuza kuti okhawo woyera adzaona Ambuye (Ahebri 12:14) ndipo Yesu akutiuza kuti oyera mtima adzaona Mulungu (Mateyu 5:8). Kusowa kwathu kwa chiyero ndi vuto lalikulu la umunthu ngati tingakhale ndi chiyembekezo chilichonse cha ubale ndi Mulungu. Kodi osayera angakhale bwanji oyera, olandiridwa kwa Ambuye ndi otha kukhala mu ufumu wake?

Nkhani yabwino ndi yakuti yesu anapereka njira imene anthu osayera atha kulowa pamaso pa Mulungu wangwiro woyera ndi kukhala ndi iye mpaka muyaya (Aefeso 5:25 – 26). Iwo amene anaika chikhulupiriro chawo mwa Yesu amagawana naye chiyero, kulowa mu moyo watsopano, moyo woona ndi moyo woyera.

Chiyero ndi mutu waukulunso wa uthenga wa Yesu wokhudza mchere mu Mateyu 5:13. Munjira yomweyonso yakuti mchere ndi yopanda phindu ukasukuluka, uthenga wathu ulibe chiyembekezo ngati titaya chiyero chathu chenicheni. Ngakhale kuti ndi ntchito yosatha ya tsidya lino la muyaya, tinayitanidwa kukhala moyo osiyana kotero kuti dziko lingathe kuzindikira chenicheni cha uthenga umene tikulalika.

Uthenga wabwino ndi uthenga woyera, kuchitira umboni kwa Mulungu oyera amene anachita munjira ya chiyero kupangitsa anthu osayera kubwezeretsedwanso ku kudziwika kwenikweni - monga anthu a chiyero a mu ufumu oyera.

MLOZO WA PHUNZIRO

KUKUMBUTSA ZA MBUYO (MPHINDI 10–20)

Khalani ndi nthawi youzana wina ndi mzake, kugawana nkhani, zilimbikitso, kuuzana za mwayi wopeeka ndi china chili chonse chimene chingalimbikitse gulu. Pemphani gulu kuti ligawane zimene anakumana nazo pamene mopemphera anawerenga mmasalimo. (phunziro 6: kuchita zimene mwaphunzira)

PEMPHERO

Perekani nthawi yanu kwa Ambuye ndi kupempherera pa zinthu zimene zikukuchitikirani, zabwino kapena zophunthwitsa, zimene zanenedwa mu nthawi yoyamba ya zokambirana.

KUPHUNZITSA (MPHINDI 30–40)

Werengani bukhu lophunzitsira lotsatirali munjira yanu, mwina powerenga liwu ndi liwu kapena powelenga pamene mukupereka phunziro lanu. Pali malemba enieni atatu mu phunziro lino.

1. MULUNGU YEKHA NDI OYERA

> 'Ndipo ndidzadziwikitsa dzina langa loyera pakati pa anthu anga Israyeli, osalola dzina langa loyera aliipsenso; ndipo amitundu adzadziwa kuti Ine ndine Yehova Woyerayo wa Israyeli.'
>
> **EZEKIELI 39:7**

Buku Lopatulika limatiuza kuti Mulungu ndi ndani kotero kuti tingathe kudziwa ndi kumulambira mu mzimu ndi muchoonadi. Pamene tikuwelenga timatulukira kuti ndi Mulungu mmodzi woona.

Ndi osagawika, wofotokozedwa mukhalidwe lake la utatu, (Tate, Mwana ndi Mzimu woyera). Ndi wangwiro. Ndi wamuyaya. Ndi mfumu.

Koma chimene Buku Lopatulika limanena momveka bwino mwapaderadera cha Mulungu ndi kuti ndi woyera. Chiyero ndi khalidwe loyambirira la Mulungu. Zikutanthauza kuti pali wofana naye ndikuti ndi opatulika kwa ena onse. Palibe cholengedwa china chomwe chingafane ndi chidziwitso chake, khalidwe lake, kapena chenicheni chimene iye ali. Ndipo ndi chikhalidwe ichichi chimene Mulungu amakhumba kuti anthu ake akhale nacho – kuti tikakhale anthu oyera opatulika mukupembedza kwathu ndi kumvera kwa iye, anthu olungama ndi opanda chilema (Levitiko 11:45) kusoweka kwathu kwa chiyero – kukana kwathu kwa chiyero cha Mulungu – kunalenga vuto loopsa kwambiri kwa umunthu. Ufumu wa Mulungu ndi ufumu wangwiro koma tinasankha kupanda ungwiro ndi kuchotsedwa pamaso pake.

2. CHIYERO CHA YESU CHIMAPANGITSA KUTHEKERA KWA CHIYERO CHA ANTHU AKE

> '... koma Iye chifukwa kuti akhale Iye nthawi yosatha ali nawo unsembe wosasinthika, kuchokera komweko akhoza kupulummutsa konse konse iwo akuyandikira kwa Mulungu mwa Iye, popeza ali nawo moyo wache chikhalire wa kuwapembedzera iwo. Pakuti mkulu wa ansembe wotere anatiyenera ife, woyera mtima, wopanda choipa, wosadetsedwa, wosiyana ndi ochimwa, wakukhala wopirirra miyamba; amene alibe chifukwa cha kupereka nsembe tsiku ndi tsiku monga akulu a nsembe yoyambira chifukwa cha zoipa za iwo eni, yinayi chifukwa cha zoipa za anthu; pakuti ichi anacita kamodzi, kwatha, podzipereka yekha.'
>
> **AHEBRI 7:24-27**

Timapangidwa mchifanizo cha Mulungu ndipo tili ndi kuthekera kokhala anthu oyera, koma mwano wathu umapangitsa kukhala kutali. Ngati Mulungu angalole kachidutswa koipa kakang'ono kwambiri mu ufumu wake, ndiye udzasiya kukhala wangwiro. Choncho, kukana kwathu kwa chiyero kumatichotsa ku chiyero cha Mulungu ndi madalitso a ufumu wake.

Uthenga wabwino umatiuza kuti Yesu anatsika kudzalowa mmalo mwathu pa mtanda kutenga imfa imene tidadzisankhira tokha. Anatha kutenga malo athu chifukwa ndi woyera mwa ngwiro (opanda tchimo kapena chilema) imene inalipilidwa ndi Yesu. Ngongole yosalipidwa ya machimo a dziko inalipidwa pakumvera kwangwiro kwa Yesu. Analipira ngongole imene sikanatha kulipira kudzera mu chuma chake chosaguga cha chiyero chake. Tsopano, pamene Mulungu ayang'ana paiwo amene anaika chikhulupiriro chawo mwa Yesu Khristu, sawona kupelewera (osayera) kwa munthu koma ungwiro (chiyero) wa Yesu.

Ganizani za izi motere: Ganizani za nthawi imene munavala chovala chimene chinakupangitsani kumva kukoma makamaka kwa inu eni? Mwina munkavalira mwambo wapadera, ndipo potuluka mnyumba mwanu munamva kudzidalira. Pamene taika chikhulupiriro chathu mwa Yesu, Buku Lopatulika limatiuza kuti Mulungu amapereka chilungamo cha Yesu mwa ife ndipo

timavekedwa ungwiro wake (Aroma 5:18, Afilipi 3:9, 1 Akorinto 1:30)

Paulo akutiuza kuti mmalo mokwaniritsa zokhumba za thupi, tiyenera "tivale Ambuye Yesu Khristu". Kuvala kwenikweni ubwino wake (Aroma 13:14).

Fanizirani izi ndi Yakobo, amene akumema owelenga ake kuvula chonyansa chonse (kumasulira kwabwino ndi kuchotsa) Yakobo 1:21. Tiyenera tichotse zinthu zakale zimene zinali zotsutsana ndi Mulungu ndi kuzipereka kwa Khristu ndipo mmalo mwake adzasinthanitsa ndi kuyikapo chilungamo cha iye mwini.

Kodi mudayamba mwabwezedwapo kumwambo wina wake chifukwa simunakwaniritse muyeso wakavalidwe kake? Muyeso wofunsidwa wolowera mufumu wangwiro wa Mulungu ndi chiyero cha ngwiro, chimene ife tilibe. Koma ngati anthu opelewera tingathe kulowa muufumu wake wangwiro chifukwa tsopano tikukwaniritsa "malamulo akavalidwe" kudzera mwa Khristu. Palibe chimene chili chochepera ungwiro chingathe, koma palibe chochepera kuposa ungwiro wa Khristu opelekedwa kwa ife kuti tivale. Patsiku limene tidzalowa mukuzindikira kwenikweni kwa ufumu, sitidzabweretsa kuperewera kwathu koma chobvala cha chilungamo.

3. KUGONJERA KWA MIMU NDI KUDZILETSA KUMABALA KUKHALA OYERA

> 'Kuti muvule, kunena za makhalidwe anu oyamba, munthu wakale, wovunda potsata zilakolako za chinyengo; koma kuti mukonzeke, mukhale atsopano mu mzimu wa mtima wanu, nimuvale munthu watsopano, amene analengedwa monga mwa Mulungu m'chilungamo, ndi mchiyero cha choonadi.'
>
> **EPHESIANS 4:22-24**

Mulungu amakhumba kuti tikule, kukhwima osati tizingobwereza zolakwitsa zathu pamene tikukhala mwa iye lero (tchimo lachizolowezi). Tinakutidwa ndi chisomo chake koma umboni wa chikhulupiriro chosanyenga ndi chenicheni ndi kusandulika ndi kukula (kukhala ophunzira). Tisakhutitsidwe ndi kuvala chiyero cha Khristu ngati kaidi womasilidwira mundende, koma tisankhe kulemekeza mtengo wachilungamo wovala pokhala mukumvera iye amene anatilipirira ife. Uwu ndi ulendo wathu wophunzira: kusuntha kuchoka pa nthawi yakubadwa kwathu kwatsopano (kulungamitsidwa) kupitiriza kukula mmoyo watsopano (kuyeretsedwa).

Izi sizingokutipatsa chitsimikizo cha ungwiro watsogolo wamuyaya umene ukutidikira ife, koma imatipatsa njira ya mmene tingakhalire mosiyana lero.

Kusanthulika kumene kumacitika mmoyo mwa ophunzira kumasonyeza mwamphamvu ndi kuunikira kwa Paulo kwa chipatso cha mzimu chimene chimayendera kuchokera mmoyo wa wotsatira weniweni wa Yesu (Agalatiya 5:22-23). Mbali yomaliza ya chipatso yatchulidwa pano ndi chiletso kapena kudzikaniza. Mulungu mwa mzimu wake amatipatsa mphamvu yokhala moyo wodziletsa - koma tili ndi bwenzi mwa iye (Afilipi 2:12-13).

Ndi izi mmalingaliro athu, tili ndi zinthu zinayi zochititsa zimene tingachite kuti tikule mu chiyero ndi kumvera kwa Mulungu:

KUDZIKHUTULA

Pamene tikukhala nthawi yaitali mmawu a Mulungu, kwambirinso tidzadziwa kukhala chimene Mulungu akufuna kuti tikhale. Chomwenso pokhala nthawi mupemphero tingathe kupempha Mulungu atithandize kuthana ndi zofooka zathu ndi mayesero athu, kukhala ndi nthawi ndi Yesu ndi kuphunzira chimene chimatanthauza kukhala woyera pomwe tikupatsidwa mphamvu yokhala motero.

KUDZIDZIWA

Pamene tikuwerenga malemba chomwechonso malemba amatiwerenga ife, kutithandiza kuyesa miyoyo yathu yomwe ndi kuwonjezera kuzidziwitsa tokha. Kuzidziwa kumathandiza ife kuzindikira zofooka zathu ndi njira zimene za mmene tingayambire kudzikaniza tokha ku zinthu zimene zingapangitse chiwonongeko.

MUDZI /DERA

Kukhala tcheru ndi moyo umene tikukhala sikukwaniritsidwa kudzera mukuzidziwa kokha. Kudzipereka mu chiyanjano chachikristu

ndi mmudzi mwathu, tidzidzamasula tokha ku mayeso okonda kuchokera kwa amene atizungulira. Kubyala kapena kuyambitsa chinthu mmudzi kumabereka danga kwa anthu ena kulankhula kumoyo wanu, ndi kukhala omasuka ndi ena kungathe kubweretsa zotchinga zina, koma chiopsezo cha kusautsidwa chisapatutse ife kuchoka pazenizeni zamu Buku Lopatulika ndi ulendo woyenda mwachisomo pamodzi pamene tikukula patokha ndiponso ngati banja la Mulungu.

KUVOMEREZA

Yakobo amatiuza kuti tivomereze machimo athu kwa wina ndi mzake osati chifukwa cha chikhulupiriro komanso khalidwe lanu (Yakobo 5:16) mkoyenera kupeza gulu la abwenzi amene tingathe kotheratu kukhala owona ndi tingawaululire zolimbana nazo, mayesero ndi zolephera. Mdaniyo akufuna kukusungani kutali ndi zokoma, mdima kumene angazitembenuze kuti muchite manyazi, koma Mulungu akutiitana kuti tiyendere ulendowu limodzi, kukuthandizani kugwirana wina ndi nzake kufotokoza mukuwala kumene angakukonzereninso. Kulephera kusakhale mathero ndi Mulungu. Kufotokozera za moyo wathu ndi njira imene tingathe kuthana ndi zolimbana nazo modzichepetsa ndi mogonja mu chisomo chake

Monga alaliki, uthenga umene timalalikira siwongowona kuti anthu akuchitapo kanthu komanso kupanga ophunzira amene akukula ndi kukhwima – anthu oyera (Akolose 1:28-29). Ndi ophunzira enieni amene angatengere uthenga umenewu mwamphamvu mudziko. Ndi ntchito yoyera ya kwa anthu oyera.

ZOKAMBIRANA (MPHINDI 15)

Unikirani mafunso ndi / kapena zokambirana za mawu obwereka otsarirawa

1. Kodi mungamufotokozere bwanji munthu amene sakudziwa za chiyero cha Mulungu?

2. Kodi “tingadziveke tokha” bwanji mwa Khristu?

3. Kodi ndi chiyani chimene chimakuthandizani kukhala, kapena kukulepheretsani kukhala a udindoa chikhalidwe chanu kwa ena?

‘Ngati mwaona kuti mungathe kuyenda muchiyero opanda kusunga chiyanjano chosatha ndi Khristu, munapanga cholakwitsa chachikulu. Ngati mungakhale oyera, muyende moyandikana kwambiri ndi Yesu’

CHARLES SPURGEON

KUCHITA ZOMWE MWAPHUNZIRA (MPHINDI 5)

Ngati mulibe gulu la abwenzi owakhulupirira (apadera osayina ndi okhala a udindo mmene timachitira ndi gulu la Msuntho) amene mmakumana nawo pafupipafupi ndipo ndi womwe mungakhale nawo moonadi, momasuka komanso kufotokoza bwino za khalidwe lanu, ganizani amene mungachite naye izi ndipo chitanipo china chake mwadongosolo msanga. Ngati mukuchita kale izi, gawanani ndi wina wake amene sakuchita za chifukwa chili chakufunikira kwa inu ndi kuwathandiza kuti ayambe ndi malangizo, chilimbikitso kapena machenjezo ena amene mungapereke.

PEMPHERO

Zindikirani ndi kutamanda chiyero cha Mulungu mu pemphero. Pemphani chikhululukiro chake ku machimo athu, ndi kupereka mathokozo chifukwa chakuti ntchito ya Yesu ikutipulumutsa timatha kugawana chilungamo chake. Pemphani Mulungu kuti apitilize kugwira ntchito mmoyo mwanu kukupangani inu kukhala oyera. Dzipelekeni kukhala moyo odziletsa mogonjera kumphamvu ya mzimu pomwe mukufunitsitsa kukula ngati ophunzira ndi kukhala kwambiri okwanira pa cholinga chokhala anthu oyera ndi uthenga woyera.

UDINDO WA KHALIDWE ANU (MPHINDI 25 MINS)

Awiriawiri, gwiritsani ntchito nthawi iyi ngati mwayi wanu wovomereza wina ndi mzake za mmene mumapezekera kuti mukuperewera mobwerezabwereza pobweretsa izi kwa ena kuti tidziwe, khazikitsani ichi kuti mudzifunsana wina ndi mzake nthawi ndi nthawi za mmene

mukuchitira mbali imeneyi ndi kupitiliza kupemphererana wina ndi mzake.

Malizani form yakufotokoza udindo wa khalidwe lanu, gawanani awiriawiri kapena mmagulu ang'onoang'ono ndi kupemphererana wina ndi mzake.

OSAIWALA...

Imodzi mwa njira zolimbikitsira milaga ya Msuntho ndi kukhala olumikizidwa ku zonse zimene Mulungu akuchita kudzera mwa abambo ndi amayi amagulu a Msuntho mozungulira dziko lonse. Tsimikizani kulembetsa kuti mudzilandira mwezi ndi mwezi e-mail kuphatikizanso nkhani ndi maumboni kuchokera gulu (mpingo) wa dziko lonse la Msuntho zimene zidzakulimbikitseni inu mu chikhulupiriro chanu ndi kufalitsa

POLEMBA

PHUNZIRO 8:
KHALIDWE LA MLALIKI

Akhristu ambiri oyera kwambiri ndi amene ali odzichepetsa kwambiri, kodi choncho kukhala odzichepetsa mu kufalitsa kwathu kumaoneka bwanji?

KUFOTOKOZERA PHUNZIRO

Kudzichepetsa ndi khalidwe labwino kwambiri la Kazembe aliyense waufumu wa Mulungu. Chithunzithunzi chinapeRekedwa kale mwangwiro mwa Yesu kuyeretsedwanso ndi kupatsidwa mphamvu ndi mzimu woyera kuulemerero wa Atate wathu wa Kumwamba.

CHIYAMBI CHA PHUNZIRO

Panthawi yomwe mngelo Gabriel anauza Maria kuti akuyembekezera mwana, kudzichepetsa, mutu waukulu mbiri ya Yesu- kunafumphuka. Maria analambira Mulungu ndi kupereka chiyamiko kwa iye kuti wamuganizira iye, mdzakazi wake, mukudzichepetsa kwake. Mmawu ena, 'ndine mtsikana wamba chifukwa chiyani Mulungu akufuna kundigwiritsa ntchito ine?'

Kodi munayamba mwadabwapo kuti Mulungu angakugwiritseni ntchito bwanji?

Nthawi zina tikhoza kukhala ndi chitsimizo chatokha mu mphatso ndi luso, kukhulupirira kuti Mulungu amasankha kugwiritsa ntchito ife chifukwa cha zinthu. Kuyitana kwa Mulungu kumaona khalidwe lathu osati luso lathu, ndipo khalidwe limene limamusangalatsa kwambiri pa mtima pake ndi lodzichepetsa. Maria akupitiliza chiyamiko chake poyimba za mmene chiyero cha Mulungu chimamwazira odzikuza ndi kukweza odzichepetsa. Ngati mtsikana wa chiyuda, chidziwitso chake cha Chipangano Chatsopano chikanamupatsa iye chili chonse chimene anakachifuna kupanga zolengeza izi za kudzidalira kwake kwa Mulungu. Ndipo tsopano akuona chenicheni mwa iye yekha. Mulungu nthawi zonse amasankha kugwiritsa ntchito odzichepetsa pa zolinga zake munjira yosayembekezera, kugonjetsa nzeru za dziko ndi kuvumbulutsa mphamvu zake ndi chisomo kudzera mwa anthu amene sitimawayembekezera. Khwelero loyamba lokhala wogwiritsidwa ntchito ndi Mulungu kuchita zinthu zodabwitsa mwa ife ndi kuzindikira kudalira kwathu kwakukulu mwa Iye.

Kubadwa kwa Yesu kunachitika kwambiri modzichepetsa. Mfumu ya Mafumu anagonetsedwa modyera ng'ombe - chida chodyetsera nyama! Kulemera kwa kubadwa kwa mfumu kunasinthanitsidwa ndi umphawi wamabadwidwe wa munthu wamba. Kuyanjanitsidwa kwathu ndi mlengi wa zinthu zonse kunakhazikitsidwa modzichepetsa.

Chilichonse chimene tikuyang'ana mmalembo – kaya ndi Yesaya 53 kumene timamva za chisauko cha mtumiki wa Ambuye amene adzatonzedwere machismo athu, kapena kulengeza kwa Yesu za kubwera kudzatumikira mmalo modzatumikiridwa, kapena kusambitsa mapazi a ophunzira ake, kapena kugonjera ku chifuniro cha Atate ake mmunda mwa Gethsemane, kapena kudzilolera yekha kumenyedwa, kutonzedwa ndi kupachikidwa pa mtanda pamene ndi mawu amodzi, akadatha kuwononga aliyense amene anamupanga iye kumva kupweteka – Buku Lopatulika limatipatsa chithunzithunzi cha mfumu wotumikira amene adzagonjetsa temberero la kunyada kwa umunthu ndi mphamvu yodzichepetsa ya chiyero.

Mulungu amalanditsa anthu ake munjira imene amafunira kuti iwowo akhale. Kunyada kumatsogoza mu chiwonongeko, kudzichepetsa kumatibweretsera ife.

- 'Pakuti mudziwa chisomo cha Ambuye wathu Yesu Khristu, kuti chifukwa cha inu

anakhala wosauka, angakale anali wolemera kuti inu ndi kusauka kwachei mukakhale olemera For you know the grace of our Lord Jesus Christ, that though he was rich, yet for your sake he became poor, so that you through his poverty might become rich.'

2 AKORINTO 8:9

MLOZO WA PHUNZIRO

KULANDIRANA / KUKUMBUTSA ZA MBUYO (MPHINDI 10–20)

Khalani ndi nthawi yowuzana wina ndi mzake, kugawana nkhani, zilimbikitso, kuwuzana za mwayi umene unapezeka ndi china chili chonse chimene chingathe kulimbikitsa gulu. Kwa magulu ochepa, funsani aliyense kugawana chopambana chimodzi ndi chotchinga chimodzi kuchokera pa mkumano wapitawo. Kwa magulu akulu, sankhani anthu anayi kapena asanu kupereka umboni wapaderadera kuchokera pa mkumano wapitawo.

PEMPHERO

Perekani nthawi iyi kwa Ambuye ndi kupempherera chili chonse chabwino kapena chotchinga, zimene zatchulidwa munthawi ya kulandirana ndi kukumbutsana za zimene zinachitika kuchokera pamene tinasiyana.

KUPHUNZITSA (MPHINDI 25–35)

Werengani bukhu lophunzitsira ili mu njira yanu, mwina powerenga liwu ndi liwu kapena kuwerenga pamene mukupereka phunziro lanu.

'Musachite kanthu monga mwa chotetana, kapena monga mwa ulemerero wopanda pache, komatu ndi kudzichepetsa mtima, yense ayese anzache omposa iye mwini; munthu yense asapenyerere zache za iye yekha koma yense apenyererenso za mnzake. Mukhale nawo mtima mkati mwanu umene unalinso mwa Khristu Yesu, Ameneyo pokhala nao maonekedwe a Mulungu, sanachiyesa cholanda kukhala wofana ndi Mulungu, koma anadzikhutula yekha, natenga maonekdwe a kapolo, nakhala mmafanizdwe a anthu; Ndipo popezedwa mmonekedwe ngati munthu, anadzichepetsa yekha, nakhala womvera kufikira imfa ndiyo imfa ya pamtanda.'

AFILIPI 2:3–8

Kulembanso zimene analemba C.S Lewis, "kukhala odzichepetsa sikutanthauza kudziganizira nokha moperewera, kukutanthauza kuganizira mochepa za inu nokha."

Buku Lopatulika silifunsa ife kukhala odzinyoza kapena odziderera. Ndinu osamalidwa ndi okondedwa ndi Mulungu – ndipo ndinu otchedwa ana ake apaderadera. Koma pali malire owoneka: kuganizira za ife tokha kwambiri kunatiyika pa chiwopsezo cha mtundu wodzikonda umene unapangitsa umunthu kukhala mmoyo wa uchimo koyambirira kuganizira modziderera kwambiri za ife ndi kukana chidziwitso chimene Mulungu anachibweretsa kwa ife, ndipo kuganizira kwambiri ndi kulephera kuzindikira ukaronga ndi ufumu wa Mulungu.

Kunyada kumakhala pa mtima pa tchimo. Miyambo limatiuza kuti "Pokudza kudzikuza padzanso manyazi koma nzeru iri ndi odzichepetsa, "Miyambo 11:2) Nzeru za Buku Lopatulika litilitcha zimatsimikiza mobwerezabwereza khalidwe la kudzichepetsa ngati chotsutsana nacho chikhalidwe chonyada ndi kukondwera madalitso amene amatsika kuchokera ku icho.

Tikukhala nyengo ya kudzikweza tokha. Tangoganizirani David akanapha Goliati lero? Mayesero a mmaganizo odzadza ndi magazi atsopano, chipambano chodzikweza patokha chikadakhala champhamvu kwambiri! Ambiri mwa ife tikadalandila mosatekeseka nyimbo zolembedwera chipambano chathu, makanema kupangidwa ndipo mayina a ulemu kupatsidwa kwa ife, palibe ngakhale kamodzi mumasalimo a David pamene akutchula za chigonjetso chake, mfundo imene mlaliki wamkulu D.L. Moody anatikodolera ku ulaliki wake wa kudzichepetsa. Lero, kungonunkhiza za kukula timalimbikitsidwa kukhala a katswiri apatokha, kumangapo ulemu ndi makwelero athu. Koma Mulungu sanakutumeni kumanga utumiki kapena kudzikweza nokha pa udindo. Koma Mulungu amakhala ndi chidwi kwambiri pa

khalidwe lanu, ndi mmene mungakwezedwere ku cholinga chake modzichepetsa (Luka 14:11)

Yesu anayenda mseu wodzichepetsa, udindo wa wantchito. Ndi mfumu amene anabwera osati kudzatumikiridwa koma kudzatumikira (Mariko 10:45). Taonani zimene Yohane ananena za Yesu pa nthawi ya kamphindi kochepa asanasambitse mapazi a ophunzira ake.

> **'Yesu podziwa kuti Atate adampatsa Iye zonse m'manja mwake,** ndi kuti anachokera kwa Mulungu, namuka kwa Mulungu, ananyamuka pa mgonero, nabvula Malaya ace; ndipo m'mene adatenga copukutira, adadzimanga m'cuuno'
>
> **YOHANE 13:3–4**

Kudziwa kuti zinthu zonse zili pansi pa mphamvu zake, ndi kudziwa kudzadza kwa chidziwitso chake, Yesu anasankha kukhala wantchito kusonyeza chifuniro cha Atate ake. Mwina munapangapo zokambirana za Buku Lopatulika pamene panakhudza kusambitsana mmapazi wina ndi mzake kwenikweni. Komabe kusambitsana mmapazi kwa lero sikuchita chilungamo cha kufunikira kwakulu kumene Yesu anaonetsa ophunzira ake. Ndi chovuta kwa ife kumvetsetsa za mmene anasowera mtendere kuona kuti mphunzitsi wawo – Mesiya wawo - akutenga ntchito iyi ngati chizindikiro cha kudzipepetsa ndi mtima wa ntchito.

GANIZIRANI ZA IZI MOTERE:
Mwamva kugogoda pa khomo panu kupita kuona kuti ndi mfumu amene akulamula dziko lanu. Akukupitilirani kulowa mnyumba mwanu, ndipo akunyamula mwana wanu ndi kuyamba kuchotsa thewera limene wawonongera. Fungo lake ndi lalikulu ndipo mukungoyang'ana mwakakasi pamene zoipa za thewera la mwana wanu zikugwera mmanja mwa ufumu. Ndipo mfumuyo akuoneka osatekeseka mkomwe pa zimene zikuchitika, kukhala okondwa kwambiri ndi nthawi imene akucheza ndi mwana, muzochitika izi zosakondweretsa koma zoyenera.

Osayiwala kuti pamene Yesu amasambitsa mapazi a ophunzira ake, anadziwa kuti Yudasi adzamupereka iye. Anadziwa kuti Petro adzamukana Iye. Anadziwa kuti omutsatira ake anali anthu onyada ndi ofooka, komabe mu mphamvu ndi ulemelero wake anadzichepetsa pamaso pawo, kupereka chitsanzo cha kwa iwo kuti atsatire. Osati anangoyenera kungosambitsa kokha mapazi a wina ndi mzake, komanso amayenera kukhala antchito odzichepetsa mu zinthu zonse.

Pali nthano yotchuka yokhudza Charles Spurgeon, amene atawona mmodzi mwa ophunzira kulalikira kupita pa gome motumbwa kwambiri komanso potsika pa gomepo ali wamanyazi atagwetsa nkhope chifukwa cha mmene ulaliki wawo walepherera, analankhula mokonza kuti " Ngati mukadapita mmene mwabwereramu, mukadatsika ngati mmene munakwelera muja."

Palibe kuti ulemero wa kuitanidwa kwanu ndi kotani, kudzionetsera kwa mphatso zathu, msinkhu wa mwayi wathu, kapena mbiri ya utumiki wathu, tilibe mphamvu yopulumutsa munthu aliyense. Mphotho yake ya uchimo ndi imfa (Aroma 6:23), koma mphontho yachifatso ndi moyo (Miyambo 22:4) kudzera mu wantchito wotonzedwa amene anatenga malo athu pa mtanda, tsopano tingathe kuika chikhulupiriro mwa Iye ndi kunyamula mtanda wathu pokufa modzichepetsa kukukhala kwathu kwakale konyada. Tikhoza kuchoka kuimfa kukhala ndi moyo. kudzichepetsa sikhalidwe lokha labwino, ndi kuchita kwathu koyenera kumene tingapaangire kwa Yesu pamene tazindikira kuti iyeyo ndi Ambuye.

> 'Popeza Yehova akondwera nao anthu ake; Adzakometsa ofatsa ndi chipulumutso.'
>
> **MASALMO 149:4**

Kudzichepetsa mukufalitsa sikutanthauza kuchepsa anthu, kuchepetsa uthenga kapena kuchokapo pakugawana choonadi chenicheni cha chimene chingakwiyitse anthu (ndipo uthenga wabwino kawirikawiri umakhala wokwiyitsa ku mitima yowumitsidwa. Mofanana choncho, kulimbamtima mukufalitsa sikutanthauza kuti tichinyize uthenga wabwino kummero kwa anthu mosaganizira za mmene ungathandizire iwo kumvetsa za chiyembekezo chimene wanyamula. Kuzichepetsa mu kufalitsa kumatanthauza mwa zina zinthu zinayi zotsatirazi.

Kambirananani: Khalani ndi nthawi yokamba zinthu zinayi mugawo la kudzichepetsa

mu kufalitsa. Kodi mungagwiritse bwanji ntchito mfundo izi?

MODZICHEPETSA TUMIKIRANI AMBUYE
Udindo wathu umodzi woyambirira ndi kulakalaka kutumikira Mulungu, ngakhale chingakhale chophunthwitsa, chosowetsa mtendere kapena chodula mtengo kwambiri. Kodi ndife ololera kuika mwachibadwidwe cha wantchito ndi kumvera kwa Mbuye wathu?

MODZICHEPETSA DZITULUTSENI NOKHA
Kudzichepetsa kumakhudza kudzitulutsa tokha kuti tidzadzidwe ndi Mzimu Woyera. Iyi ndi ntchito yodzichepetsa payokha, koma pamene tikuyitanira Mzimu kutenga malo kukhazikika m'miyoyo yathu, timachoka pakukhala wodzipereka kukudzichepetsa kufikira popatsidwa mphamvu ku icho.

MODZICHEPETSA KUMALANDIRA MAU AKE
Dzichepetseni nokha pamaso pa Mau a Mulungu. Phunzirani kuwerenga bwino ndi kuwalandira mmene alili osawakakamiza kuti anana mokomera zosowa zathu. Modzichepetsa funitsitsani kumva choonadi cha Mulungu, osasamala kuti ndi chophunthwitsa bwanji kuti chitsimikizire ku maganizo athu okhazikika kale kapena okhazikitsidwa ndi miyambo yathu. Kuzindikira choonadi cha Mulungu ndi kugwiritsa ntchito mnzeru zake kumafunika kudzichepetsa.

MODZICHEPETSA TUMIKIRANI IWO AMENE TIKUFUNA KUWAFALITSIRA MAWU
Kulalikira ndi kofunikira kwambiri, komanso tikonde iwo amene tikuwalalikira. Tidzitumikira iwo amene tikufuna kuwalalikira. Titumikire iwo amene ali osowa. Pamene tikulingalira kukonda anthu bwino tiyenera kumvetseranso kwa iwo bwino. Ngati chimene tingachite ndi kuwalankhula kokha, ndiye kuti tikhoza kusemphana ndi mfundo zofunikira kwambiri zapakati pa uthenga wabwino ndi miyoyo yawo ndi kuchepetsa kuthekera kwa kukhala ndi ubale wabwino ndi iwo.

Polemekeza Mulungu, kupereka mpata kwa Mzimu kugwira ntchito mwa ife kumangirira pa choonadi cha mawu ake tingathe kukhala atumiki amphamvu mdziko – amene akumane ndi zosowa zochitika, mvetserani bwino kwa anthu (dera lalikulu mu kufalitsa limene limatayiriridwa), ndi mokhulupurika kulalika za mbiri ya Yesu. Ngati tikufuna kukhala opindula mu kufalitsa kwathu, kuyima kwathu poyambirira kuyenera kukhala kudzichepetsa pamaso pa Ambuye. D.L. Moody akutipatsa njira iyi mu ulaliki wake wa kudzichepetsa:

> 'Ndili ndi mtengo wa peyala pakhomo panga umene ndi okongola kwambiri; umaoneka kuti ndi umodzi wa mitengo yokongola pa malo anga. Nthambi iliyonse imawoneka kuti ikufikira kuwala ndi kuimilira ngati chikonga cha kandulo, koma osadyapo chipatso chake chochokera mumtengo wake. Ndili ndi mtengo wina umene unadzadza ndi zipatso chaka chatha zakuti nthambi zake zinalendewera kutsala pang'ono kugunda pansi. Ngati tingadzitsitse pansi pang'ono, anzanga, Mulungu adzatigwiritsa ntchito aliyense wa ife kuulemero wake.'

ZOKAMBIRANA (MPHINDI 15)

Unikiranani mafunso ndi / kapena zokambirana zonenedwa zotsatirazi:

1. Kodi pali madera mmoyo mwanu amene mumavutika ndi kudzichepetsa?

2. Kodi pali kulimbana kokhazikika pakati pakupereka uthenga wabwino ndi mphamvu ndi kugawa uthenga modzichepetsa?

3. Kodi tingathe mwachikondi kulankhula ndi vuto losowa kudzichepetsa kapena kupeza kudzichepetsa kwa chinyengo mwa ena?

> 'Ndakopeka kuti Chikondi ndi kuzichepetsa zokhoza kwambiri mu sukulu ya Khristu ndi umboni owala zedi wakuti Iye ndi Mbuye wathudi"
>
> **JOHN NEWTON**

KUCHITA ZIMENE TAPHUNZIRA (MPHINDI 5)

Ganizirani mosamala za mmene mungatumikire ndi kudalitsa iwo amene atizungulira munjira yosayembekezera ndi yosadula. Kodi utumiki wanu kapena mpingo wanu unalemba ntchito munthu okolopa? Muuzeni kuti apite ku tchuthi cha tsiku limodzi kukakhala ndi banja lawo kapena mumbindikiro wa uzimu ndi kugwira ntchito yawo. Khalani oyamba kupanga tiyi kapena khofi siku lililonse. Apatseni tipi ogwira ntchito mmalo ogulitsa zakudya mokoma mtima mutatha kudya chakudya ndi kuwalembera pa pepala zosonyeza Chikondi cha Mulungu kwa iwo... Khalani okonda kupereka zinthu ndi kuchita zinthu ndi cholinga.

Mbali ina, palibe mwa zinthu izi chimene chingagwire ndi mphamvu yodzadza ya Yesu yosambitsa mapazi a ophunzira ake, komanso kwinaku, zisangotchulidwa ngati zochitika za 'apo ndi apo za kukoma mtima'. Izi ndi zochita zadala za kuganizira, kukonda ndi kudzichepetsa kwa anthu amene amaona mwayi pa zonse zowazungulira kudalitsa ena munjira zakuti zikulozera kwa mtumiki wotonzedwa. Sitichita izi kuti tikonderedwe ndi Mulungu kapena kuwoneka abwino pamaso pa ena (zoona mzakuti sitinka tikukuwa za zinthu zimene tikuchita pa masamba a mchezo) – timachita izi ngati njira imene tingaphunzirire kukula mu kudzichepetsa, ndipo ngati chinthu chachibadwa chotuluka mu kudzichepetsa kumene Mulungu akukukuza mwa ife.

PEMPHERO

Thokozani Mulungu chifukwa chakuzichepetsa kwa Khristu ndi chitsanzo cha mtima wake wotumikira. Pemphani Mulungu kukuthandizani kuti mudzione nokha monga mmene Iye amakuonerani inu, ndi kuti mudzakula mu kudzichepetsa ndi nzeru tsiku lili lonse. Pemphereranani wina ndi nzake, kuti mukhale olimba ndi odzichepetsa mukalalikira kwanu kwa uthenga wabwino.

UDINDO WA KHLAIDWE LANU (MPHINDI 15)

Itanani wina aliyense amene akulimbana ndi kunyada kuti avomereze ichi - chimene movomerezeka ndi chovuta kwa munthu onyada kuchita - ndi kupemphera pamodzi ndi iwo ndiponso kuwapempherera, kuti Mulungu akuthandizeni nonse kukula mu kudzichepetsa ndi kutukula mtima wa wantchito.

Malizani fomu ya udindo wowona khalidwe lanu gawanani awiriawiri kapena mmagulu a anthu ochepa ndi kupemphererana wina ndi nzake.

OSAIWALA...

Njira imodzi yodzichepetsa ife eni ndi kuvomera kuti sitidziwa zonse ndipo tikusowekera kupitiliza kuphunzira. Gawo la Blog la Advancegroups.org/blog kawirikawiri limapereka bukhu la nkhani ndi kuphunzitsira zimene zidzatithandize kukhwima mu chikhulupiriro ndi umboni wathu.

POLEMBA

PHUNZIRO 9:
MWAYI WA MLALIKI

Chizindikiro chimodzi cha mphatso yakufalitsa ndi kutha kuona – ndi khumbo lochitapo kanthu – mwayi uliwonse umene wapezeka kugawa uthenga wabwino ndi iwo amene atiyandikira. Muphunziro lino tidzaunikira za mmene tingagwiritsire ntchito mwayi ulionse.

KUFOTOKOZERA PHUNZIRO

Nthawi zonse tidzikhala okonzeka kugwiritsa ntchito mwayi umene wapezeka wa uthenga wabwino umene tingaupeze, kufotokoza nkhani yabwino momveka bwino zochitika zili zonse ndi mu nyengo zonse.

CHIYAMBI CHA PHUNZIRO

Petro akutiuza kuti tidzikhala okonzeka nthawi zonse kugawa uthenga wabwino kwa aliyense wakukufunsani chifukwa cha chiyembekezo chiri mwa inu (1 Petro 3:15). Paulo akuuza Timoteo kukhala okonzeka kulalikira mawu, kuchita nawo pa nthawi yake muzochitika zonse za moyo (2 Timoteo 4:2) ndipo akulemba kwina kwake kuti tichite machawi nthawi ingatayike (Akolose 4:5). Yesu akusonyeza moyo wokhala chikonzekere kutumikira ndi kugawa nthawi zonse. Nthawi zina kutanthauza kuti kuyang'ana mmalo mosayembekezereka kuwona mwayi (monga anachitira ndi Zakeyo mu Luka 19:1-10), kukhala okonzeka muzochitika zobetchera za makhalidwe a anthu (monga kwa mayi wa ku Samaria mu Yohane 4:1-26), kulimba mtima pa malo a mwayi (kumbukirani mayi wochimwa mnyumba ya mafalisi mu Luka 7:36-50) kugawana ndi anthu opilikitsidwa mmudzi (monga kuchiritsa a khate mu Luka 17:11-19) kapena kulengeza choonadi nthawi ya masautso anu omwe (monga anachitira ndi mbamva ya pa mtanda mu Luka 23:39-43)... Ndipo ndandanda ukupitilira.

Misonkhano ya chitsitsimutso ya Billy Graham kudzera kumene analalikira kwa anthu ambiri kuposa munthu wina aliyense amene anakhala ndi moyo – anali wotchuka kwambiri munkhani ya kufalitsa. Koma ichi sichinali njira yokhayo imene Billy anagawira uthenga wabwino mmoyo wake wonse. Kaya akukumana ndi atsogoleri kapena afumu, kuwonekera pa njira zina za zoyankhula pa makina monga wailesi ndi kanema, kubweretsa chithandizo mmadera amene kuli ngozi zadzidzidzi, kutumikira asirikali a kunja kwa dziko, kapena kugawana ndi munthu mmodzi payekha mkati mwa njira, Billy nthawi zonse anali okonzeka, anakonzeka ndi kulolera kugawa uthenga kwa iwo amene anakumana nawo.

Chikonzero cha misonkhano ya chitsitsimutso cha Billy Graham sichinatakasidwe ndi kumasulira kwa kukulitsa kwa utumiki waukulu. Chimene chimamupatsa mphamvu ndi kuwona mwayi ndi kugwiritsa ntchito danga lililonse lopezeka kuchokera kukumvetsetsa kowona, kulandiridwa, ndi kugonjera kwa uthenga wabwino kwa iye mwini.

Chizindikiro chimodzi cha amene anadalitsidwa ngati alaliki ndi chakuti mosakaikira amakhala wachifundo chachibadwidwe cha kwa anthu otayika chimene chimadutsa kukhutitsidwa kwa kukwaniritsa ntchito za kufalitsa kapena mwayi olalikira. Mlaliki amakhala kakasi kuti aliyense amve ndi kulandira uthenga wabwino, ndipo, ngakhale pansi pa chiwopsezo cha kunyozedwa ndi zotsatira zowawa, sakanatha kudzisiyitsa iwo okha kuyankhula za Yesu pa mwayi uliwonse (Machitidwe Atumwi 4:18-20 koma choonadi ndi ichi, pamene okhulupirira osati okhawo ali ndi mphatso ya ulaliki – akumvetsetsa nkhani yabwino kwa iwo eni ndi kukhala moyo mkati mwa chisomo chodula, ndiye kuti akula kwambiri muchifundo cha kwa anthu otayika, kugawana nawo muchifundo cha Mulungu

mwini pamene tikukula mmoyo watsopano wa mu chifanizo chake.

Mbiri yeniyeni yopatsa chidwi ya Desmond Doss, imene inanenedwa ndi wopanga kanema wa Hollywood ndi Kacksaw Ridge, amavumbulutsa mwamuna amene anakopeka kulembetsa ngati wachipatala mnthawi ya nkhondo ya dziko lonse lapansi yachiwiri, koma amene anakana kugwira mfuti mwanjira ina iliyonse chifukwa cha chikhulupiriro chake chozama mwa Mulungu. Anatumizidwa ku zilumba za ku Japan za Okinawa, Doss anapezeka kumbuyo kwa adani pa "Hacksaw Ridge". Pansi pa kuwombela kwa mfuti kwa adani anamvabe kulira kwa asirikali ovulala a gulu la adani onse pamodzi a ku America ndi a Japan – Doss anayamba kupulumutsa aliyense amene akanatha, chimene chinakhudza kuwatsitsa kuchoka pa mlatho kugwiritsa ntchito chingwe chongopanga kuti chigwire ntchito ngati dongosolo la chigudumwa chokokera zinthu. Doss anawomberedwa pa mkono wake ndi mufti ndipo kenaka anazindikira kuti anali ndi zipolopolo khumi ndi mphambu zisanu ndi ziwiri mthupi mwake, ndipo anapitiliza kugwira ntchito mmene akanathera kuti apulumutse anthu ambiri.

Pofunsidwa za nkhaniyi zaka zotsatira Doss anafotokoza kuti pamene kutopa kunafika ndi kumva kuti sakadatha kuthandiza aliyense anapemphera. "Ambuye, thandizeni kupeza ena". Doss anapulumutsa pafupifupi amuna 75 pa mzere umenewo.

Pemphero la Doss ndi kulira kwa mlaliki. Ndi kulira kwa onse amene amagawa mtima wa Mulungu kwa anthu otayika. "Ambuye, kudzera mu mwayi uliwonse, kaya ovuta kapena odula ndithandizeni kupeza ena.

MLOZO WA PHUNZIRO

KUKUMBUTSA ZA MBUYO (MPHINDI 10–20)

Khalani ndi nthawi yokambirana wina ndi nzake, kugawana nkhani, zilimbikitso kunena za mwayi ndi chilichonse chimene chingalimbikitse gulu. Kwa magulu ochepa, funsanani wina ndi nzake za kugawana chipambano kuchokera pa msonkhano wapitawo kwa magulu akuluakulu, sankhani anthu anayi kapena asanu kugawana umboni wapaderadera kuchokera ku msonkhano watha.

PEMPHERO

Dziperekeni nthawi iyi kwa Ambuye ndi kupempherera china chili chonse chabwino kapena chobetchera, zimene zatchulidwa pa nthawi ya kulandirana ndu kumbutsana za mbuyo.

KUPHUNZITSA (MPHINDI 20-30)

Werengani bukhu lophunzitsira lotsatirali munjira yanu, kapena, powerenga liwu ndi liwu kapena kuwerenga pamene mukapereka phunziro.

> '"Koma Petro ndi Yohane anali kukwera kunka ku Kachisi pa ora lakupembedza, ndilo lachisanu ndi chinayi. Ndipo munthu wina wopunduka miyendo chibadwire ananyamulidwa, amene akamuika masiku onse pa khomo la kachisi lochedwa Lokongola, kuti apemphe zaulere kwa iwo akulowa m'Kachisi; ameneyo, pakuona Petro ndi Yohane akuti alowe m'Kachisi, anapempha alandire chaulere. Ndipo Petro, pompenyetsetsa iye pamodzi ndi Yohane, anati, Tiyang'ane ife. Ndipo iye anabvomereza icho, nalingalira kuti adzalandira kanthu. Koma Petro anati, siliva ndi golidi ndiribe; koma chimene ndiri nacho, ichi ndikupatsa, M'dzina la Yesu Mnazarayo, yenda."
>
> **MACHITIDWE ATUMWI 3:1-6**

Ndi chinthu chophweka kusemphana ndi mwayi. Anthu ambiri amakhala otsutsika mmoyo wawo chifukwa cha nthawi ina imene anataya mwayi mmbuyomo – zinthu zimene amalakalaka akadachita akadalimba mtima ndi kuyesera, kapena zimene sakadandaula konse za zimene anthu angawaganizire atachita.

Dziko la masamba a mchezo ladzutsa kukwera kodabwitsa kwapadera kwa "mantha akuti zisandidutse (MAZ). Mudziko lolumikizidwa pompopompo, tingathe nthawi zonse kuwona zimene anthu akuchita - ndipo pamene

zikuoneka ngati ena akukhala ndi moyo wabwino kuposera ife. MAZ amabwera. kulankhula kwina MAZ akuganiziridwa ngati zotsatira zapadera za kalumikizidwe kosathandiza ndi kopanda ukhondo kodi nanga tingawerenge Buku Lopatulika ngati? Kodi munayamba mwakhalapo ndi mantha akuti mukutsalira mutawerenga za zimene anachita ophunzira a Yesu ndi mpingo woyamba mu bukhu la Machitidwe a Atumwi?

Kuwerenga zokhudza Atumwi mu Chipangano Chatsopano kumatisiya ndi maganizo owona kuti tikutsalira pa mulingo wa pa chiwopsezo chimene anakumana nacho pogawa uthenga wabwino. Pamene ambiri mwa ife sitilakalaka zinthu zochititsa mantha – monga kuphedwa kuponyedwa miyala (!) - tikadakonda kuwona ndi kuchita nawo mu zizindikiro ndi zodabwitsa zimene zinatsatira utumiki wa a Atumwi.

Mu Machitidwe Atumwi 3, Petro ndi Yohane anapezeka kuti apatsidwa zochita za tsiku lililonse: wopemphetsa wopunduka miyendo anawapempha iwo ndalama. Chinali chosavuta kwa atumwi awa kungomudutsa bambo watsoka ameneyu, kapena kumupatsa ndalama yochepa ndi kupitilira.

Yang'anitsitsani mwapadera chilankhulo chili apa: Petro ndi Yohane anayang'ana mmaso munthuyu, kumasulira kwa NRSV kukuona Petro ndi Yohane akuyang'anitsitsa mwacholinga munthuyu, amene pobwezera analunjika chidwi chake muchiyembekezo cholandira china chake.

Kukambirana: Kodi mukuyang'ana bwanji ndi cholinga mudziko limene lakuzungulirani? Muli bwino bwanji popeza ndikuwona mwayi wapezeka woti mugawe uthenga wabwino?

Bambo wopunduka anaona mwayi wopeza chinthu china chimene anaona kuti chinali chosoweka pamoyo wake – ndalama. Mwamwayi wake, Atumwi amalabadira za mwayi umene unali patsogolo pawo, kutanthauza kuti anali ndi kuthekera komupatsa chimene amachisowa koposa Yesu. Chinali Chikondi cha kwa anthu otayika chinapangitsa Petro ndi Yohane kuima, osati chifundo chakuti chakupunduka kwake kapena udindo ulemu wake mmudzi.

Buku Lopatulika limatiuza kuti iye amene andilemekeza ine, inenso ndidzawalemekeza (1 Samuel 2:30). Ichi ndi choona chachikulu choposa ndi pamene tilemekeza Mulungu mu "zinthu zazing'ono" pamene tikutsindikiza kukhala odalilika mu mmalo a chinsinsi – mu mmalo osazindikilika bwino a moyo – Mulungu amatidalira ndi zinthu zazikulu kwambiri. Pakhoza kukhala pamsanja yayikulu, koma chifukwa chiyani timakhazikika pa chinamtindi cha anthu? Chabwino choposa msanja yayikulu chiomasonyezedwa ndi mphamvu ya mzimu woyera mmiyoyo yathu. Kudzadza kotheratu kwa mzimu wa Mulungu wa moyo kulipo lero pamene mukugo njera kwa Ambuye, koma zikuoneka ngati kukhulupirirra kodzadza kwambiri ndipo kawirikawiri kwamene iwo amene akudziwa adzagwiritsidwa ntchito bwino kwambiri mu tmiki wake. Wina aliyense mugulu la a nkhondo a Israel akadatha kugonjetsa Goliati ndi chithandizo cha Mulungu, koma anali David amene anabwera poyera ndi kutsimikiza kudalilika kwake mu ntchito yapaderadera, kotero kuti ulendo wopita kumpando wachifumu unayikidwa.

Ngati mukufuna kuona zoopsa zodzadza, khalani okhulupirika mu zinthu zazing'ono, mu mwayi opezeka tsiku lirilonse, ndi kuona chimene Mulungu amachita. Ngati mukulimbana ndi kukhala olimbikitsidwa pokhudza kugwiritsa ntchito mwayi umenewu, pemphani Mulungu akuchotseni pamalo anu a mtendere ndi kulimbikira kusankha mwadala ngakhale musakumva kutero. Ngati mukusawutsidwa mkati mwanu pokhudza za mwayi umene munasemphana nawo ndipo mukumva ngati munakhumudwitsa Mulungu, kumbukirani kuti Mulungu sakufuna kuti inu muzidandaula za kusemphana ndi mwayi umene unapezeka akufuna kuti inuyo mukonde otayika ndi Chikondi chanu pa iye.

Palibe aliyense wa ife amene ali wangwiro. Ngakhale atumwi analakwitsapo mukufalitsa kwawo ndipo anasemphana ndi mwayi umene unali patsogolo pawo. Mfundo ndiyakuti musadzimangirire nokha ku mulingo umene simungathe, umene umaunjika chipsinjo, koma kudzimangirira tokha ku chikondi chopanda malire cha Mulungu chimene chimaunjika pachisomo. Ndi kuchokera pa chenicheni ichi pamene timakula, kukhwima kukhala woonjezera muchikhulupiriro ku mwayi umene Mulungu amatipatsa patsogolo pathu tsiku ndi tsiku.

D.L. Moody motchuka ananena kuti Mulungu wandipatsa bwato la moyo ndipo anati .... "Moody, pulumutsa onse amene ungathe." Kuthekera kwawo ndi kupalasa, kuwonetsetsa iwo amene akumira ndi kuwavuula mmadzi kukupezeka muchikondi chako cha Mulungu, ndi Chikondi chake ku dziko.

Pano pali maganizo a zochita atatu a mmene mungakhalire odziwa kwambiri za mwayi wa tsiku ndi tsiku ndi kukhala okhulupirika kwa iwo.

1. KABUKU KOLEMBAMO ZOCHITIKA TSIKU NDI TSIKU

Pali mfundo zambiri zothandiza za zofunikira kwakusunga zinthu polemba mubukhu. Ndi mwayi mmaganizo, lembani zonse mwatsatanetsatane za tsiku lanu. Munakhala nthawi yayitali ndi ndani ku ntchito kwanu? Kodi nthawi zonse mumadutsa munthu yemweyo wosowa nyumba tsiku lililonse pamalo pomwepo mu mzinda wanu tsiku ndi tsiku? Mumayankhula ndi ndani pa chipata cholowera ku sukulu? Kulemba mubukhu lanu lolembamo zochitika tsiku ndi tsiku kudzakupangitsani inu kusunga izi ngati zatsopano mmaganizo anu kotero kuti mudzatha kuwayika mmapemphero anu, komanso mungathe kugwiritsa ntchito izi ngati zowunikira za udindo khalidwe lanu poyera: Kodi mukuchita mwadala kuyankhula nawo zokhudza chikhulupiriro chanu mukucheza kwanu mu nthawi ikupita? Kodi zolankhulana zanu zakhala zopanda pake mwamasabata, kapena munayesetsa kupanga chotheka kuti muzame? Ngati mukumva kuti mutha, mukhonzanso kufunsa anzanu amene mmaunikirana nawo za khalidwe lanu kuti awerenge bukhu lanu la zolembamo ndi kukufunsani mafunso okhudza madera amenenewa.

2. ZOTSAMWITSA

Kodi bwanji osadziyikira zobetchera zanu ngati mukulimbana ndi kugwiritsa ntchito mwayi opezeka tsiku ndi tsiku? "Sabata lino ndikufuna ndilankhulane ndi mmodzi osamudziwa za khristu. Kubetchela uku kutha kukhala zochita kapena zolengeza, ndipo zikutengereni inu kukudutsitsani pa chizolowezi chanu cha kufalitsa.

3. ZOCHITA ZA CHIOPSEZO

Chotsani maganizo anu pa ntchito yanu kuziyika poopsa. Tili ndi udindo wa kufalitsa ndipo timafuna kukhala omvera watipempha kuti tichite, koma popanda Chikondi tikusemphana ndi mfundo. Ganizirani za mwayi umene ungapezeke musabata ikubwerayi osati ngati ntchito yolemetsa yokha, koma ngati mfundo yapamwamba ya kuchita chinthu chowopsa. Anthu ambiri amene ali mu gulu la oyamba nine-to-five grind - ngakhale amene amakonda ntchito yawo, amaona kuchedwa kuti mapeto a sabata afike. Kodi ife tili mu gulu la anthu amene timaona kuchedwa kudikira kuti mwayi wina upezeka liti wogawa Yesu ndi chidwi chomwecho? Ngati tingathe, tidzayambe kufungatira chowopsa ndi maganizo abwino, kotero kuti ngakhale chili chobetchera, tidzasasa fumbi ndi kupitanso.

Mau a Martin Luther,

> 'Ngati tili ndi chikhulupiriro, okhulupirira sangaletsedwe. Amadzinyenga yekha. Amasweka mtima. Amavomereza ndi kuphunzitsa uthenga wabwino kwa anthu pa chiwopsezo cha moyo wake womwe.'

ZOKAMBIRANA (MPHINDI 20)

Unikirani mafunso ndi / kapena zokambirana zonena ena zotsatirazi

1. Kodi munasemphako mwayi owonekera? Munaphunzirapo chiyani apapa?

2. Kodi chobetchera chachikulu munakumana nacho ndi chotani chakuti mugwiritse ntchito mwayi opezekeratu wogawa uthenga wabwino?

3. Kodi mmapanga mwadala bwanji mwayi wogawana uthenga wabwino umene mwina sukadapezekapo?

4. Kambiranani maganizo atatu kuchokera kukuphunzitsani (bukhu, kutchera, choopsa). Kodi mukuwona phindu la zinthu izi ndipo mutha kuzigwiritsa ntchito?

> '"Pali choonadi chachikulu – sinthani moyenera mulingo wanu ku zosowekera za anthu amene mukufuna kuti muwatumikire. Mukuyenera kutengera uthenga wabwino kwa iwo munjira ya kachitidwe ndi mnyengo

zimenezo pamene mudzapindulira iwo pakumvera iwo.'

CATHERINE BOOTH

KUCHITA ZIMENE MWAPHUNZIRA (MPHINDI 5)

Khalani mwadala mwezi uno za kugwiritsa ntchito mwayi umene nthawi zambiri mmatha kuwudutsa kapena mmasankha osachitapo kanthu. Kodi pali nzanu wakale amene mungamufikire? Kodi mungakhale ndi nthawi yapadera yokhala pansi ndi kulankhula kwa munthu opanda nyumba? Kodi mumagula khofi kwa ogulitsa khofi emweyo nthawi zonse, ngati ndi choncho kodi mungatembenuzire zokamba zanu kwa Yesu?

Ndi zachidziwikire kuti aliyense mugulu adzatha kuganizira za mwayi mu sabata yawo ya nthawi zonse imene adzathe mwadala za kugawana Yesu. Dziperekeni kutenga mwayi uwu pakati pa inu eni ndi kuwuzana wina ndi nzake kuti adzapereke ndondomeko ya zimene anapanga mwezi wamawa. Kumbukirani, ichi sichongokhazikitsa zolinga zodzagamula ndi muyeso oti tikwanitse koma kusintha chizolowezi ndi maonekedwe akhalidwe lathu. Chimene chimayamba ngati chochita mwadala chingathe kukhala khalidwe lachibadwa nthawi ikamapita.

Ganizirani zoyamba kukhala ndi bukhu lolembano zochitika tsiku ndi tsiku.

PEMPHERO

Thokozani Mulungu kuti amapereka mwayi wowonekeratu wolalikira uthenga wake ndi kugawana chikhulupiriro chathu ndi ena. Mupempheni kuti apereke mwayi wa paderadera mu nyengo imene mmwakhala kuyembekezera kwa kubowoleza, ndi mwayi wina wa tsiku ndi tsiku. Pemphereranani wina ndi mnzake kuti mudzawona moyenera a mwayi wokuzungulirani, ndi kukhala wokhulupirira kwa wina ndi mzake.

UDINDO WA CHIKHALIDWE CHANU (MPHINDI 15)

Atatuatatu kambiranani mwayi wopezekeratu umene mwautayirira. Lankhulani chifukwa chiyani mukuganiza kuti izi zili chonchi, Muyesere moonadi kufika ku mizu ya nkhani iyi. Funani chikhululukiro kwa Mulungu amene kuli koyenera kutero, ndi kulimbikitsana wina ndi mnzake mnjira zochitika za mmene mungachitire kupita chitsogolo mukugwiritsa ntchito mwayi umenewu mtsogolo.

Malizitsani fomu ya udindo wa khalidwe, gawanani awiriawiri kapena magulu anthu aochepa ndi kupemphererana wina ndi nzake.

OSAIWALA...

Chilimbikitso pakati pa magulu ndi gawo lalikulu la ulendo, khalani machawi mukulankhulana kwanu (kudzera mu njira ili yonse yotumizira uthenga imene gulu lingasankhe). Kukondwerera zipambano ndi zobowoleza, kutumizirana ndi kuyankha kuzopemphedwa kuti zipempheredwe ndi kuchezetsana wina ndi nzake.

POLEMBA

PHUNZIRO 10: KUDZIPERERA KWA MLALIKI

Buku Lopatulika ndi chibvumbulutso cha mayitanidwe a Mulungu kuti titembenuke kusiya machimo athu ndi kukhala ndi ubale ndi iye, kudzera muchikhulupiriro chathu cha mwa Yesu Khristu. Kodi tingatsimikizire bwanji kuti sitikungofotokoza ndi kulengezako kokha kuti uthenga wabwino ndi chiyani, molimba komanso tikuyitanira anthu kuti achitepo kanthu pamene zimene amva?

KUFOTOKOZA ZA PHUNZIRO

Ntchito ya kufalitsa ndi kudzipereka kolalikira uthenga wonse wa uthenga wabwino – zimene zikuphatikiza kuyitanira omvera kuti asinthe njira ndi kukhala ndi moyo woona kudzera muchikhulupiriro cha mwa Yesu Khristu.

CHIYAMBI CHA PHUNZIRO

Talingalirani mkwati pakhomo la kachisi pa tsiku lake la ukwati. Amayang'ana mozungulira nyumba imene yakongoletsedwa ali ndi abwenzi ndi abale odzadza ndi chimwemwe akudikira kulowa kwa mkwatibwi. Mkazi wa kumaloto kwake afika mphindi iliyonse. Mphindi khumi zatha koma mkwatibwi sanafike? Ndi chizolowezi kuti mkwatibwi amachedwa akuganizira mwa iye yekha kulibe chizindikiro kuti atulukira. Amaseka mwamantha. Mphindi makumi atatu zatha ndipo kukadalibe mkwatibwi ndipo palibe mawu amene abwera ofotokoza chimene wachedwera. Kenako amayamba kuda nkhawa pamene anthu amene asonkhana ayamba kung'ung'udza. Mphindi makumi anayi ndi zisanu, kenako ora, ndipo kukadalibe mkwatibwi. Kung'ung'udza pakati pa alendo oyitanidwa kwafika pachimake. Kodi chikuchitika ndi chiyani? Kodi wangochedwa kwambiri kapena wachita zosaganizirika ndipo waganiza kuti asabwere mkomwe?.

Maganizo a mkwati amayamba kuthamanga kuganizira zifukwa zonse zotheka za zimene zamuchedwetsa ndiye kenako mwadzidzi, mmimba mwake ndikutentha chikumbumtima chitamumenya sanamufunseko mkwatibwi kuti amukwatire iye.

Kuyitanira ndi kofunikira ngati pali mwayi wakuti munthu wina akhoza kuchitapo kanthu pa zimene wamva. Kumasulira mwachifupi kwambiri kwa uthenga wabwino kunalembedwa ndi Mark Motsatiramu: "Nanena nthawi yakwanira, ndipo ufumu wa Mulungu wayandikira; tembenukani mtima, khulupirirani uthenga wabwino" (Marko 1:15)

Mawu akuti "lapani" angathe kuyambitsa mavuto ochepa - makamaka chifukwa chakuti anthu ambiri sadziwa chenicheni chimene amatanthauza kulapa kawirikawiri kumalumikizana ndi "kutembenuka kapena kutentha kwa kachitidwe ka kulalikira kwa uthenga wabwino. kutanthauza kuti ena akhoza kumva ngati ndi kulengeza kokha kwa chiweruzo kwa anthu ambiri lero, mawu akuti lapani saoneka ngati ndi mawu a 'nkhani yabwino'."

Koma ngati timvetsetsa moyenera mawu akuti 'lapani' ali ndi chibvumbulutso chodabwitsa cha choonadi cha uthenga wabwino. Akutanthauza kuti kusintha maganizo, kusintha zochitika za moyo wanu. " Mukuyenda njira yolakwa; Yesu akutero, koma chifukwa cha ine mungathe kuyenda njira yolondola – njira ya choonadi imene imatsogolera kwa Atate". Kulapa ndi nkhani yabwino chifukwa kumapereka mwayi kwa aliyense amene wamva kudziwa moyo aliyense amene wamva kudziwa moyo mmalo mwa imfa. Tinadzibweretsera chiweruzo pa ife tokha chifukwa cha mwano wathu potsutsana

ndi Mulungu, kutembenuka ndi belu losonyeza kuti moyo wayaka kutichenjeza za choonadi chimenechi ndi kuyitanira kuzindikira Yesu ngati choonadi chimene chingatimasule.

Alaliki oyamba a uthenga wabwino anali osamalitsa kuphatikiza kupereka mwayi kwa omvera awo kuchitapo kanthu pa uthenga wawo, monga mmene Yesu anachitira. Kudandaulira kwa kulapa kunapangidwa ngati mapeto pa kulalikira mbiri ya Yesu (Machitidwe Atumwi 2:39-39, 3:25-26; 4:12, 5:31, 10:43)

Uthenga wabwino umapitiliza kuyitanira kwa anthu kusiya kuthawa kwa Mulungu kudzera mwa Yesu Khristu tikhoza kutembenuka ndi kuwonana ndi Mulungu ndipo tikamatero, tilolele maganizo anthu kukhala osinthika ndi choonadi cha chimene iye ali, ndi kuwona miyoyo yathu ikusandulizika ndi mphamvu ya Mzimu wake.

MLOZO WA PHUNZIRO

KUKUMBUTSA ZA MBUYO (MPHINDI 10–20)

Khalani ndi nthawi yowuzana wina ndi nzake, kugawana nkhani, zilimbikitso kukambirana za mwayi ndi china chili chonse chimene chingalimbikitse gulu. Gawanani za mwayi umene munakumana nawo mogwirizana ndi phunziro latha (phunziro la chisanu ndi chinayi: kuchita zimene mwaphunzira).

PEMPHERO

Khalani ndi nthawi ndi Ambuye ndi kuthokoza pa mwayi umene munali nawo mmasabata ochepa apitazo wogawira uthenga wabwino. Pemphererani iwo amene apereka chikhulupiriro chawo mwa Yesu kudzera mwayi umenewu.

KUPHUNZITSA (MPHINDI 30–40)

Werengani bukhu lophunzitsira mu njira yanu, kaya powerenga liwu ndi liwu", kapena kuwerenga pamene mukupereka phunziro.

> 'Koma pamene anamva ichi,analaswa mtima, natitu kwa Petro ndi atumwi enawo, Tidzachita chiyani,amuna inu abale" Koma Petro anati kwa iwo, Lapani, batizidwani yense wa inu m'dzina la Yesu Khristu kuloza ku chikhululukiro cha machimo anu; ndipo mudzalandira mphatso ya Mzimu Woyera. Pakuti lonjezano lili kwa inu, ndi kwa ana anu, ndi kwa onse akutali, onse amene Ambuye Mulungu wathu adzaitana.'
>
> **MACHITIDWE ATUMWI 2:37–39**

Kuyitanira ndi gawonso la uthenga la uthenga wabwino ngati mnene mtanda ulili. Atakumana ndi kubwera kwa Mzimu Woyera tsiku la Pentocost, Petro anayamba kulalikira ku khamu limene linasonkhana. Kudzera mu mphamvu ya Mzimu yogwira ntchito mu kulalikira kwake, gulu la anthu "analaswa mtima, pamene anamva nkhani ya mu uthenga wabwino.

Tangoganizirani pano nkhani yakutembenuka? Pamene gulu la anthu lakonzekera kukhulupirira Yesu, Petro mkunena kuti "zikomo ndipo gonani bwino! "ndikuchokapo kupita ku chakudya chokonzedwa bwino utatha ulaliki ndi anzake. khamu la anthu, anasiyidwa atasunthika ndi uthenga wake koma atasokonekera za mmene angachitire mmiyoyo yawo, kubalalika kubwerera ku miyoyo yawo ali ndi mafunso ambiri opanda mayankho, kukhala opanda mwayi oyika chikhulupiriro chawo kwa Yesu monga mmene Petro wawauzira iwo.

Tikuthokoza kuti ich sichimene chinachitika! Petro anawayitanira kuchitapo kanthu ndipo anaitana gululo kuti alape - kuwapatsa njira yeniyeni ya mmnene angachitire pa uthenga umene awumvetsetsa ndi kuchita kanthu pa kuyitana kwa Mzimu kumene kwachitika mmitima yawo. Uthenga wabwino wodzadza kumaphatikiza kuyitanira kukulapa, ndi kufotokozera za mmene angachitire pa chimene amva. Ophunzira anadzipereka mokwanira ku kulalikira uthenga wabwino wonse ndiye choncho zitero.

Kwa iwo onse amene amakonzekera ulaliki kapena kulankhula, mudzadziwa kufunikira kwa kuphatikiza njira zina zakagwiritsedwe ntchito ka uthenga ku moyo watsiku ndi tsiku. kulalika kwa Yesu ndi kwa atumwi kunadzadza ndi zinthu zochitika zokhudza moyo wa tsiku ndi tsiku. Kupereka kwa uthenga wabwino koyambira kwa Yesu mu Marko – kuyitanira

‘lapani , ufumu wa Mulungu wayandikira’ ndi wochita: akunena kuti “Nonse mukuyenda njira yolakwika, mukufunika kutembenuka ndi kudziwa kusandulika!

Mu uthenga wabwino wonse Yesu mobwerezabwereza akupitiliza kuyitanira: “Idzani kuno kwa Ine nonsenu akulema ndi akuthodwa (Mateyu 11:28) “Tiyeni mukaone” (Yohane 1:39) “Tiyeni pa mbuyo panga” (Mateyu 4:19) “Ngati pali munthu akumva ludzu adze kwa ine namwe” (Yohane 7:37) “Idzani mufisule (Yohane 21:12).

Kuyitana kumeneku sikungoweruza chabe kapena kopanda pake, kukuwulula chidziwitso chenicheni cha Yesu ku dziko lapansi ndipo kuli ndi zotsatira zenizeni za zimene zingachitike mukalandira kapena kukana. Chinthu chotanthauzira cha kuyitanira ndi chakuti kumafuna kuchitapo kanthu. Ngakhale kukhala pansi pa mpanda ndi kukana kuyitanira pakuti ndi “inde” yekha kumabweretsa kulandira kwa kuyitanira ndi madalitso amene amatsatira.

Kambiranani: Yang’anani zitsanzo zitatu izi za mu Buku Lopatulika za kuyitanira ndikudzikambirana ngati gulu:

1. Kuyitana kwa ophunzira (Marko 1:17) kuyitana kwa munthu payekha

2. Kuyitana kwa wachinyamata wachuma (Mateyu 19:16-22) kuyitana kwa Yesu kuli ndi malipiro

3. Kuyitana akufa (Yohane 11:43) kuyitana kwa Yesu ndi kwa mphamvu.

Mwayi wochitapo kanthu ku uthenga wabwino ndi chinthu chofunikira kwambiri pakulalikira. Kulengeza uthenga wabwino weniweni, tiyenera nthawi zonse kupereka malo oyitanira kulandira Yesu ngati Mbuye ndi Mpulumutsi.

Izi zingakhale zovutirapo – mwayi wina wa uthenga wabwino umaoneka kuti wapezeka wabwino kuposa wina poyitanira kuti achitepo kanthu. Tsono ndingathe bwanji mokhulupirika “kuyitana” kuchitapo kanthu pa kufalitsa kwathu, osatengera kuti tili munyengo yotani kapena nthawi yotani? Kaya tili pa msanja kapena tikulankhulana ndi munthu payekha, tisangokhala odzipereka kuwafunsa anthu kubwera ku kachisi kumapemphero a tsiku la Mulungu (ngakhale muchite izi mwanjira ili yonse) komanso kukhala odzipereka kuyitanira anthu ku ufumu wa Mulungu. Sitingapeze mlozo wotilozera mlingo uli wonse wa izi mmalemba, koma mfundo izi zikupereka malo abwino oyambira.

FUNSANI MAFUNSO A CHINDUNJI

Mafunso anu akhale achindunji ndi ophweka. Mwachitsanzo, mutafotokoza kuti Yesu ndi ndani ndi chimene chikutanthauza kumutsata iye, mosavuta funsani; “Kodi mungakonde kuyika chikhulupiriro chanu mwa Yesu Khristu ndi kuyamba moyo watsopano wa ubale ndi iye? Kapena kodi pali chinthu china chake chikuletsani kuyika chikhulupiriro chanu mwa Yesu lero?

Ngati munagwiritsa ntchito chitsanzo kapena mwambi kulumikizitsa ndi anthu amene mukuwafikira, gwiritsani ntchito izi ngati mfundo zoti mulunjikepo. Mwa chitsanzo, ngati mukugawana kuchokera ku nkhani ya mwana wolowerera; “Mulungu akukuitanani kunyumba lero. Kodi mukufuna kubwerera kunyumba mu fukato wa Mulungu monga mmene mwana wolowerera anabwererera kwawo?” Funso ili ndi lothandiza inu kuti muone ngati omvera anu ali omasuka kunena inde kwa Yesu. Chotsatira, mubweretse kumvetsetsa kwabwino kwa kuyankha kwawo, koma funso lanu loyambirira likhale lachindunji, lophweka ndi lolumikiza ku uthenga umene mwagawa kale.

SUNGANI NTHAWI YOFUNIKIRA

Pamene mukukanhula ku chinamtindi cha anthu, dikirani mwanthawi iliyonse mpaka mumve kutsogozedwa kuti mulole Mzimu akhudze mitima ya anthu. Kaya zitenga nthawi yayitali bwanji (kapena mukumva ngati zowoneka zolakwa) ndi zosafunikira kwenikweni chofunikira kwambiri ndi chakuti anthu ali ndi nthawi yoganizira za zimene zapatsidwa, ndi kuti mupereke danga kwa Mulungu kuchita zimene akufuna kuchita. Pa nthawi yogawana wina ndi nzake, zikhoza kutheka kuti Munthuyo akufunikira nthawi ndi mpata kuganizira choncho kukhonza kukonza nthawi yokumananso kukambirananso izi. Kumbukirani, sitikuyesera kukaniza kapena kuwumiriza kuti achitepo kanthu, tikuyang’anira kwa Mulungu kulowererapo pa nthawi yake, kotero kuti

mukhale omasuka kulola kuti kuyankha kwa anthu kuchitike pa nthawi yoyenera.

MUPANGE ZOYEMBEKEZERA ZANU KUKHALA ZOMVEKA BWINO

Mulongosole bwino chimene chingachirike kwa munthuyo akavomera kuti inde ndi chimene akuyitanidwira. Mwa chitsanzo, fotokozani kuti mupemphera limodzi, mwinanso muwapatsa Buku Lopatulika ndi ndondomeko ya kawerengedwe, ndi kuti muwalumikizitsa ku mpingo kwamu kapena mpingo wina kapena magulu a ophunzira kuti mudziwalandola. Munene momveka bwino kuti sikuti moyo ukhala wabwino pompopompo, koma kuti kudzera mukudzikhula kwa tsiku ndi tsiku kwa Yesu, moyo wochuluka umene akupereka udzawonekera mosavuta. Fotokozani ndondomeko yotsatira za zochitika zotsatira ndi chenicheni cha uzimu cha moyo wokhala ophunzira umene umatsatira ukalandira Yesu.

KONDWERERANI KULANDIRA KHALANI NDI CHIFUNDO AKAKUKANANI

Pamene munthu akusonyeza kuti akufuna kulandira kuyitanidwa, alimbikitseni ndi chimwemwe. Musalole kuti zikhale zoti mwangopanga - ngati chimwemwe chanu sichenicheni ku mayankhidwe amenewa mwina nkutheka munadzitsogoza kwambiri kugawana uthenga wabwino koyambirira; momwenso ngati munthu wayankha momvekeratu kuti ayi, khalani achisoni ndi odzichepetsa yeserani kumusiya munthu amene wakana kuyitana ndi kuyitanira komasuka kuvomera pa okha, Mulungu adzionetsere yekha kwa iwo pa nthawi ina ndipo ngati mkotheka apatseni zoyenereza kuti ngati angakufuneni athe kukupezani kapena alozereni ku mpingo waderalo kumene angathe kupita atavomera.

Chimodzi mwa zifukwa zodziwika bwino zimene anthu satha kulandira ndi chakuti palibe amene amawayitana. Chimodzi mwa zifukwa zodziwika bwino zimene alaliki sayitanira kuti anthu achitepo kanthu ndi chakuti amawopa kuti palibe amene avomere ndipo iwowo (kapena uthenga wabwino) awoneka opusa. Koma mphamvu ya Chipulumutso siyanu, ndipo ngakhale Yesu anali ndi anthu amene anamuthawa kukana kuiyanira kwake. Tinayitanidwa kungokhala okhulupirika ku uthenga wabwino, kuyitanira ndi zonse, ndi china chili chonse chotsatira. Choonadi chake ndi chakuti kuyitanira kwa Khristu ndi kwa ife kubwera ndi kudzifera, kunyamula mtanda wathu ndi kumutsata iye (Mateyu 16:24) kutanthauza kuti kudzifera tokha ndi kufalitsanso, osalabadira kuti mtengo wake ndi wotani kapena kuti tingawoneke woputa.

Yesu ndi atumwi anayitanira pamene amalalikira uthenga wabwino ndipo nafenso titero. Osalabadira mayankhidwe tingatsimikiziridwe kuti takhala okhulupirika ndi uthenga wa uthenga wabwino ndi chindunji chake chamayitanidwe kuyitanira kulapa ndi kukhulupirira Yesu Khristu. Mulungu adzasamala zina zonse.

ZOKAMBIRANA (MPHINDI 15)

Unikirani mafunso otsatirawa:

1. Kodi ndi zotheka kulalikira kwenikweni uthenga wabwino popanda kupereka mwayi wochitapo kanthu ku chikhulupiriro mwa Yesu?

2. Kodi chimene mmapeza kuti chovuta / chophweka ndi chiti zokhudza nkhani yakuchitirapo kanthu ya kufalitsa.

3. Kodi mwaphunzirapo chiyani za kuthaniza anthu kuchitapo kanthu pa uthenga wabwino umene mwafalitsa,

KUCHITA ZIMENE MWAPHUNZIRA (MPHINDI 5)

Chitani mwadala za kupereka mayitanidwe akuchitapo kanthu pa za uthenga umene mwagawa nthawi ili yonse. Mwina ndinu mlaliki wa pa msanja amene mwakhala mukulimbana ndi nkhani iyi. Yeserani njira zina zosiyana za kuitanira anthu kuti achitepo kanthu ndipo musawope kuwoneka kupusa ngati palibe amene wachitapo kanthu. Momwemonso, mwina ndinu katswiri woyambitsa anthu za Yesu, koma mmakanika kulumikizitsa ku ndondomeko zotsatira. Tulukani molimba mtima mwezi uno ndi kufunsa mmunthu mmodzi mutatha kukambirana za uthenga wabwino ngati angafune kupereka chikhulupiriro chawo kwa Yesu.

PEMPHERO

Thokozani Mulungu pakuyitanira kwake kumene amapereka kwa mmodzi modzi wa ife kubwezeretsedwanso kwa Iye. Mupempheni kuti mulimbe mtima pamene mukugawa uthenga wabwino ndi kuti tikhale omveka bwino ndi wolimba pamene tikuyitanira anthu kukulapa – kuwathandiza iwo kuti asangowona kuweruzidwa koma awone chiyembekezo. Pempherani kuti mitima idzamva mayitanidwe amenewa.

UDINDO WA KHALIDWE LANU (MPHINDI 15)

Awiriawiri, kambiranani za dera la moyo wanu za zimene mukuganiza kuti mukufunikira kugwirapo ntchito pang'ono molingana ndi mawu akuti "kudzifera." Tonse tithe kumalimbana ndi madera mafano, kapena khalidwe lina loperewera limene likufunika kugwirapo ntchito. Pamene tikuganizira zopereka maitanidwe a uthenga wabwino kwa ena, tiyeni tionenso maitanidwe omwewo atsopano amene Mulungu akupereka - kudzifera tokha ndi kumutsatira iye. Limbikitsanani ndi kupemphererana pamene mukugawa mudera ili.

Malizani formu ya udindo wa khallidwe lanu, gawanani awiriawiri kapena magulu ang'onoang'ono ndi kupemphererana wina ndi mzake.

OSAIWALA...

Msuntho uli ndi (podcast channel) chimene chimaonetsa nkhani zosiyanasiyana za kuphunzitsa ndi chilimbikitso. Fufuzani Msuntho (advanced) pa podcast channel platform kapena lowani pa advancegroups.org/podcast kuti mupeze zambiri ndi kumvera.

POLEMBA

PHUNZIRO 11: CHILIMBIKITSO CHA MLALIKI

Utumiki wa ofalitsa sikungolalika kokha uthenga wabwino kwa anthu a mdziko komanso kugwedeza mpingo wonse kukufalitsa. Muphunziro lino tiwunikira za mmene tonse tingatengere gawo kukhala oyatsa moto mu mpingo kuti tithandizire kulimbikitsa ndi kupereka zida kwa onse amene atizungulira kukhala okhulupirika kwa Mulungu mu kufalitsa

KUFOTOKOZERA PHUNZIRO

Pambali pa kulalikira uthenga wabwino ku dziko, Mlaliki adzadzikhuthulanso kukugwedeza mpingo kufalitsa polimbikitsa ndi kupatsa mphamvu oyera mtima ku ntchito ya utumiki.

CHIYAMBI CHA PHUNZIRO

Chifukwa chakukula kwa masamba a mchezo kwadza mtundu wina wakutchuka wotchedwa "mkoka." Awa ndi anthu amene akoka anthu ambiri owatsatira pa tsamba lawo lamchezo (makamaka youTube) ndipo kuti amatha kukopa gulu la anthu. Izi sinzeru zatsopano kwenikweni - anthu otchuka kuchokera kumsangalutso ndi masewero akhala akutiwuza ife kwa zaka kudzera muzimene amaika kuyitanira malonda za zimene tivale, tinunkhirire. Koma m'bado uwu wa anthu otchuka ndi woyamba kusonkhanitsa anthu wowatsatira ndi cholinga chongofuna kukopa anthu basi.

Paulo akutiuza ku Aroma kuti tisafanizidwe ndi makhalidwe a pansi pano, koma tikhale osandulika mwa kungonjera kwa Mzimu woyera (Aroma 12:2). Monga ngati anthu oyera a Mulungu, ndife anthu oyambirira a mkoka, ndi uthenga umene umabweretsa moyo, mtendere ndi chiyembekezo.

Muphunziro lachisanu ndi chiwiri, tinakumbutsana kuti mchere umene wasuluka ulibe ntchito. Mphamvu za mkoka wa pa masamba a mchezo umadalira kuti otsalira tsamba lake ndi angati ndi mmene omutsatirawo akuchitira ndi zimene iye akufuna zichitike. Kwa mpingo kusiyanitsidwa kwathu ndi kofunikira koposa, ndipo kutaya chimenechi ndi chinthu chosapindula. Mkoka wa pa masamba a mchezo akhoza kusiya kutchuka ndi ntchito yawo pamene akuguga kukhala achikoka. Koma ngati mpingo utaye makopedwe ake ndi kutaya kusiyanatsidwa kwawo. Dziko lapansi lidzataya mwayi wowona uthenga wabwino ukukhala moyo ndi kumva ukulalikidwa mu njira imene ingathe kumvetsetsa.

Alaliki ali ndi chifundo kuwona dziko lapansi likulandira uthenga wabwino, komanso akhale ndi chifundo chopitiliza kutasaka mpingo kunyamula mkoka wa dziko lapansi. Mzonse izi, palibenso ndondomeko ina ikubwera yokhudza nkhani ya uthenga wabwino ndi kuti mpingo wa Yesu Khristu akazembe ake okha. Pamene mpingo wayiwala ichi kapena kukhala osokonezedwa, alaliki ndi ena amene ali ndi chikondi chakuchita kwa kufalitsa mnjira ina ili yonse angathe mwachikondinso kutsira mafuta ndi kusunga moto wa kufalitsa kotero kuti mphamvu ya uthenga wabwino ikawale kuti onse awuone.

Kuti mpingo onse utengere uthenga wabwino wonse kudziko lonse lapansi ku ulemerero wa Mulungu.

MLOZO WA PHUNZIRO

KUKUMBUTSA ZA MBUYO (MPHINDI 10–20)

Khalani ndi nthawi ywuzana wina ndi mnzake, kugawana nkhani, zilimbikitso, kukambirana za mwayi umene umapezeka ndi china chilichonse chimene chingalimbikitse gulu. Gawani zokhudza zimene zikukuchitikirani pamene mumayitanira anthu kuchitapo kanthu pauthenga wabwino mowunikira phunziro latha (phunziro lachikhumi, kuchita zomwe taphunzira), kodi mwakhalapo ndi mwayi wokhala mwadala mudera ili kuchokera nthawi yapita? Ngati ndi choncho, zotsatira zinali zotani?

PEMPHERO

Khalani ndi nthawi ndi Ambuye ndikupempherera chinthu china chilichonse, chabwino kapena chobetchera zimene zatchulidwa mu nthawi ya kulandirana ndi kukumbutsana

KUPHUNZITSA (MPHINDI 20-30)

Werengani bukhu ili lophunzitsira munjira yanu, mwina powelenga iwu ndi liwu kapena kuwelenga pamene mukupeleka phunziro.

> 'Ndipo Iye anapatsa ena akhale atumwi; ndi ena aneneri; ndi ena alaliki; ndi ena abusa, ndi ena aphunzitsi; kuti akonzere oyera mtima ku ntchito ya utumiki, kumangirira thupi la Khristu; kufikira ife tonse tikafikira ku umodzi wa chikhulupiriro, ndi wa chizindikiritso cha Mwana wa Mulungu, kwa munthu wangwiro, ku muyeso wa msinkhu wa chidzalo cha cha Khristu.'
>
> **AEFESO 4:11–13**

Ngakhale iwo amene ndi a msanja yayikulu kwambiri ayenera chilimbikitso mmoyo, monga anachitira umboni ngwazi ya kanema ya Hollwood Dwayne "The Rock" Johnson mu nthawi yofunsidwa mafunso.

> 'Ndili ndi zaka zisanu ndi zitatu ndinaonera kanena ya "Raiders of the Lost Ark" in Charlotte ku North Carolina. Ndinatuluka mmenemo molimbikitsidwa. Ndinaikonda kanema imeneyo, ndipo ndinadziwa kuti ndi chimene ndimafuna kukhala ngati bambo ameneyo.'

Kambiranani: Munayamba mwakumanapo ndi munthu woti anakukopani kwakuti nthawi yomweyo munayamba kuchita kapena kukhala ngati iwowo? Chinali chiyani cha iwo kapena chimene anachita chimene chinakhala ndi mphamvu yosintha moyo wanu?

Kaya ndinu munthu wapabanja lanu, chinthu cha mbiri yakale chithunzithunzi cha khalidwe kapena ngakhalenso chithunzi cha zinthu zongopeka, tikhoza kupeza a chikoka malo onse osiyanasiyana. Chikoka china chimakhudza zochita zathu mwa chizolowezi, ndi ntchito zomwe timafuna kuti tidzagwire ndipo zimathanso kuumba khalidwe lanu ndi mmene timalionera dziko. Nthawi zina zimagwira ntchito mnjira ina – mukhoza kuona wina waluso koposa mwakuti amakuchititsani mphwayi ndi kusiya kuchita china chake: kodi Mfundo ndi iti, "sindingathe kukhala ngati iwowo!"

MuBuku Lopatulika muli anthu ambiri achikoka, ndipo ndi chinthu chopambana kuyang'ana ngwazi za chikhulupiriro zonse mmasamba a Buku Lopatulika komanso kunja kwa Buku Lopatulika – makamaka pamene tikuzindikira ichi, ngakhale ataoneka ochita bwino bwanji, anali anthu wamba okhala okhulupirira kwa Mulungu. Kudziwa kuti chifukwa chimene Mose anatha kulankhula mwamphamvu kwa Pharaoh sizinatengere luso lake lakulankhula koma kuchita chilichonse mokhulupirika ku maitanidwe a Mulungu ndi kugonjera ku mphamvu zake ndi chilimbikitso chokwanira ndi chikoka. Mulungu ndi yemweyo kotero tikhozanso kuchita zomwezo.

Mapeto ake tili ndi mmodzi amene angatipatse chikoka ndikutipatsa mphamvu. Mwayesu tili ndi chitsanzo changwiro cha mmene moyo wathu uyenera kukhalira, ndi mphamvu yangwiro imene tingakhale nayo imene tingayembekezere kukhala moyo wotero. Pamene tikukopeka kutero ndi chitsanzo ndi

zophunzitsa za Yesu, ndi pamene tikupatsidwa mphamvu ndi Iye za moyo wathu za chikhulupiriro, tiyenera kuganiziranso kuthekera kwathu kwakukopa kwa iwo amene atizungulira.

Paulo akuphunzitsa ku Aefeso kuti Yesu anadalitsa mpingo ndi mphatso zosiyanasiyana zimene zili zopindulitsa kuzolinga za ufumu wake. Alaliki anaikidwa pa mulingo omwewo wa atumwi, abusa, aphunzitsi (kapena aphunzitsi oti ndi abusa) ndi aneneri, ndipo Paulo akuti anthu amene ali ndi mphatsozi akwaniritse mayitanidwe amenewa pakupatsa mpingo zida zogwirira ntchito mu utumiki ndi kumanga thupi la Khristu.

Chingathe kukhala cholakwa kuyang'ana maudindo a utumiki a mu Aefeso 4 ndi kumangirira mophweketsa kuti akulozera ku anthu ena opatulika mmipingo yathu. Kalata ya Paulo ikuvumbulutsa china chake chabwino kwambiri. Mautumiki alipo chifukwa ndi opatulika ku mpingo, ndipo Mulungu ali pantchito kudzera mwa anthu wamba kutsimikiza kuti akukula kukhala okhwina ngati thupi limodzi. Timasamalira iwo amene ali mdera la mpingo pamenepo tikufikira ena amene ali kunja, aliyense ali ndi malo ogwira.

Tili ndi udindo wogwiritsa bwino ntchito mphatso zathu, izi zikutanthauza kuchita mwadala kuti mukhale a chikoka. Zikutanthauzanso kuti ndi kudzichepetsa ndi chiyero tawunikikira mmaphunziro ambuyo, titsogolere njira yotetezera kugwiritsa molakwika mphatso zimenezi zikhoza kubweretsa kugawanika kwa mpingo. Kunyada, kudzikuza, nsanje ndi kugwiritsa ntchito molakwa mphamvu zathu ndi chidule chobweretsa magawano.

Kambiranani: Kodi mumpingo mwanu amene amaoneka kuti ndi osisirika ndi ndani, ndi izi mmaganizo mwanu, ndi udindo wanji ndi ntchito yanji mu mpingo wanu zosisirika ndi anthu lero? Mwina kungakhale kukhala mbusa kapena wogwira ntchito ndi achinyamata, wotsogolera kupembedzera kapena mphunzitsi wa Buku Lopatulika. Kodi anthu amalakalaka kuchita umboni ndi kufalitsa, ndipo ngati sichoncho ndi chifukwa chiyani?

Pano pali njira zisanu zimene tikuyeserera kulimbikitsa ena – kaya timaganizira patokha kuti ndife alaliki kapena ayi – kugawa uthenga mokhulupira.

LENGEZANI UTHENGA WABWINO

Njira imodzi yabwino kwambiri yokopera anthu ndi kugawa uthenga wabwinondi kuchita choncho kawirikawiri misonkhano yathu. Njira ina ndi kuyitanira abale ndi alongo a chikhristu kubwera kuzochitika kumene tikukalalilkira (osangoti chifukwa cha thandizo lawo la pemphero, komanso kumangiririra chikhulupiriro chawo pamene akuona mphamvu yake ikugwira ntchito pamene anthu akukumana ndi Yesu kwa nthawi yoyamba), kapena kubwera nafe pamodzi kumene / pamene tikudziwa kuti tikhala ndi mwayi wolankhula za uthenga wabwino ndi munthu wina wake. Pamene tikugawa uthenga, pagulu kapena munthu payekha tingathe mosadukiza kutsimikiza kuti kufalitsa ndi mwayi ndi chimwemwe kwa okhulupirira onse.

KONZANI UMBONI

Thandizani anthu kuganiza za umboni wawo ndi mphamvu ya Mulungu pa moyo wawo kuyambira pamene anakumana naye mpaka pano. Kodi anachita bwanji poyamba kuyika chikhulupiriro chawo mwa iye, ndikuti wakhala akuchita chiyani mmoyo wawo tsopano? Mwadala konzekera umboni wanu ndi njira yayikulu yolimbikitsa ndi kupeleka mphamvu kwa ena za kufalitsa ndi ndiponso chochita cha kupembedza pamene tikuthokoza Mulungu pa zimene wachita mmoyo wathu.

TSOGOZANI KUNENA NTHANO ZABWINO

Mmisonkhano yathu ndi kulankhula kwathu nthawi zambiri kukhale kogawana nkhani zokhudza zochita zathu za kufalitsa. Kondwererani ndi kulimbikitsidwa pamene Mulungu wagwira ntchito kudzera mwa ife, ndi kusankha kuganizira mwabwino ndi mokonza za zinthu zimene tingathe kuphunzira mu zinthu zimene sizinayende bwino. Pamene anthu a mdera lanu akumva nkhani za mmene Mulungu akugwirira ntchito kudzera mwa anthu wamba monga ngati iwowo, adzakuza kulimba kwawo kuti Mulungu angathe kuwagwilitsa ntchito.

YESERANI LIMODZI
Zikhoza kuoneka zopanda pake ' kuyesera kufalitsa poyesera pa wina ndi mnzake, koma ndi njira yabwino kwambiri yokonzekera zokambirana zimene zingathandizire kuumba kulimba mtima kwa anathu. Sitingayembekezere munthu wina kungoyamba kuyendetsa galimoto pamseu wa onse opanda kuyesera kale kapena kuthandizidwa, chomwechonso tisayembekezere kuti anthu akachitira umboni popanda kuwapatsa mwayi wokula mukulimba mtima kudzera mukuyeserera ndi kuphunzira pamodzi.

PEREKANI MWAYI
Kudzera ku mpingo kwanu ndi magulu amaubwenzi ena, pangirani anthu ena mwayi wokhala nawo pakufalitsa. Konzani mwayi wapompo komanso wakunja kwa dziko lanu wa utumuki, itanilani anthu kukhala gawo la timu ya utumiki la zochitika zimene mukuyendetsa, kapena mutenge anzanu pang'ono kwa maola angapo kukalalikira mmisewu. Njira za mmene mungachitire izi ndi zochuluka kwabasi: khalani ndi maphunziro ena musanapite ndi kubwerenza mwachidule pamene mwabwerera.

Nthawi ikamapita anthu ayamba kukhala kwambiri ozolowera muzochitika izi za mwayi "wokhazikitsidwa" wa tsiku ndi tsiku ndipo kufalitsa kwawo kudzachoka kuchita izi kwa sabata imodzi yokhazikika ya utumiki kufika pochita izi ndi mwayi tsiku ndi tsiku.

Komabe pamene tikupitiliza kuchita izi, tiyeni tidzikhuthule kugwedeza ndi kuwathandiza abale ndi alongo mwa Khristu kulowa mukusefukira kwa chidziwitso chawo ngati ana otumikira a Mulungu.

ZOKAMBIRANA (MPHINDI 20)

Unikirani mafunso ndi / kapena zokamba za ena zotsatirazi:

1. Kodi zikutanthauza chiyani kumanga mpingo munjira imene paulo akufotokozera mu Aefeso?
2. Kodi timasunga bwanji kusiyana kwathu ndi dziko ngati otsatira Yesu, ndi mumpingo ngati alaliki a chikondi?
3. Kupatula njira zisanu izi tawunikira muphunziro ili, tingatakase ena bwanji kufalitsa?

KUCHITA ZIMENE MWAPHUNZIRO (MPHINDI 10)

Mwachiyembekezero mudzakhala ndi khumbo lokhalabe mugulumu kudutsa kumapeto kwa chaka chake choyamba ndi kupitiliza ulendo wake pamodzi ndi ena kukula ngati alaliki mchaka chachiwirii koma ndi maganizo otakasa mpingo ku kufalitsa, tsopano itha kukhala nthawi yabwino yoganizira kuti zidzawoneka bwanji kuyendetsa gulu lanu la Msuntho pamodzi ndi lino.

Kuchulukitsa ndi Mfundo yacholinga ya gulu la Msuntho chifukwa chikhale chokhumba chathu ngati alaliki kuwalimbikitsa ena mukufalitsa kwawo. Choncho tengani nthawi yolemba ndandanda wa anthu amene angakhale osangalatsidwa wolondola ulendo womwewo mwakhala nawo ndipo muyambe kufikira ena mmasabata akubwerawa. Gwiritsani ntchito ukadaulo wanu kuchokera ku gulu lino ndi mabuku a Msuntho kukuthandizani kukonza ndi kusonkhetsa gulu lanulanu.

PEMPHERO

Khalani ndi nthawi yopempherera mpingo wanu, kuti onse amkatimo akhale wokhulupirika ku kuyitanira uthenga wabwino mmiyoyo yawo. Pempherani mwayi wolimbikitsa ena, ndi kupemphererana wina ndi mnzake mu gulu osangoti kulalikira uthenga wabwino wokha kudziko losowa, koma kutakasa ndi kupatsa mphamvu otsatira ena a Yesu kuchita chimodzimodzi.

UDINDO WA KHALIDWE LANU (MPHINDI 15)

Kodi munasowako mtendere ndi kukwiyira mpingo kapena anthu a mkatimo chifukwa cha chimene mukuwona ngati kusowa chochitika cha kufalitsa kapena ngakhalenso mtima wa anthu otayika? Ndi zomvetsetseka kumva choncho koma m'daniyo angatembenuze mosavuta zakumva zimenezi kukhala chonyozetsa, chapamwamba kapena kusakhululuka. Chezani zokhudza maganizo awa ngati gulu lonse ndi kupemphera awiriawiri kuti mitima ifewetsedwere abale ndi alongo athu, ndi nzeru zammene tingalimbikitsire ena. Kukhala ochitira umboni okhulupirika.

Malizani form ya udindo wa khalidwe lathu, gawanani awiriawiri kapena magulu ang'ono ndi kupemphererana wina ndi nzake.

OSAIWALA...

Ngati mukufuna kuyamba gulu la Advance lanu mungathe kutilembera ku advancegroup.org ndipo ngati mtsogoleri wagulu mukhale wodziwitsidwa za zimene zikuchitika za mabuku atsopano wothandizira gulu lanu, nkhani zochokera mmaiko ena zolimbikitsa ndi chidziwitso chakuti mukupemphereredwa pafupi pafupi.

POLEMBA

PHUNZIRO 12: M'BINDIKIRO

Mapeto a zonse a za chaka cha gulu la Msuntho ndi kukhala ndi nthawi ya m'bindikiro. Mmene mungaganizire kachitidwe kake ka izi zili ndi inu, koma pano mupeza maganizo chabe a mmene mungagwiritsire ntchito nthawi yanu mogwilizana ndi Mfundo za gulu la misonkhano ya Msuntho ndi kubweretsa chaka chanu choyamba kumapeto kwake ndi cholinga.

MMENE MUNGAYENDETSERE M'BINDIKIRO WA GULU LA MSUNTHO

Maganizo a m'bindikiro ndi kuchoka kaye pamalo anu a nthawi zonse ndi kupatula nthawi yayitalipo kuposera maphunziro a magulu anu a nthawi zonse. Ngati mungapatule mmawa, masana kapena madzulo chitani zimenezi nthawi iyiyi, koma ngati kungatheke, m'bindikiro wa tsiku lonse ndwopindulitsa kwambiri.

Pano pali maganizo ena a zimene mungachite munthawi yanu ya m'bindikiro.

NDIME YOFUNIKA

Ndime yotsatilayi kuchokera kwaAkolose idzagwira bwino ntchito monga mfungulo wamalembo wa nthawi yanu pamodzi ngati mukuyang'ana cholinga chenicheni cha nthawi ya m'bindikiro.he following passage from Colossians will work well as a key scripture for your time together if you are looking for a specifi focus during the retreat:

> 'Chitani khama m'kupemphera, nimudikire momwemonso ndi chiyamiko; ndi kutipempherera ifenso pomwepo, kuti Mulungu atitsegulire ife pakhomo pa mau, kuti tilankhule chinsinsi cha Khristu; chimenenso ndikhalira m'ndende, kuti ndichionetse ichi monga ndiyenera kulankhula. Muyendere munzeru ndi iwo akunja, kuchita machawi nthawi ingatayike. Mau anu akhale mchisomo okoleretsa, kuti mukadziwe inu mayankhidwe anu a kwayense akatani.'
>
> **AKOLOSE 4:2–6**

Mkati mwa ndime yayifupi imeneyi muli zinthu khumi ndi ziwiri zimene Paulo akupeleka zimene zingathe kuwunikiridwa ndi kutsimikizira ku kufalitsa uthenga.

1. Dzikhuthureni (dzikhuthureni nokha ku pemphero)
2. Limbikitsani chiyanjano cha uzimu (mutipempherererenso ife)
3. Dalirani pa Mulungu (Mulungu angatsegule chitseko)
4. Dziperekeni kukulalika (tingalalikire za zozizwa za Khristu)
5. Khumbani kumveka bwino (kuti ndikathe kulalika momveka bwino)
6. Landirani nsembe yauthenga wabwino (chimene chinandiika mu nsinga)
7. Dalirani pa nzeru zakumwamba (khalani a nzeru)
8. Gwiritsani ntchito mwayi (mugwiritse ntchito kwambiri mwayi uliwonse)
9. Lankhulani ndi kumvera (kukambirana)

10. Khalani a chisomo ndi odzichepetsa (nthawi zonse odzala ndi chisomo)

11. Khalani osiyana (okometsedwa ndi mchere).

12. Khalani okonzeka (kuti mudziwe mmene mungayankhire aliyense)

Kaya muwelenga ngati gulu kapena panokha (onani mmunsimu), mmene mungatsitsire Mfundo zimenezi, ndi mmene mungazikambirane pamodzi zili mmanja mwanu malingana ndi mmene mukuyendetsera nthawi yanu ya m'bindikiro koma musunge ndimeyi ndi mfundozi mmaganizo anu pamene mukuyang'ana zochitka za mmunsizi.

MAWU

Mfundo yacholinga ya gulu la Msuntho ndi kuthandizana wina ndi Mnzake kukula ngati alaliki amene ndi odzipereka ku mawu a Mulungu. Nthawi ya m'bindikiro iyi ikhale nthawi ya mwayi wakulu yozama mu mawu.

KUPHUNZIRA NDI KUWERENGA BUKHU LOPATULIKA PA NOKHA

Nthawi yotalikitsidwa yowelenga mawu a mulungu sinakhalepo nthawi yongotaya. Kukhala ndi nthawi yowelenga bukhu lonse la uthenga wabwino la Marko kapena limodzi la makalata a Chipangano Chatsopano pa kukhala kwapakamodzi ndi njira yaikulu yokhalira ndi maganizo odzala ndizimene zili mubukhumo. Ngati ndi bukhu laifupi bwanji osangoliwerenga kambiri, kupemphera ndi kulingalira pakati pa kuwerenga, kupanga notsi, ndipo kenako ndi kubwerezanso. Mukhonza nonse kusankha kuwerenga zomwezo kapena kukhala ndi maganizo angapo osiyana amene anthu angathe kugawana zokhudza nthawi yawo ya kuwerenga ndi kulingalira.

KUPHUNZIRA NDI KUWERENGA BUKHU LOPATULIKA PA GULU

Pali njira zingapo za mmene mungatsogolere kuphunzira ndi kuwerenga Buku Lopatulika pamodzi mnthawi ya m'bindikiro, mwina mwake mungathe kufuna kubwereranso ku ndime yanu yaikulu imene mwaunikira pamaphunziro a gulu la Msuntho. Njira inanso mwina mungamve kutsogozedwa ku ndime kapena mutu wina umene udzayika kayambidwe ka m'bindikiro wanu. Mwa nthawi zonse, tsimikizani kusunga izi molingana ndi kulitsana wina ndi mzake monga alaliki.

MAPHUNZIRO OWONJEZERA NDI MABUKU KAPENA ZOWERENGA ZOWONJEZERA ZA MSUNTHO

Limodzi mwa phunziro lowonjezera la mlozo uno ndi kuyendetsa maphunziro a gulu la Msuntho ngat gawo la m'bindikiro wanu. Mungathenso kukhala ndi maganizo anu a mmene mungayendetsere phunziro lanu munjira zofanana ndi zimene mwakhala mukugwiritsa ntchito.

Momwenso mungathe kufuna kuyang'ananso pa One Thing Blog pa Advance Website (advancegroups.org) pamene pamapelekedwa alaliki osiyanasiyana akugawana za chinthu chimodzi chimene amafuna akadadziwa asanayambe kulalikira za uthenga wabwino. Izi za zing'onozing'ono zimapereka kukambirana kwabwino kwa oyamba.

PEMPHERO

Sungani nthawi yambiri mu nthawi iyi ya m'bindikiro. Konzani dongosolo labwino la nthawi ya pemphero ndi cholinga chenecheni, komanso nthawi ya kupemphera kudzera mmalembo ndi pemphero lapompopompo. Chili chonse chimene mungachite nthawi yopemphera mu m'bindikiro, zolinga zitatu izi zotsatirazi ndi zoyenerezedwa.

KUPEMPHERERANA WINA NDI MNZAKE

Onetsetsani kuti kupemphererana wina ndi mzake ndi cholinga choyambirira cha nthawi yanu pamodzi.

Funsani anthu agawane dera limodzi limene akuyamika Mulungu ndi dera limodzi limene akufuna kuperekedwa kudzera mu kubowoleza. Limbikitsani anthu kukhala a chindunji ndi owona pa zopempha zawo, ndipo musathamangire kwa wina koma mukhuthule nthawi yeniyeni ya wina ndi mnzake. Onetsetsani kuti nthawi iyi mukusunga mawu ndi zilimbikitso zimene zimabwera.

KUPEMPHERERA MPINGO WA KUMUDZI NDI DZIKO LONSE

Khalani ndi nthawi yopempherera kufala kwa uthenga wabwino kudera kwanu ndi dziko lonse. Ngati pali zinthu zapadera zimene zili mumtima mwathu zokhudza dera lathu kapena dziko lonse ndiye kuti muzipempherere. Pempherani munthu payekha, mipingo, mautumiki, atumiki ogwirira ntchito kunja kwa dera lawo, ndi zinthu zina zochokera nkhani zapa wailesi ndi kanema.

KUPEMPHERERA ZA ULENDO WA MSUNTHO

Thokozani Mulungu chifukwa cha ulendo umene mwakhala mgulu lino, kuwunikiranso zakakhalidwe ka munthu mwini ndi nkhani za zopindula ndi chipulumutso. Pemphani Ambuye kupitiliza kugwira ntchito mwa inu imene wayamba kale, ndi kuti dziko lisandulike kukhala chifanizo chake cha ulemerero wake wongokulirabe (mutha kupemphera kugwiritsa ntchito 2 Akorinto 3: 17-18)

KUPEMBEDZA

Nthawi yokhala mmawu a Mulungu, pemphero ndi chiyanjano zonsezi ndi gawo lakupembedza. koma khalani ndi nthawi yapadera yodzikhuthula mukupembedza pa gulu nonse pamodzi kaya kudzera mkuimba kaya mu zinthu zongopeka.

NYIMBO YOPEMBEDZERA

Ngati muli ndi munthu waluso la mayimbidwe, mumuyitane kuti atsogolere nthawi ya nyimbo za chipembedzo. Ngakhalenso pamasamba a makina a mchezo pangapezeke nyimbo yakumtima kwanu ndi a kanema ambiri a chipembedzo, amene ambiri mwa iwo ndi aulere.

NKHANI NDI MATAMANDO

Khalani ndi nthawi yogawana nkhani za mmene Mulungu wagwirira ntchito mmoyo wanu chaka chino. Nkhani za kukula, kubowoleza, mwayi wofalitsira uthenga ndi zipatso zake. Ikatha nkhani iliyonse khalani ndi nthawi yotamanda Mulungu kudzera mmapemphero, nyimbo kapena njira ina ili yonse imene imagwira bwino ntchito ku gulu lanu pamene mukufunitsitsa kuthhokoza Mulungu pa chimene iye ali ndi chimene wachita/akuchita.

KUMUKA

Njira ina yabwino imene mungagawane yakuchita mwagulu ingakhale kutumizana wina ndi mnzake pamaso pa Mulungu ku ntchito yofalitsa imene anakuyitanirani inu ndi kukupatsani mphamvu . Kumapeto kwa chaka ichi choyamba cha gulu la Msuntho kudzalimbikitsa ndi kutsimikiza za kukwera kopambana kumeneko, choncho thokozani Mulungu pa chimenechi ndi kupemphererana wina ndi mnzake pamene mukuyang'ananso za kupitanso ndi uthenga wabwino ku dziko lapansi ku ulemerero wa Mulungu.

CHIYANJANO

Pamene tikkusonk;hana pamodzi timakula mmaubwezi ndikudalirana wina ndi mnzake. Chiyanjano cha gulu la Msuntho mwachiyembekezo chakhala mdalitso kwa munthu aliyense , ndipo pa m'bindikiro mungathe kupitiriza kudzipereka kwanu kwa wina ndi nzake kuwonerana khalidwe ndi chimwemwe cha kukhalira pamodzi.

UDINDO WA KHALIDWE LANU

Kukhala a dindo a khalidwe lanu lakhala gawo la cholinga chachikulu cha phunziro lili lonse, ndipo gawo lino laphunziro lomaliza la chaka, bwerezaninso kudzipereka ku ndondomeko yomweyo kutsimikiza kuti mukukhala moyo wachiyero ndi wodzichepetsa.

KUSALA / PHWANDO

Mungathe kufuna kupereka nthawi ya kusala ngati gawo lanu la m'bindikiro, kapena kutenga nthawi yanu pa chakudya pamodzi pamene mungasonkhane bwino ndi kuwapanga malo a zokambirana. Palibe njira yabwino kapena yoyipa yopangira izi- chofunukira kwambiri ndi chakuti zikuthandizani kukwaniritsa zolinga zanu zanthawi ya m'bindikiro. e goals of your retreat time.

ZOCHITA

Mungathe kukonza chochita nonse pamodzi – mwa chitsanzo, ngati mukukumana ku phiri kwina kwake, pitani mukayende limodzi ndi

kupanga zochita zina za kudzipereka za mmwambazo nthawi ino. Ngati mukupapangira munzinda, mukhoza kukayenda kumene kuli malo ogulitsira za luso la manja la zojambula ndi kuchita chimodzimodzi , kugwiritsa nthito zina za zojambulazo ngati zokufulumizitsani kuti mulingalire ndi kudzikhuthula.

Momwenso mukhoza kuchita chinthu china chongosangalatsa chabe – kuchita zinthu ngati timu, masewero, kusankha za msangulutso ndi zinz zambiri. Kaya ndi chiyanjano cholimbikitsa kudzikhuthula kapena chiyanjano chongofuna mukondwerere kukhala pamodzi kwanu ndi kukula pa ubale wanu wina ndi mnzake, khazikitsani nthawi yopambana ya wina ndi mnzake.

NDONDOMEKO ZINA

Choyamba cha Msuntho chatha. Musanatsekere chakachi (ndi m'bindikiro) onetsetsani kuyang'ana ndondomeko zotsatirazi za gulu lino ndi magulu ena amene mukhazikitse kuchokera pa linoli.

GULU LINO

Pangani nkhani yakuti anthu agawane za mmene awonera mmoyo mwawo zochitika za mgulu la Msuntho. Gawani mobwereza za mmene nonse mwakulira ndi kutukuka, ndipo muganizire chinthu chachikulu chimene mwaphunzira mchakachi. Limbikitsanani wina ndi mnzake za zinthu izi.

Pempherani ndi kuthokoza Mulungu chifukwa cha chaka choyamba cha cha gulu la Msuntho ndi kuperekeza tsogolo lake kwa Ambuye.

Tengani mwayi uwu ngati opangira masiku oyambirira a chaka chachiwiri limodzi.

MAGULU ATSOPANO

Zidzakhalanso za phindu kutenga za zimene zachitika ndi magulu atsopano amene ayambika mu phunziro lathali. Onani mmene anthu akuchitira ndi kuthekera kwakuti atha kuyamba lawo gulu lina ndi kuti ngati pali magulu akuti akuyamba , muwapempherere.

Komabe mmene mungayambire nthawi yanu ya m'bindikiro, sungani cholinga chachikulu cha Msuntho mmalingaliro anu, unikiraninso ulendo mwayenda ngati gulu pamodzi, ndi kupempherera za zimene zikubwera mtsogolo.

POLEMBA

ZOWONJEZERA:
ZIPHUNZITSO ZA UTHENGA WABWINO

Simunapangidwe mwa ngozi. Munalengedwa ndi ndi ndi mwachifaniziro cha Mulungu wangwiro ndi wachikondi (Tate, Mzimu,Mwana) amene ndi gwero ndi wosunga moyo (Genesis 1).

Tonse tinakana Mulungu (tinachimwa)poyenda njira zathu, mmalo mokhala moyo womvera mlengi wathu. Ichi ndi chifukwa chake dziko lapansi ndi losweka ndi lodzadza ndi masautso. Kusalungama uku kumamvetsa chisoni Mulungu, amene salekerera tchimo pongolisiya kapena kusalabadira ilo, koma amene molungama amalanga amene achimwa (Aroma 3:23).

Tilibe mphamvu yobwezera zinthu mokhoza pamene tawukira Mulungu, titapanga ntchito yogalukira mfumu ya dziko lonse. Kukana Mulungu ndi kukana moyo. Timatsala ndi imfa ya muyaya, chipatso chachibadwa cha kukana moyo ndi chilango cha mulungu (chilungamo cha umulungu) pophwanya mulingo wake wakukhala wolungama (Aroma 6:23).

Koma Mulungu amakhumba kuti aliyense asadziwe imfa, pakuti Iyeyo ndi chikondi ndipo amafuna ubale wamuyaya ndi ife, ana ake okondedwa kwambiri. Mwa chisomo cha Mulungu anayika mmalo utumiki wopulumutsa ife (1 Timoteo 2:4-6)

Mulungu anatumiza mwana wake, Yesu Khristu, mudziko lapansi monga munthu, kudzakhala moyo wangwiro wamunthu amene sanakaneko Atate. Yesu anaphedwa pa mtanda, kulowa mmalo mwathu ndi kusankha kudzitengera iye mwini imfa imene inatiyenera titakana Mulungu wathu (Yohane 3;16: Aroma 3;23-25)

Atatha masiku atatu, Yesu anauka kwa akufa, kusonyeza kuti tembereereo la imfa linadulidwa. Tsopano moyo ndi otheka kudzera mukukhuliupirira mwa yesu Khristu ndi kupempha chikhululukiro cha machismo (Miyambo 28:3; Aefeso 2:1-10; 1 Yohane 1:7-9)

Imfa ndi kuuka kwa Yesu kunakwaniritsa chiyanjano, chiwombolo, chitonthonzo(chamsembe) ndi kugonjetsa choipa. Tchimo lathu linalipiridwa ndi Yesu ndipo chilungamo chake chinabwera kwa ife. Chofunikira chokha kumbali yathu mmalonda awa kuti akakhale ndi mphamvu ndi chakuti tikhulupirire mwa Yesu ngati Ambuye (chikhulupiriro), ndi kukhulupirira kuti Mulungu anamuwukitsa kuchoka kwa akufa. Ndife opulumutsidwa ndi chikhulupiriro chokha basi (Mateyu 20:28; Aroma 10:9; 2 Akorinto 5: 5:18-21; Yohane 12:31; Akolose 2:15).

Yesu anakwera kumwamba, kumene akulamulira kudzanja lamanja la Atate, koma anatumizira okhulupirira mphatso ya Mzimu Woyera kutipatsa mphamvu yokhala momvera mu chidzalo chamoyo, ndi kutithandiza ife kugawa nkhani yake yabwino ndi dziko lapansi. Timakhala olengedwa atsopano-ophunzira-osandulika ndi ntchito ya Mzimu mmiyoyo yathu,chimenen chimatitsogoza kubala zipatso. Timagwira ntchito ngati akazembe a Mulungu mdziko lapansi, kuyimirira ufumu wa mtendere, kutumikira ngati mboni za choonadi cha mbiri ya Yesu mmawu ndi mzochita (Mika 6;8; 2 akorinto 5:11-21; Agalatiya 5;22-23)

Tsiku lina, Yesu adzabwerera kudaaweruza amoyo ndi akufa. Ufumu wa Mulungu wangwiro udzabwezeretsedwa ndipo moyo wamuyaya ndi Atate athu achikondi ukudikira iwo amene adzadalira mwa Yesu ngati Ambuye. Imfa ya muyaya (gahena) ikudikira iwo amene sanatero. Nkhani yabwino ndi yakuti palibe akufunikira kukapsya kwamuyaya , onse angathe kudziwa moyo wosatha ndi chimwemwe cha muubale ndi Mulungu, kudzera mu chikhulupiririro mwa Yesu Khristu (1 Akorinto 15; Chibvumbulutso 21:1-8; 22:1-5)

ZOWONJEZERA:
KUSIMBA UTHENGA WABWINO

Pasanalengedwe zonse, Mulungu, analipo muubale wangwiro ndi Iye mwini, Atate, Mzimu ndi Mwana. Mulungu analenga dziko lapansi ndipo linali labwino, ndipo anagawa ubale wapaderadera ndi mtundu wa anthu. Tinalengedwera moyo wangwiro ndi iye, mfumu ya dziko lapansi, ndi moyo pawokha! Koma Mulungu sanakakamize anthu kumukonda Iye, anatilola kusankha tokha. Ndi ufulu uwu wosankha anthu anasankha njira yawo, kukana Mulungu.

Kukhala mfumu ya dziko lonse lapansi ndi mlandu wogalukira wopanda ofanana nawo, ndi kuwukira moyo okha. Imfa, masautso ndi kumva kupweteka zinalowa mdzik0. anthu anadzipatsa tsoka okha podzipatula kuchoka kwa Atate mopanda kubwerera. Mulungu sakadalekerera kuwukira , pakuti sipanakhala chilungamo pa chimenecho. Mulungu wachilungamo ndi wolondola amayitanitsa chilango kuti chiperekedwe ku machimo amene achitidwa. Chilango chowukira moyo ndi imfa

Koma Mulungu anakonda dziko lonse lapansi kotero kuti anapanga dongosolo lopulumutsira anthu kuwachotsa ku imfa - kupanga chotheka kuti ife tidziwe chidzalo cha moyo ndi chikondi chosatha. Mulungu anatumiza mwana wake Yesu mdziko kudzakhala wa umunthu wangwiro, moyo umene sunawukirepo ndi kupezeka wolakwa pa tchimo lili lonse lochimwira Mulungu.

Yesu mwakufuna kwake anafa pa mtanda kutitengera ife chilango cha imfa chimene chinayenera anthu chifukwa cha kuwukira kwawo ndipo pochita choncho anakhala mlowa mmalo mwathu. Masiku atatu atatha anakhalanso ndi moyo, chifukwa Iyeyo ndi Mulungu ndipo imfa sikanatha kumusunga Iye. Munthawi iyi kunakakhala kotheka kwa mtundu wa anthu osati kungolandira kokha chikhululukiro cha machimo chowukira Mulungu, komanso kugawana moyo umene Yesu anapanga kukhala wotheka. Temberero la imfa linaphwanyidwa.

Chimene tikufunukira kuchita ndi kukhulupirira kuti Yesu ndi amene akunena kuti ndi Iye –mpulumutsi wadziko wopachikidwa ndi wowuka, mfumu ya dziko lonse lapansi – ndi kusankha kumupanga Iye kukhala Mbuye wa miyoyo yathu. Pali chipulumutso ndi moyo kwa onse okhulupirira Iye, ndi kupereka mphamvu ya Mzimu Woyera zotheketsa ife kukhala mtundu wa miyoyo imene imawonetsa chifaniziro cha Mulungu kotero kuti tonse tingathe kudziwa moyo weniweni. Poyika chikhulupiriro chathu mwa Yesu, timafa kumoyo wathu wakale ndi kukhala wabadwanso mmoyo watsopano. Tsiku limodzi Yesu adzabwera ndipo ufumu wake wangwiro udzabwezeretsedwa. Onse amene anamukhulupirira adzakhala muyaya mkati mwa ufumu wake, ndiye choncho tinayitanidwa ndi kumemedwa kugawa chikondi cha Mulungu cha dziko lonse lapansi kotero kuti tingathe kudziwa chiyembekezo chamuyaya cha lero ndi mpaka kalekale.

ZOWONJEZERA: CHITSANZO CHA KULANKHULA UTHENGA WABWINO KWA ACHINYAMATA

CHOYAMBA: INU SINDINU TSOKA!

Anthu ambiri amayenda akuganiza kuti anapangidwa mwangozi, kuti ali padziko pano chifukwa anangopezeka kuti ndi anthu opanda poyambira, ndiye kenako tinangopezeka tafika patatha zaka miyandamiyanda. Koma izi zilibe phindu, komanso sizipereka chiyembekezo cha chimene moyo umatanthawuza.

Buku Lopatulika limatiwuza kuti Mulungu ndi wachikhalire ndipo analenga dziko lapansi kuchokera kukhumbo logawa chikondi chake kwa chilengedwe chake – anthu. Choncho siyinu ngozi – ndinu wolengedwa a Mulungu, ndinuwokondedwa ndipo muli ndi cholinga. Mulungu anaganiza kuti dziko lapansi ndi labwino kwa inuyo, ndipo ndi chifukwa chake muli pano.

CHACHIWIRI: MWAPHONYA MFUNDO

Vuto ndi ili, pamene anthu sakudziwa kuti Mulungu anawalenga iwo ndi kuti amawakonda – amaphonyana ndi cholinga chonse cha moyo! Kudziwa Mulungu ndi kukhala ndi moyo monga mmene tiyenera kukhalira – muwubwenzi ndi mlengi wathu, muubale ndi Mulungu wokonda, wokoma mtima, wachifundo, wachisomo, wodekha ndi wanzeru. Buku Lopatulika limakamba za Mulungu ngati Tate wangwiro, amene amafunira ana ake zinthu zabwino – amene ndi inuyo ndi ine! Koma Buku Lopatulika limakambanso za ife kukhala ana ogawukira, tinathawa kuchoka ku chikondi cha Atate wathu.

Kusadziwa Mulungu kuli ngati kuthamanga pabwalo la masewera a mpira wa miyendo wa chikho cha dziko lonse lapansi koma osalabadira zochinya chigoli chili chonse ... palibe angathe kuchinya chigoli,palibe angathe kupeza mphotho – zingakhale zopanda mfundo, anthu basi kungothamangathamanga mpaka kumapeto a masewera.

CHACHITATU: MUNGAATHE KUDZIWA CHIDZALO CHA MOYO

Buku Lopatulika limatiwuza kuti ngati tikukana moyo wa mulungu mwa ife, zinthu zoyipa zidzachitika mu dziko lapansi chifukwa tikuganiza za mmene tingakhalire moyo wabwino kuposera za moyo analenga ife. Kuchita zinthu nkwathu mopererwera kudzachititsa kukhala mu dziko loperewra ungwiro. Buku Lopatulika limatchula chimenechi kuti tchimo – kutanthawuza kuti kuphonya chizindikiro cha chimene tinalengedwera. Njira ina yoganizira za tchimo ndi kudzikuza.

Timasankha njira yathu mmalo mwanjira ya Mulungu. Timati 'haaa Mulungu, ndine wabwino kuposera inu; sindifuna Inu; Ndingathe kukhala Mulungu wabwino kuposa inu. ' tingofunika kutsegula kanema wathu wa nkhani kuti tiwone mmene dziko limene tikukhala linasokonezekera, ndipo izi ndi zotsatira za anthu za kuphonyana ndo mfundo, kukhala kwa pawokha, kapena pa china chili chonse kupatula Atate Mulungu wachikondi amene ndi gwero la moyo. Masawutso onse, kusalungama konse,ndi chisokonezo timachiwona mu dziko lapansi zimakhalapo chifukwa timaganiza kuti

ndife abwino kuposera Mulungu – tinamukana Iye.

Kukana uku kunabweretsa chotchinga pakati pa ife ndi iye – anthu opnanda ungwiro ndi wowukira – ndi Mulungu wangwiro wa chilengedwe chonse. Pamene tikana Mulungu pamakhala zotsatira zake za zochita zathu. Ngati mutsutsana ndi aphunzitsi anu ndi kuphwanya malamulo a sukulu mukhoza kumangidwa, zotsatira zoyipa zakupanga chisankho choyipa. Koma ngati mulakwira mulungu zotsatira zake sichilango chochepa chongokukonzani khalidwe , zotsatira zimenezi ndi chibadwa chak chenicheni chimene chimalondolazochita zathu. Pokana Mulungu timakana moyo ndipo ngati timakana moyo mwatsala ndi chiyani? Imfa

Koma Mulungu sakufuna kuti mufe, anakulengani kukhala ndi moyo wa chidzalo chonse mu ubale ndi Iye. Buku Lopatulika limatiwuza kuti Mulungu anachita china chake kukonza vuto limene tinalipanga tokha, anatitumizira mwana wake Yesu mu dziko – Mulungu mwa munthu – kudzakhala moyo wa umunthu wangwiro umatisonyezera ife mmene tiyenera kukhalira, ndi kutenga zotsatira za kukana kwathu pa Iye mwini.

Yesu anaphedwa pa mtanda kutitengera imfa imene tinasankha titakana Mulungu, kutitengera ndende yathu. Pano pali nkhani yodabwitsa , patatha masiku atatu anakhalanso ndi moyo!

Anthu akhoza kunena kuti “ndinu wa misala munthu angabwerere bwanji ku moyo kuchokera kwa akufa?” Koma kumbukirani , Yesu ndi Mulungu ndipo Mulungu ndi moyo – imfa siyikanamusunga! Buku Lopatulika limanena kuti ngati tinena kuti pepeni kwa Mulungu chifukwa tinathawa kuchoka pa chikondi chake ndi kukhulupirira Yesu ngati Ambuye – kutanthawuza munthu wangwiro amene tinalengedwera kuti tikhale choncho mmalo mwakusalungama ndi chisokonezo chakukhala mmoyo watokha – tingathe kusuntha kuchoka ku imfa imene tidasankha kulowa mmoyo wa ubale ndi Yesu, lero ndi mpaka muyaya kumwamba: ufumu wangwiro wa Mulungu.

(Nkhani ya mwana wolowerera ingakambidwe ngati chitsanzo cha chili chonse cha chonenedwa mpaka pa mfundo iyi, za kuthawa kuchoka kwabambo ake omukonda, kuthera mu chisokonezo, ndi pobwerera kwawo atazindikira kuti tili ndi kulandiridwa kwabwino kuposera kumene timayembekeza. Ndife olandiridwanso monga ana amuna ndi akazi okhala ndi madalitso onse ndi zabwino zotsatira)

CHACHINAYI: KODI ALI PA MPANDO WOTENTHA NDI NDANI MMOYO MWANU?

Kodi muli mpando wokondedwa kwambiri mnyumba mwanu? Mpando umene mumakwiya nawo munthu wina akakhalapo kupeza malo abwino kwambiri kuti athe kuwonera bwino TV? Miyoyo yathu ili ndi mipando yotentha –mpando wa chifumu umene timalamulira ndi kuchitira ufumu pakupezeka kwathu. Sitilola wina aliyense kukhala pa mpando wa chifumu umenewo, kulamulira moyo wathu. Timanena kwa Mulungu , Haaa Mulungu , simungakhale pa mpando wotentha wanga, ndikufuna ndilamulire!

Koma Mulungu amatikonda kwambiri kwakuti amafuna ife tidziwe moyo wowonadi umene anatilengera,kutithandiza ife, kutitsogolera, kukhala pamene tiyenera kukhala, mpando wachifumu mkati mwa mtima wathu. Kumuyamika Mulungu pamalo ake oyenera kutanthawuza kuti tingathe kukhala mowona modzadza ndi chikondi chake, kuti tingathe kukhala mowona

Ambiri mwa ife ndi ozunguzika ndi kuti za moyo ndi chiyani. Enafe timalimbana ndi kutaya mtima, kudzipweteka, uchimadyo, kumvetsetsa kuti ndife ndani? Ena sakondwera ndi zimene amadziwona akayang’ana pa kalilole. Ena mwa inu munazama mukusakondwa ndi kupysinjika. Ena mwa inu mukumva kukoma mu chili chonse cha mmoyo wanu komabe pali china chake chimene chikusowa kotero kuti simungakwanitse ngakhale kuyika chala chanu...

(umboni pano ukhoza kugwiritsidwa ntchito kuti mulumikizitse maganizo amene mukupereka ndi zinthu zenizeni zimene za zinakuchitikirani)

Mulungu ali ndi mayankho a zonse zochitika, akuti “Mukumva choncho chifukwa munalibe moyo weniweni mumangomva chithunzithunzi cha moyo,kungokhala basi. Onse amene ali ndi mpweya mmapapo mwawo amangokhala chabe koma amathera mu imfa, munalengedwa kuti mukhale ndi moyo ndipo umapezeka mwa Mwana wanga Yesu ndi kukhala ndi moyo mwa Iye.

Osaphonya mfundo ya moyo. Tembenukirani kwa Mulungu, nenani pepani pomukana Iye ndipo adzakukhululukirani. Ikani chikhulupiriro chanu mwa Iye ngati Ambuye ndipo adzakusonyezani kuti inuyo ndinu ndani weniweni. Adzakupatsani moyo wochuluka, moyo weniweni ndipo simudzawona imfa. Pamene mudzapuma mpweya wanu womaliza mmoyo uno mudzakhala a moyo wambiri kuposera omwe munakhala muyaya. Kutsimikiza kuti moyo uno udzakhalabe ndi zophunthwitsa, sikuti vuto lili lonse la mdziko lapansi lidzatha pompopompo pamene mwatsatira Yesu – ndipo mukhoza kuwona zophunthwitsa zina zatsopano zikubwera chifukwa chakuti mukulondola Iye – koma Mulungu adzakuthandizani. Adzakupatsani Mzimu Woyera kukuthandizani kukhala moyo umenne ali nawo wa inu mdziko lovuta. Adzakubweretsani ku mpingo wake, kumene ngakhale musali a ngwiro, mubanja lake lapansi pano - lokonzedwa kukuthandizani inu kumudziwa Iye kwambiri – pitirizani kuyenda ngakhale pamene moyo uli wovuta, ndi kuvumbulutsa chikondi chake ndi chisamaliro cha dziko lapansi. Simudzakhalanso chimodzimodzi.

Sinu ngozi, mumakondedwa mopanda choyerekezera ndi Mulungu wangwiro. Koma Mulungu sadzakakamiza inu kuti mumukhulipirire, chikondi chenicheni chimakhala chisankho, mumadzisankhira nokha. Mungathe kutembenukira kwa Mulungu lero, ndi kudziwa moyo weniweeni wa ubale ndi Iye.

Kodi mukhoza kusankha chiyani?

Mafunso:

Kodi chabwino ndi chiyani pa phunziro ili?

Kodi chilipo china chikusowa?

Kodi chifukwa chiyani chikhoza kuganiziridwa ngati ‘chilankhulidwe cha achinyamata’?

Kodi mungatentengere bwanji zolankhula izi ku gulu lina (e.g. mkumano waophunzira ku sukulu, gulu la amayi amene ali ndi makanda,nkhomaliro ya atsogoleri a za malonda, gulu la anthu opuma pa ntchito?

NJIRA ZA UTHENGA WABWINO

NDINE NDANI?
(ADVANCEGROUPS.ORG)

YESU PA CHITSEKO
(JESUSATTHEDOOR.COM)

ZINGERENGERE ZITATU
(ZITSANZO ZOSIYANASIYANA ZA YOUTUBE)

MFUNDO ZINAYI
(THE4POINTS.COM)

NJIRA ZIWIRI ZOKHALIRA NDI MOYO
(TWOWAYSTOLIVE.COM)

3,2,1: NKHANI ZA MULUNGU, DZIKO LAPANSI NDI INU
(THREE-TWO-ONE.ORG)

BUKHU LOPANDA MAWU
(LETTHELITTLECHILDRENCOME.COM)

MAFUNSO A KUKHALA ADINDO A MOYO WANU

KIYI

✓ Zabwino
— Pakatikati
✗ Zoipa

‘Mundisanthule, Mulungu, nimudziwe mtima wanga.’ (Masalimo 139:23)

Kulolerana wina ndi mnzake (Aroma 15:7).
Kuvomereza zolakwa zanu wina ndi mnzake (Yakobo 5:16).
Kulimbikitsana wina ndi mnzake ndi kumangirirana wina ndi mnzake (1 Atesolinika 5:11).

‘Khalani moyo wa chikhalidwe cha Mulungu. Khalani moyo wokonda ndi wachisomo kwa ena monga Atate achitira kwa inu.’ (Mateyu 5:48).

Kodi masomphenya a moyo wanga akuoneka bwanji?

Kodi masomphenya a moyo wanga ali bwanji mu ntchito imene ndikugwira?

Kodi ndikusangalala ndi zimene ndi zochita zanga?

Kodi ndikumva chisangalalo cha Mulungu mu zimene ndikuchita?

Moyo wanga umakhala okhudzika bwanji?

Kodi ndi kusinkhasinkha ubale wanga ndi Yesu?

Kodi ndili ndi mpata wokwanira wa pemphero?

Kodi ndikumakhala ndi nthawi ya kuwerenga Buku Lopatulika pa ndekha?

Kodi Buku Lopatulika ndi la moyo kwa ine lero?

Kodi ndikusinkhasinkha umboni wa mphamvu za Mulungu mmoyo wanga ndi mu utumiki?

Kodi Yesu ndi weniweni?

Kodi ndine wophunzitsika ndi kukhala mdindo wa moyo wanga?

Kodi ndilipo ndipo ndikotheka kufilikid a?

Kodi ndikumvetsera bwino?

Kodi ndikukhala chiopsezo kwa ena?

Kodi ndikuphunzitsa ndi mtima watumikira?

Kodi ndine wodalilika?

Kodi ndikusunga lonjezo langa?

Kodi nkhani ya za umoyo wa thupi ndi kuzitsata?

Kodi ndikukwaniritsa kuthetsa kupanikizika kwanga bwinobwino. (kuchokera kwa anzanga, ku ntchito, zochitika zina).

Kodi thanzi langa lili bwanji?

Kodi ndikudya mwathanzi?

Kodi ndikugona mokwanira?

Kodi ndikulola mmalinganiro mwanga mukhale zoganiza zonyansa?

Kodi ndikutha kukumbuikira odwala, osweka mtima ndi osowa?

Kodi banja langa ndi lachimwemwe?

Kodi ubale ndi anthu ena uli bwanji?

Kodi ubale wanga ndi anthu amene ndimatumikira uli bwanji? (anzanga, atsogoleri, amuna kapena akazi)

Kodi kuyankha kwanga kuli bwanji pamene ndili ndi njala, ndakwiya, ndili ndekha, ndi pamene ndatopa?

Kodi ndikukhala ndi malingaliro onyenga osayenera?

Kodi ndikukhala ndi nthawi yopuma mokwanira?

Kodi nthawi yanga ndi kuigwiritsa ntchito bwino?

Kodi nthawi yanga yapadera ndi kuigwiritsa ntchito bwino?

Kodi nthawi ndikuikwaniritsa bwino pakati pa ku Tchalitchi, ku ntchito ndi kunyumba?

Kodi ndi kupanga ndi kusamalira ubale pakati ndi anthu amene sali Akhristu?

Kodi ndikudzionetsera ndekha ku zinthu zochititsa dama?

Kodi ndikugonjetsedwa mwa njira ina iliyonse pa moyo wansanje, wodzidetsa, wosokoneza, wodzikundikira ndi wonyansa?

Kodi ndikugwiritsa bwino ndalama zanga?

Kodi ndikupatsa ena ndalama moyenerera?

Kodi ndasankha kusasilira za anthu ena?

Kodi ndasankha kusaipidwa kapena kudandaula?

Kodi ndikuyenda mu ungwiro?

Kodi ndikuganiza bwino mukusankha kwanga ndi kudzidalira?

Kodi ndine wololera kukumana ndi mavuto?

Kodi ndili ndi zolinga zanga ndipo zikukwaniritsidwa?

Kodi ndi wololera kuchita zinthu modzikhutula

Kodi ndikumakhala ndi malire?

Kodi ndikuyenda mu mphamvu ya Mzimu?

Kodi alipo amene ndikumusungira mangawa osakukhulukira?

Kodi ndikufunafuna kukhala ndi mtendere kuchoka ku chionongeko kapena zinthu zondimanga.

Dalirani Mulungu kochokera pansi pa mtima wanu. Musayesere kuchita zinthu mwa inu nokha. Mvetserani mau a Mulungu mu china chilichonse chimene mukuchita. Iye ndiye amene adzakuyendetsani mnjira yabwino. Osangoganizira kuti mukudziwa zonse. Thawirani kwa Mulungu! Thawani kwa Woipayo! (Miyambo 3:5-7).

UTHENGA WABWINO. PALIBE NDONDOMEKO INANSO.

ADVANCEGROUPS.ORG

Malembo (Ndime) zatengedwa mu Buku Lopatulika. Umwini wa bukhuli ndi wotetezedwa ndi kulolezedwa ndi a Zondervan pa dziko lonse. www.zondervan.com.
Wolemba ndi **The Message Trust**
© 2021 The Message Trust

LUIS PALAU ASSOCIATION

the message